# KUZUNZIKA CHIFUKWA CHA KHRISITU

RICHARD WURMBRAND



**Kuponderezedwa kwa Mpingo Masiku ano**

# KUZUNZIKA CHIFUKWA CHA KHRISITU

*wolemba*

**RICHARD WURMBRAND**

Wofotokoza Mbusa W. Harris F.R.G.S. amene amayang'anira a mishoni m'maiko aku Ulaya.

The Love In Action Society
V-31, Green Park, New Delhi-110 016, India.

# KUZUNZIKA CHIFUKWA CHA KHRISITU

*wolemba*

**RICHARD WURMBRAND**

©Richard Wurmbrand
1st Edition 1991
Copy 5,000

**Printed and published by Dr. P.P. Job, V-31, Green Park, New Delhi-110016, at Sabina Printing Press, Faridabad, India.**

Bukuli ndi buku logwira mtima ndi lolimbikitsa kwambiri pa moyo wa mkhrisitu. Ndiye abale ndi alongo tikupemphani kuti muwerenge bukuli ndi kulingalira mozama zomwe mwini bukuli ndi ena onse otchulidwa mkatimu adakumana nazo pa moyo wawo chifukwa cha ntchito ya Mulungu.

kuzunzika chifukwa
cha
Kristu

Wotanthauzira m'chichewa ndi A Dyson G. Gonthi ndi mkazi wawo Pauline Gonthi.

# Mbiri Ya Mwini Bukuli

Mbusa Richard Wurmbrand waku Rumania yemwe ndi mlaliki wodziwika anakhala m'ndende zaka khumi ndi zinayi (14) m'dzikolo. Iyeyu ndi mmodzi mwa akhrisitu amene alembapo mabuku ndi kuphunzitsa ena za kufunika kwa moyo wa chikhrisitu. Mzaka zambiri pamene boma la Rumania lakhala pa ulamuliro wa chikomunisiti, a Wurmbrand akhala ali kuzunzika chifukwa choti bomalo sirigwirizana ndi m'chitidwe wolalikira mau a Mulungu.

Pamene boma la chikomunisiti lidatenga ulamuliro wa dziko la Rumania m'chaka cha 1945, mbusa Wurmbrand adayamba kuyendetsa utumiki wake mobisa. Iwo ankalalikira mobisala chifukwa choopa asirikali adziko la Russia amene adalanda dzikolo ndi kuthetsa chipembedzo cha chikristu. M'chaka cha 1948, mbusa Wurmbrand pamodzi ndi mkazi wawo a Sabina anawatsekera m'ndende chifukwa chosafuna kusiya kulalikira mau a Mulungu. Akazi a Wurmbrand anakhala mṇdende zaka zitatu kumene anali kuwagwiritsa ntchito yakalabvula gaga. Amuna awo adakawatsekera m'chipinda cha wokha momwe asirikali anali kuwazuza mopanda chifundo. Ndiye patatha zaka zitatu anawachotsamo m'ndendemo ndi kuwaika komwe kumakhala akaidi anzawo ambiri m'menemo anakhalamo zaka zisanu akuzunzika ndi asirikali a bomalo.

A Wurmbrand monga mtumiki ndi mtsogoleri

wodziwika m'maiko osiyanasiyana, akazembe woimirira maikowo adachita zotheka kupempha boma la Rumania kuti a Wurmbrand awasamale ndiku mawasunga bwino m'ndendemo. Ndipo poyankha nkhaniyi, akuluakulu a boma la Rumania adawauza akazembewo kuti mbusa Wurmbrand adathawa m'dzikolo. Ndipo a polisi ena nthawi ina adakonza chinyengo chokadzionetsera kwa akazi a Wurmbrand monga ngati kuti iwo anali akaidi anzawo a mbusayu ndikuwauza akazi awo kuti amuna awo anamwalira kotero kuti iwo anali nawo pa mwambo woika malemu Wurmbrand ku manda ya akaidi. Ndipo kuchokera pamenepo bomalo lidauza banja la Wurmbrand ndi abwenzi awo kuti aiwale za mbusa Wurmbrand chifukwa tsopano ndi malemu.

Patangotha zaka zisanu ndi zitatu, mbusa Wurmbrand anaturuka m'ndende. Iwo ngakhale adaona mabvuto osiyanasiyana ku ndende, sadaleke kuchititsa misonkhano ya mtseri ya mau a Mulungu. Ndipo patangotha zaka ziwiri m'chaka cha 1959 adawagwiranso ndi kuwauza kuti akhala m'ndende zaka 25.

Mwamwayi, pa msonkhano waukulu wa maiko osiyanasiyana wokambirana za chitetezo cha akaidi umene unachitika m'chaka cha 1964, mbusayu anam'masula potsatira pa zimene adakambiranazo. Tsono malinga ndi ntchito yawo a Wurmbrand adapitirizabe kulalikira mwantseri. Ndipo powona umo zinthu zinaliri, ku Rumania, atsogoleri amipingo ku Norway adapempha boma la Rumania kuti limutumize Wurmbrand ku Norway kuopa kuti angamumangenso kachitatu. Nthawi imeneyi dziko la Rumania lidakhazikitsa mchitidwe womagulitsa akaidi aza ndale ku maiko ena. Ndipo mkaidi aliyense amamumasula ndi kumu-

tumiza kunja kwa dzikolo pokhapokha bomalo litalandira ndarama zokwana £800. Koma a Wurmbrand adawalola kuwatumiza kunja kwa dzikolo ngati atalandira ndarama zochuluka zokwana £2,500. Akhrisitu aku Norway adachita zotheka potumiza ndaramazo kotero kuti mbusayu anapita ku Norawy. Ali kumeneko, pa mwezi wa May 1966, anapita ku Washington m'dziko la United States kukachitira umboni za mmene amazunira ali m'ndende ku Rumania. A Wurmbrand anali kufotokoza mabvuto awo pa maso pa msonkhano waukulu waza chitetezo m'dziko la United States. Pamene mkuluyu amafotokoza za moyo waku ndendewo, anabvula malaya ake kuwalangiza anthu aku msonkhanowo zipsera za mabala wochititsa mantha zokwana 18 chifukwa chobaidwa ndi kuchekedwachekedwa pamene anali mkaidi. Pakutha pa msonkhano, nkhaniyi adailemba m'nyuzi pepala zosiyanasiyana ndipo nkhani imeneyi inamveka m'maiko ambiri makamaka m'dziko la Amerika, maiko aku Ulaya ndi m'maiko aku Asia. Pa mwezi wa September 1966, boma la Rumania powona kuti nkhani ya Wurmbrand yadziwika m'maiko ambiri bomalo lidakonza chiwembu choti mbusa Wurmbrand aphedwe. Komabe ngakhale panali chiwembu cha mtundu umenewu, Mbusa Wurmbrand sadaleke kufotokozera ena za mazuzo awo m'ndende. Ndipo anthu anayamba kuwatchula a Wurmbrand ndi dzina loti "Mau a Chalichi Chobisika." Ena amamuitana ndi dzina ioti "Mtumiki wophedwa." Lina ankati "Paulo wa ndende."

# Dongosolo

Wolongosola nkhaniyi ndi mbusa W. Stuart Harris, F.R.G.S. Mtsogoleri wa mamishonale wochokera ku maiko aku Ulaya.

Panali pa mwezi wa December 1964, pamene ine ndinakalowa m'dziko la Rumania Mzaka zapita m'mbuyomu, kusiya dziko la Albania ndi dziko la Rumania lokha laku Ulaya komwe ndinali ndisanafikeko. Pa miyezi ingapo yapita m'moyo wanga ndimabva kukakamizidwa kuti ndiyenera kukacheza m'dziko la Rumania. Ndipo pa chifukwa ichi, ine ndidatsagana ndi mbusa John Moseley kudzera m'malire ochokera ku Hungary kulowa m'dziko la Rumania. Ndiye titalowa m'dzikolo, zochitika zake za dzikolo zidatitsimikizira kuti tiri m'dziko la chikomunisiti chifukwa akuluakulu a boma la dzikolo ankatilondola m'mapazi. Tsono ngakhale zinthu zinali choncho akhrisitu akumeneko adatirandira ndi manja awiri kotero kuti usiku wa tsiku lina tinakakhala nawo ku mpingo wa German Baptist ku Bucharest m'dzikomo. M'chalichimo atsogoleri adatipempha kuti tipereke malonje ndi kuchitira umboni paza moyo wathu wa chikhrisitu. Atatha mapempherowo, ambiri adali nafe ndi chidwi cholankhula nafe ndipo pakati pa anthuwo padali munthu wina wamtali yemwe adatsimikiza kuti zibvute zitani ndi okonzeka pa chirichonse chifukwa chowatenga alendowo kupita nawo ku nyumba kwake. Ndipo usiku

wa tsikulo nthawi ya 10.koloko tidapita ku nyumba kwake komwe a Wurmbrand ndi akazi awo nkudzanso mwana wawo Mihai amakhala.

Titalowa mkachipindamo mwakachetechete, tidapezamo mbusa amene ndakhala ndikumumvera mbiri yake pa nthawi yaitali. Iyeyu ndi mbusa Wurmbrand. Pa nthawiyi anandifotokonzera zonse za moyo wake pa utumiki ndi za masautso anali nawo pamene anali m'ndende pa zaka 14. Alikundifotokonzera za nkhaniyi, Mkazi wawo mai Sabina pamodzi ndi mwana wawo anatuluka kupita kunja kwa nyumbayo kukaona ngati kuli asilikali chifukwa choti banjalo limazondedwa kawirikawiri ndi bomalo. Atabwerako, adauza anthu anali m'nyumbamo kuti asilikali azungulira nyumba yonse ndi kuti galimoto lawo analiimika mopenyana ndi nyumba amachezeramoyo. "Akhala akuilonda nyumbayi mpaka liti ndipo zotsatira zake zidzakhala zotani?" Mosasamala za mafunsowa, a Richard Wrumbrand adatsirizabe nkhani yawo yonse ndipo kenaka tinapemphera. Mapemphero tinali nawowo anali mapemphero wosaiwalika wompempha Ambuye kuti apitirize kuteteza atumiki ake. Nthawi imeneyi a Wurmbrand adationetsa mabala a m'thupi lawo ndipodi inali nthawi yochititsa mantha pamene a Wurmbrand anali m'ndende. Koma mabvutowo adatitsimikizira chigonjetso ndi kuunika pakati pa m'dima, komanso anasonyeza ulemerero ndi chikondi. Ndipo Mulungu adabva mapemphero athu ndipo pamene timatuluka kupita tidapeza asilikali aja atapita.

Inali nthawi yathu yoyamba kukumana ndi banja la Mulunguli limene limachitira umboni za Yesu Khrisitu ndipo kuchokera nthawi imeneyo tinakhala osin-

thika pa miyoyo yathu. Nchifukwa chake kwa ine ndi chaulemu kwambiri kufotokoza za bukuli ndipo ndirikulipereka poliikiza m'mapemphero kuti aliyense woliwerenga bukuli akakhale nacho chikondi chopempherera anthu a m'maiko a chikomunisiti, amene akubvutika chifukwa cha dzina la Yesu.

Mbusa W. Stuart Harris yemwenso ndi mkulu woyang'anira mamishonale a m'maiko aku Ulaya ndiye amene anali woyamba kudzandiona nditangotuluka m'ndende m'chaka cha 1964 m'dziko la Rumania-lo. Mbusa Harris adadzalowa m'nyumba ndi makhalamo nthawi ya usiku mozemba ndi mwatcheru kuopa a polisi a dzikolo. Mbusayu anabwera ndi mau achikondi ndi wolimbikitsa mabanja amene akuzunzika chifukwa cha moyo wa chi khrisitu. Ndipo ndithokoza kwambiri chifukwa cha mau abwino adandirimbikitsa nawo pa nthawi ya masautso athu.

# Chidziwitso

**CHIFUKWA CHIYANI NDALEMBA BUKULI**

Cholinga changa nkufotokonzera akhrisitu onse omasuka, za utumiki wanga wa mseri.

Utumiki wochita mobisawo ndakhala ndikuwuyendetsa pa zaka zambiri ndipo ndawona kuti nkofunikira kuti zomwe ndakhala ndi kukumana nazo pa utumiki wa mtundu umenewu ndi auze azanga zimene ndaona ndi zomwe Mulungu wakhala akuchita nane pa nthawi yonseyi. Mwa chisomo cha Ambuye, ine ndabzola mu zowawa zoopsya zomwe ndazilemba m'bukuli ndipo zina ndakhala ndi kufotokonzera a Khrisitu ambiri m'maiko mmene muli ufulu wachipembedzo. M'bukuli ndafotokozamonso zakufunika kwa chikhulupiriro ngakhale pa nthawi imene munthu ali pa masautso monga ndi naziona ine mu utumiki wa charichi chobisika m'maiko achikomunisiti.

Uthenga wangawu, ndi wofuna kuti inu akhrisitu musakhale chete koma kuti mukadzipereke pa utumiki wa Ambuye malinga ndi zomwe zikuchitika pa moyo wa mkhrisitu. Poyamba ndi kuwuzani za umboni wanga ndipo kenaka ndi kufotokozerani za mmene ntchito ya charichi chobisika inali kuyendera m'maiko oopsya a chikomunisiti.

# MUTU 1

**Munthu Wosapembedza amlandira khrisitu.**

Ine ndidakulira m'banja la chikunja losadziwa chipembedzo china chiri chonse. Pa ubwana wanga ndidalibe mwayi wophunzira za mau a Mulungu ndipo pamene ndimafika zaka 14 ndinali ndichikhulupiriro choti kulibe Mulungu ndipo ndinali nkunja weniweni. Chifukwa cha moyo umenewu, ndi nali mwana wouma mtima. Ine ndinali mwana wa masiye kuchokera pa ukhanda wanga ndipo ndinali waumphawi kuchokera nthawi ya masautso a nkhondo yoyamba ya dziko lonse la pansi. Pamene nditafika zaka khumi ndi zinayi (14) ndinali kukonda kuwerenga mabuku achikunja achikomunisiti wonena kuti kunja kuno kulibe Mulungu. Ndipo mabuku osimba za chipembedzo ndi madana nawo chifukwa ndimati ndi mabuku osokoneza nzeru za munthu ndipo chifukwa cha ichi ndinali mnyamata wa nkharwe wouma mtima ndipo wosafuna kumva nkhani ya chipembedzo.

Koma inandifikira nthawi kuti mwa chisomo cha Ambuye ndinakhala mmodzi wosankhidwa wa Mulungu ndipo mpaka pano sindidziwa kuti zidachitika bwanji. Ndipo zifukwa zidapangitsa kuti ine ndikhale mtumiki wa Mulungu ndi zozizwitsa chifukwa ine ndinali munthu woipitsitsa ndi wopanda chikhulupiriro. Koma mwa chisomo cha Ambuye, ndinangopezeka ndiri mtumiki wa Yesu.

Komabe ngakhale kuti ndinali wakunja panali chinthu china chake chimachitika m'moyo wanga kuti pa zifukwa zosaoneka bwino nthawi zina ndi matengeka kufuna kukapemphera nawo ku chalitchi. Kawirikawiri ndi machiona chobvuta kuti ndingodutsa pa chalitchi osakapemphera nawo. Ndikalowa nawo m'chalichimo chomvetsa chisoni n'chakuti sindimamva kapena kuzindikira zimachitika m'machalichimo. Ndinali kutchera khutu kwa wolalikirayo koma osamva zimene ankatanthauza pa ulaliki wake. Ine ndidali ndi chikhulupiriro choti kulibe Mulungu ndipo ndimadana ndi nkhani yoti ndi zimvera za Mulungu. Koma chimene ndinkachita nacho chidwi nchakuti ndimaganizabe kuti chiripo china chake chodzaza ndi chikondi chimene chimayang'anira dzikoli. Pa moyo wanga ndinali ndi masiku ochepa okhala ndi chisangalalo ndipo chifukwa cha ichi ndimakhulupirira kuti pali chikondi chimene chinali kundidikira chomwe ndidadziwa kuti ndi chimene chingabweretse chimwemwe m'moyo wanga.

Chikhulupiriro changa chinali choti kulibe Mulungu ndipo nkhani imeneyi imandimvetsa chisoni chifukwa pansi pa mtima wanga ndidafunabe kuti pakhale Mulungu wachikondi. Tsiku lina lake ndikuzunguzikabe ndi nkhani ya Mulunguyi, ndidalowa m'chalichi cha Katolika ndipo ndidapeza anthu atagwada ndikumalankhula mau. Pomwepo ine ndidasendera pafupi kuti ndimvetsetse zomwe ankalankhulazo ndi cholinga choti inenso ndikalankhule mau amanenawo ndi cholinga choti ndione ngati pangachitike kanthu kena. Anthu m'chalichimo, ankapemphera motero "Tikuoneni Mariya wa chaulele chodzaza" Ine ndinab-

wereza mau awo monena chimodzimodzi ndikuyan-g'ana choumba chofanizira mai Mariya chomwe chinali kutsogolo kwathu. Koma osaona chosinthika chiric-honse ndipo izi zidandimvetsa chisoni kwambiri. Ndipo tsiku lina lake, monga munthu wosakhulupirika za Mulungu ndi dapemphera motere. "Muzalungu ndi-kudziwa kuti inu kulibe koma ngati ndi zowona kuti inu Mulungu mulipo chimene ine sindikhulupirira; ndi ntchito yanu kuti mudziwonetsere nokha kwa ine." Ine ndinali wakunja kwa mpingo ndipo ukunja wangawo sudandipatse ine mtendere ku mtima kwanga.

Pa nthawi imene ndimasinkhasinkha za moyo wan-gawu, chifukwa chosowa mtendere ndi dafika m'mudzi wina wake wapa mwamba pa phiri m'dziko la Rumania komwe ndinakapeza munthu wachikulire yemwe ntchito yake inali yopala matabwa. Iyeyu ndidampeza akupemphera motere: "Mulungu wanga ndakhala ndi kukutumikirani pano pa dziko la pansi ndipo ndikufuna ndirandire mphotho ya pano pa dziko la pansi ndi yaku mwamba. Ndipo mphotho yomwe ndikufunayo n'ya-kuti ine ndisamwalire msanga mpaka apo nditatemben-uza myuda kuti akadziwe inu Khrisitu chifukwa inu Yesu munali wa mtundu wa chi Yuda. Tsono taonani ndine munthu wodwaladwala, wosauka komanso woka-lamba kotero kuti sindingathe kuyenda m'mudzi onsewu kuyang'ana mYuda. Ndiponso m'mudzi mwangamu mulibe mYuda. Kotero ndikukupemphani mubweretse m'Yuda m'mudzi mwanga ndipo ndidza-chita zotheka kuti adzamulandire Khrisitu."

Litangochitika pemphero la munthuyo, ndidamva kukakamizidwa m'moyo wanga kuti ndikacheze

m'mudzi mwa mkulu uja ngakhale kuti ndinalibe cholinga choti ndikachite m'mudzimo. Dziko la Rumania liri ndi midzi yokwana 12-sauzande. Pomwepo mkulu uja atandiona m'mudzimo, adalankhula mau ondisangalatsa ondiyamikira kuti ndinali munthu wokongola wamaonekedwe abwino layankhidwa ndipo nthawi yomweyo adandipatsa buku lopatulika kuti ndiwerenga. Ine mzaka za m'mbuyomu ndakhala ndikuwerenga baibulo. Koma baibulo ndnalandira kwa mkuluyu linali ngati lina lakenso. Atamaliza kundiwuza zofunika mbukulo, iwo pamodzi ndi akazi awo adagundika kundipempherera pa nthawi yaitali kuti ine pamodzi ndi mkazi wanga titembenuke mtima ndikumulandira Ambuye. Baibulo adandipatsalo linali lodzala ndi mau a chikondi ndi mapemphero omwe anali kundipempherera mkulu-yo. Nthawi zambiri ndimalephera kuti ndi werenge m'malo mwake ndi mangolira poganizira kuipa kwanga komwe Yesu adazuzikira; kuipa mtima kwanga ndi kukoma mtima kwa Yesu; Udani wanga ndi chikondi cha Yesu kuti ine mkundirandirabe kukhala wake wa Yesu.

Ine ntangotembenuka sipadapite nthawi, mkazi wangaso naye anatembenuka. Ndipo mkazi wangayo anatembenuza-nso ena kuti abwere kwa Ambuye ndipo enawonso adatembenuza anzaonso kuti akhale akhrisitu ndipo kuchokera pamenepo, mpingo wa Lutheran udayambika m'dziko la Rumania.

Posakhalitsa zinthu zidasintha m'dzikomo mudalowa boma la nkhaza la Nazi. Akhirisitu nthawi imeneyi adazuzika kuphatikizapo Ayuda nawo anali pa mabvuto ndi boma latsopanolo.

Nthawi imeneyi ngakhale ndinali ndisanadzozedwe ndi kukonzekera za kuyendetsa utumiki, ndinali ntakhala kale mtsogoleri wa mpingo wa Lutheran malinga nkuti ine ndinali munthu amene ndidayambitsa mpingowo. Udindo onse wokhudza chalichi-cho unali m'manja mwanga. Ndipo akazi anga ndi ine timakhalira kumangidwa, ndi kumenyedwa pa maso pa akuluakulu woweruza mirandu. Boma la Nazi linali loopsyeza ndipo tsoka ilo, pa mbuyo pa bomalo panafika boma la chikomunisiti. Mwana wanga Mihai adamupatsa dzina lomwe silinali la chiyuda kupewa kuti angamuphe.

Ubwino wa mchitidwe wa Nazi kwa ife udali woti bomalo lidatiphunzitsa kuti kumenyedwa kunalibe kanthu malinga mzimu wako uli wotetezedwa ndi Mulungu. A Nazi adatiphunzitsa mmene tingamayendetsere chikhrisitu chathu mtseli ndipo zinkachitikazo zinali ngati zokonzekera mabvuto omwe anali nkubwera pansi pa ulamuliro wa chikomunisiti.

## Utumiki Wanga Pakati Pa Anthu Aku Russia

Malinga ndi zimene ndakhala ndikuchita zotsutsa mau woti kulibe Mulungu sindimaupeza mtima ndinalakalaka kukachitira umboni zakutembenuka kwanga pakati pa mtundu waku Russia. A Russia ndi anthu amene pa misinkhu yawo yonse amakula ndi moyo wachikunja wosadziwa nawo Mulungu. Ndipo mwamwayi chilakolako chofuna kufalitsa uthenga pakati pa a Russia ndi nachikwaniritsa popeza m'dziko la Rumania muli anthu ambiri ochokera ku dziko la Russia ndipo ambiri mwa iwo anali akaidi ankhondo ndipo ndinali

kuwalalikira zakufunika kwake kotembenuka mtima.

Utumiki wanga unali utumiki wamphamvu, chifukwa sichinali chapafupi kutembenuza munthu waku Russia. Ndikumbuka tsiku lina lake ndinalankhula ndi mkaidi yemwe adandiuza kuti iye ntchito yake ndi ya umakaniko. Ndipo ndidamufusa ngati amakhulupirira Mulungu. Kwa ine munthu akandiyankha kuti sakhulupirira Mulungu sindimadandaula naye chifukwa ndi madziwa kuti munthu ali ndi ufulu wosankha. Tsono mkaidi-yo adandituzulira maso ndi kundiyankha kuti boma lake silinalamulire kuti akakhulupirire kuti kuli Mulungu. Iye adati, ngati bomalo litamuuza za nkhaniyi adzakhulupirira. Koma ngati boma silimuuza kanthu pa nkhani imeneyi palibe chimene angakhulupirire.

Nditamva kalankhulidwe kake ka munthuyu, ndinadza misozi m'maso mwanga mtima wanga unasweka pomva zimene adandiyankhazo zotsimikiza kuti munthuyo ndi wakufa wosadziwa chimene Mulungu ali, kwa iye. M'malo mwake angoyendera maganizo a chikomunisiti womuuza zoti akhulupirire chinthu chokhacho chimene boma lake la muuza kuti akhulupirire. Munthuyu analibe mwayi woganiza pa yekha. Umu ndi mmene mchitidwe wachi komunisiti umaononongera anthu kuti sangaganize chinthu pa okha koma boma lawo liganize m'malo mwawo. Machitidwe awa ine adandirimbikitsa ndi kulonjeza kwa Mulungu kuti ndidzachita zotheka kuwalalikira anthuwo ndi kuwadziwitsa chowonadi kuti munthu adalengedwa kuti akhale ndi ufulu woganiza pa yekha ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndi mwa mwana wake Yesu Khrisitu.

Pa tsiku la 23 August, 1944, m'dziko la Rumania mudafika asilikali aku Russia okwana 1-miliyoni. Nthawi imeneyi ndi nthawi imene boma la chikomunisiti lidayamba ulamuliro m'dzikolo. Zinthu nthawi imeneyi zidayamba kufika poipa ndipo bomalo lidali la nkhaza zoopsya kuposa boma la Nazi.

M'masiku amenewo, dziko la Rumania lidali ndi anthu okwana 18-miliyoni, pamene a chipani cha chikomunisiti analipo 10-thousand okha. Tsiku lina a Vishinsky omwe anali kazembe woimira dziko la Russia ku Rumania adadzalowa mu ofesi ya mfumu Michael I, ndi kumenya pa tebulo la mu ofesilo uku akunena mau awa: "Mu ofesi muno tsopano mukhale a boma la chikomunisiti. "Asilikali a dziko la Rumania nthawiyi nkuti atawalanda futi zawo ndiponso a polisi atawasiyitsa ntchito zawo ndipo panali chipolowe cha dzaoneni panalibenso kuyanjana, zinthu zinali pwirikiti pakati pa Amerika ndi a Britishi.

Ndi ntchito yathu kupembedzera kwa mulungu osati ife tokha ayi koma mtundu onse. Zimene zidachitikazo nthawi imeneyi ndi chifukwa cha mkhalidwe oipa wa Americans chifukwa iwo ndiwo amasokoneza zinthu kuti zifike poipa. Tsono malinga ndi mmene zinthu zinaliri inali ntchito ya Akhrisitu m'maiko aku Amerika ndi ku Britain kuthandizapo kuthetsa m'chitidwe wa nkhazawo wopha anthu wopanda chifukwa.

## Mau Onena Za Chikondi Ndi Onena Za Kushashalika ndi Amodzi

Pamene boma la chikomunisiti lidayamba kulamulira boma-lo, akuluakulu achikomunisiti adayamba

kulowerera m'machalichi ndi mau onyengerera pamene kunali kuthetsa mapemphero ndikumachita zina zosiyana ndi cholinga cha machalichiwo. Iwo polankhula kwa anthu ampingo amalankhula ngati kuti naonso ndi anthu a chalichi chiri chinyengo chofuna kubweretsa chikunja.

Iwo anayamba kufotokonzera akhrisitu kuti mau akuti chikondi ndi amodzi kaya mwamuna akufuna kutchita ukwati ndi mtsikana kwa iwo amauza anthu kuti ndi chikondi ndipo ngati mwamunayo afuna mtsikanayo osati mwa chikwati koma kungonyengangana kwa iwo amati ndi chimodzimodzi ndi munthu amene walonjeza za ukwati. Mafotokozedwe awa anali ongofuna chisokonezo ndi kubweretsa choipa pakati pa anthu. "Yesu adatiuza za chikondi chenicheni osati chachinyengo chodzionetsera ngati wabwino pamene uli wamakhalidwe oipa. Tsono anthu achikomunisitiwo atayamba kulankhula motere, ambiri abusa ndi alaliki adayamba kusokonezeka osadziwa kusiyanitsa pakati pa mau a chinyengo ndi ya chilungamo.

Akuluakulu a boma latsopanolo la chikomunisiti, adaitanitsa msonkhano omwe unakachitikira m'nyumba ya malamulo ya azibusa okhaokha a mipingo yosiyanasiyana. Onsewo pamodzi anali 4-thousande ndipo pa msonkhanowo adasankha a Joseph Stalin kukhala woyang'anira msonkhano-wo. Iwowanso anali president wa gulu losakhulupirira Mulungu la dziko lonse la pansi ndiponso anali chigawenga chopha anthu makamaka akhrisitu. Polankhula pa msonkhanowo, azibusawo, mabishopu ndi akuluakulu ena amipingo anatsimikizira pa msonkhanowo kuti chikomunisiti ndi

chikhrisitu ndi zinthu zofanana. Atsogoleri amipingowo, pokondweretsa boma latsopanolo, amati adzachita zotheka kuti mipingo yawo izitumikira bomalo ndipo anatsimikiza kuti adzalilemekeza boma la chikomunisiti-lo.

Ineyo ndi mkazi wanga tinali nawo mu msonkhanowo ndipo tinamva zonse zinali kukambidwazo.

Mkazi wanga atamva zolankhulazo, anati, "A muna anga tadzukani ndipo mu mpupute Khrisitu pa maso chifukwa cha zonse zoipa zanenedwazi, chifukwa uku ndi kumulabvulira malobvu Khrisitu. "Ine poyankha ndinati, kuwuza mkazi wangayo "Ngati ndi lankhula motsutsana nawo anthuwa ndiye kuti sukhala ndi mwamuna." Poyankha mkazi wanga anati, "Kuli bwino kukhala opanda mwamuna kusiyana ndi kukhala ndi mwamuna amene ali wa mantha.

Pomwepo ine ndidadzuka ndikupereka ulemu wanga wonse wa Khrisitu ndi Mulungu atate ndi kuwatsimikizira anthu pa msonkhanowo kuti poyamba tiyenera kulemekeza Ambuye mwini zonse. Nkhani zinkalankhulidwa pa msonkhanowo zidamveka pa wailesi kuti ine ndidatsimikiza zakufunika kwa uthenga wa Khrisitu ku anthu onse. Ndipo kenaka ndidalandira chirango koma sindinadandaule chifukwa kunali koyenera kulankhula za ukulu wa Mulungu pa msonkhano ngati umenewu.

Mipingo yosiyanasiyana nthawi imeneyi idayamba kutsutsana paza mchitidwe wogonjera mchitidwe wachikomunisiti. Ndipo Bishop wa mpingo wina pofuna kusonyeza ulemu ku boma la chikomunisiti adawandika kapena nditi kusindikiza chikwangwani pa

malaya awo cha chithuzi cha nyundo ndi chisikiro. Ndipo iwo adauza azibusa onse kuti asamamuitanenso Bishop woyera koma aziti "Mzathu bishop." Ndinakakhala nawonso ku msonkhano wa chalichi cha Baptist omwe unakachitikira mtauni ya Resita ndipo pa msonkhanopo anaikapo mbendera yofiira ndipo pamene nyimbo ya fuko la chikomunisiti anali kuimba anthu onse anali ataima kupereka ulemu. Prezidenti wa Baptist anati a Stalin ndi munthu yemwe wakwaniritsa malamulo a Mulungu. Iye adayamikira a Stalin kuti ati ndi mphunzitsi wamkulu wa baibulo. Ndipo a Patrascoiu ndi a Rosianu ndiwo anali otengeka kwambiri ndi zochitikazo kotero kuti anthu awiriwa anawaika kukhala apolisi obisika kuti aziona bwino zochitika. Wachiwiri kwa Bishop wa mpingo wa Lutheran m'dziko la Rumania adayamba kuphunzitsa chiphunzitso cha chilendo kuti ati Mulungu adapatsa masomphenya kwa anthu atatu okha omwe ndi Mose, Yesu ndi Stalin. A Rapp bishop adati a Stalin ndi woponsa ena onse pa masomphenya omwe Mulungu akuwagwiritsira ntchito.

Kunena zowona iwo amene anali akhrisitu enieni a mpingo wa baptist omwe ine ndinali kuwakonda sadagwirizane nazo zimene zinali kuchitikazo ndipo iwo anali kupitirizabe kuika chikhulupiriro mwa Yesu. Tsoka ndilo a chikomunisiti kenaka adadzasankha atsogoleri awo mu mpingomo kotero kuti zidali zobvuta kuti awakane. Zoterezi zimachitikanso ngakhale masiku ano kuti amene amatsogolera si omwe anthu amawafuna ayi.

Iwo amene adayamba kutumikira chikomunisiti m'malo mwa khrisitu adayamba kunyoza iwo amene sadawatsatire pa zochita zawozo. Pamene akhrisitu ku

Russia adaona kuti zinthu zafika poipa, adayamba kuyendetsa ntchito ya mipingo yawo mobisala ndipo ifeso tidayamba kuchita chimodzimodzi powona kuti wokhulupirira ambiri anali kuwamanga. A chikomunisiti adaletseratu kulalikira uthenga kapena kuphunzitsa ana za chikhrisitu. Ndipo malinga ndi mmene zidaliri zinthu nawonso akuluakulu a mpingo adayamba kumvomereza kutsatira zolinga za boma la tsopanolo. Komabe ineyo ndidapitiriza kuyendetsa utumiki wanga mobisa kuti boma lisadziwe ndipo china chimene chidapangitsa kuti ndisadziwike msanga n'chifukwa choti ndinali ndi bungwe la zosamalira anthu limene silimakhudzana konse ndi utumiki wa mau a Mulungu. Bungwe limeneli linali ngati chophimba kuti ena asadziwe zenizeni zimene ndimachita monga mtumiki wa Yehova. Pa utumiki wanga monga mtsogoleri wa chalichi cha Lutheran ndinalinso woimirira bungwe la World Council of Churches bungwe loimira mipingo yosiyanasiyana ya m'dziko lonse la pansi.

Pamene ndi matumikira m'bungweli, ndidalibe ganizo loti tsiku lina bungweli nkudzagwirizana ndi zochita za chikomunisiti. Nthawi imeneyo dziko langalo silimachita ntchito ina iriyonse koma kuthandiza anthu obvutika pa zifukwa zosiyanasiyana. Ntchito imeneyi ya bungwe loimira mipingo yosiyanasiyana ndiyo idandithandiza kuti ndisagwidwe msanga pa ntchito yanga yautumiki.

Utumiki wanga udagawidwa motere; Utumiki woyamba unali wochita mwakabisira pakati pa asilikali 1-million aku Russia. Ndipo wachiwiri ndi matumikira pakati pa anthu amene amazuzika chifukwa cha chikhu-

lupiriro chawo. Mautumiki onsewo ndimachita mwakabisira kuti boma lisanditulukire msanga.

**A Russia Ndi Anthu Omwe Miyoyo Yawo Iri Ya Ludzu. Ndi mau a Mulungu.**

Kwa ine kulalikira pakati pa anthu a dziko laku Russia kumakhala ngati ndiri dziko lina lake osatinso ku dziko la pansi ayi. Ine ndalalikira anthu amaiko ambiri koma sindinaone anthu onthunthumira ndi aludzu la mau ngati aku Russia. Anthu akumeneko ndi aludzu lofunitsitsa mau a Mulungu.

Mbusa wina wake amene anali bwezi langa adandichitira ine foni kundiuza kuti ofisala wina wa boma la Russia anabwera kwa iye kudzalapa. Ndiye pokhala mzangayo samatha kulankhula chilankhulo cha chi Russia adangomutumiza kwa ine mkuluyo. Ndipo atafika munthu ameneyu adanditsimikizira kuti ankonda Mulungu ndipo amamulakalaka koma anali asadalione buku lopatulika. Ndipo pa moyo wake sanakhalepo pa msonkhano wa mau a Mulungu ichi nchifukwa choti ku Russia mwayi womva uthenga ndi wochepa kwambiri. Iyeyu adamukonda Mulungu ngakhale kuti analibe nzeru ina iriyonse yosimba za Mulungu.

Ine ndidamuwerengera mau achiphunsitso cha paphiri omwe ankaphunzitsa Yesu. Ndipo nditatha kumulongosolera za chiphunzitsocho, mkuluyo nthawi yomweyo adayamba kubvina kuzungulira m'chipindamo ali ndi chimwemwe chodzala tsaya. Ndipo nkulankhula kwake anati, "Nzodabwitsa izi ndipo nzabwino kuzimva! Nkanakhala munthu wa mtundu wanji osadziwa Khrisitu." Iyeyu anali munthu

woyamba kuona akusangalala chomwechi chifukwa cha dzina la Khrisitu.

Nthawi imeneyi ine ndinalakwa chinthu chimodzi, ndidamufotokozeranso za Yesu m'mene adazuzikira kunkwapula ndi kumkhomerera pa mtanda ndipo kenako kufa. Nditangonena za kufa kwa Yesu, mkuluyu adagwa pansi ndi kulira kwambiri chifukwa choti iye adaika chikhulupiriro kwa mpulumutsi wakufa. Ine ndidamuyang'anitsitsa ndipo ndidamva chisoni kuti sindikadayenera kumuuza nsanga za infa ya Ambuye Yesu. Iye nkulira kwake kunandikumbutsa kulira kwa Maria wamagadala pansi pamtanda wa Yesu kulira kos-weka nako mtima.

Pamene anali kusisimabe, ndidayamba kumuwer-engera za mbiri ya kuuka kwa Yesu Khrisitu ndipo atamva kuti Yesu ndi wa moyo adadzuka kwa akufa, adakondwa ndi kufuwula mwa chisangalalo akunena mau woti "Ndi wa moyo ndi wa moyo" nthawi imeneyi akuzungulira mchipindamo uku akubvina. Ndipo pom-aliza ndidamuuza kuti tipemphere. Iye sadadziwe kuti kupemphera n'chiyani. Ndipo iye ndi ine pamodzi tinagwada ndipo nkulankhula kwake anati "Mulungu ndinu wabwino mukanakhala ngati moyo wanga simu-kadandikhulukira koma inu mwa ndikhululukira machimo anga. Ndinu nokha wabwino! ndipo ndiku-kondani ndi mtima wanga wonse."

Ndikukhulupirira kuti angelo kumwambako ada-siya kuchita zina zonse ndi kutchera khutu kupemphero la mkuluyu. Ofisalayu kuchokera pamenepo adamulan-dira Yesu.

Tsiku lina lake ndinafika ku sitolo komwe ndina-

kapeza m Russia akugula zinthu zofunikira koma chinthu chimodzi chidabvuta n'chakuti wogulayo samadziwa zimene ankalankhula wogulitsayo kotero kuti ine ndidawathandiza kutanthauzira ndipo kuchokera pomwepo tinakhala abwezi. Tsono ine ndinamuitanira ku nyumba kwanga kuti akakhale nawo pa chakudya chathu cha masana. Ndipo pa nthawi-yo tisanayambe kudya ndidawauza kuti m'nyumba alimo ndi mwa mkhrisitu kotero kuti tisanayambe kudya tiyenera kupemphera. Ndipo ine ndidapemphera mchinenero cha chi Russia. Alendowa adaika pansi mafoloko ndi mipeni yodyera ndipo chidwi choti adye nawo chakudyacho chinawachokera. Ndipo adayamba kufusa mafunso aza Mulungu ndi Khrisitu nkudzanso baibulo. Zonsezi sankazidziwa.

Sichinali chapafupi kugwirizana nawo alendo angawo chifukwa zonse ndimafotokoza kwa iwo zinali zachirendo. Mwachitsazo ndi nawafotokozera za munthu amene adali ndi nkhosa zokwana 100 ndi kuti imodzi ya izi idasowa ndi mmene mwini wake adabvutikira pofuna kuti aipeze. Iwo poyankha adati zingatheke bwanji kuti munthu mmodzi angakhale ndi nkhosa 100 koposa boma lokha. Ndipo ndidawauzanso kuti Yesu ndi mfumu. Iwo poyankha adati mafumu onse anali oipa a nkharwe kusonyeza kuti Yesu nayeso anali wouma mtima. Kenako ndi nawauza za mwini munda yemwe adafuna kuti amuphe, iwo adati ndi bwino kupha munthu wotero chifukwa sibwino kuti munthu pa yekha akhale ndi munda ayi koma boma. Ndinawauza za kubadwa kwa Yesu ndi Mariya ndipo iwo nkufunsa kwawo adandifusa kuti kodi Mariya anali

mkazi wake wa Mulungu? Kuchokera pamenepo ndidadziwa kuti pofuna kuchitira umboni kwa a Russia ndi bwino kudziwa malankhulidwe ake kuti akamvetsetse chifukwa chikomunisiti chidawalowerera.

A mishonale oyambirira kupita ku Afrika adapeza mabvuto omasulira mau ena a baibulo. Mwachitsazo pa buku la Yesaya pamene pali mau woti "Ngakhale machimo anu ali wofiila ngati kapesi adzayera ngati matalala." Kumasulira mau otero ku Afrika kunali kobvuta chifukwa ku Afrika kulibe ayezi ndipo chisanu cha mtundu wumenewo sichimadziwika. Ndiye a mishonalewo amati machimo anu adzayera–

IWO amatchula zinthu zodziwika kuti anthuwo akhoze kumvetsetsa zimene zinkalankhulidwazo. Ichi ndi chimodzimodzi ndi anzathu aku Russia kuti amvetsetse uyenera kulankhula mchilankhulidwe chawo ndi kupereka zitsazo zimene iwo amazidziwa ndi kuziwona. Tsono zoterezi sizapafupi mpofuna mzimu wa Mulungu kuti uzitsogolera.

Mlendo wanga uja pamodzi ndi akazi awo adatembenuka ndipo anali amodzi wotithandiza pa utumiki wanga wa mseriwo. Pali mabuku amau a Mulungu ambiri amene tinawamasulira mchi Russia ndi ku watumiza ku Russia kudzera mwa akhrisitu aku Russia omwe adatembenuka mtima ena amene amatithandiza kupititsa ma baibulo ku Russia ndi asilikali otembenuka a chi Russia.

Panali njira inanso yofalitsira uthenga kwa asilikali achi Russia, iwo monga anthu omwe akhala pa nkhondo nthawi yaitali anali atasiya ana awo kwawo pa nthawi, nchiye poti ndi mtundu wokonda ana kwambiri nthawi

zina amati akaona mwana wanga Mihai ali kusewera ndi ana anzake azaka khumi, asilikaliwo amachita nawo chidwi kukumbukira ana awo ku mudzi. Ndiye chimene timachita, anawo timawapatsa mabaibulo ndi mabuku ena achikhrisitu ndipo anawo amakapereka kwa asilikaliwo akatha kusewera. Asilikali amatenga mabukuwo ndi kumawapatsa anawo masiwiti. Njira imeneyi inali yoopsya kwa munthu wa mkulu ndiye poti anali ana sadasamale koma chokondweretsa nchakuti anali kuwerenga mabukuwo. Anawo anagwira ntchitoyo monga mamishonale ang'ono.

## Kulalikira Ku Malo A Asilikali AchiRussia

Tinkalalikira pakati pa a Russia, osati kwa munthu mmodzi pa yekha pokha ayi, ngakhale m'magulu timakhoza kuchitira umboni. A russia ndi anthu okonda kukhala ndi mawochi ndipo chifukwa cha ichi amakonda kuwabera anthu ma wochi awo. Nthawi zina amakhoza kuwabweza anthu oyenda mu msewu ndi cholinga choti awabere kapena nditi kuwalanda mawochi awo. Nthawi zambiri asilikaliwo amapezeka atamvala mawochi manja onse chimodzimodzinso asilikali achizimai nawonso amakhala ndi mawochi oyenndera mabatiri m'makosi mwawo. Pa chifukwa ichi anthu aku Rumania amapita komwe kuli asilikali a ku Russia-wo kukagula mawochi akubawo ndiye ife, atumiki wobisika tinali kupita nawo monga ngati kuti tifuna kukagula wochi pamene ife cholinga chathu chinali chokalalikira ndi kuchitira umboni za Yesu.

Ine ulendo wanga woyamba ndidatsimikiza zoka-

lalikira ku malo komwe kumakhala asilikaliwo nditapita kumeneko ndidasonyeza ngati munthu wofuna kugula wotchi. Ndiye ndi dazungulira pa malopo kuyang'ana wachi zosiyanasiyana ndi kumaonetsa ngati kuti ndi zodula komaso zing'onozing'ono ndiye kenaka asilikali ambiri anandiunjirira ndipo ndinawafunsa ngati analipo wina yemwe dzina lake ndi Paul kapena Petulo ndipo padapezekadi kuti ena mwa iwo anali ndi maina amenewa. Ndipo ndinayamba kuwafotokonzera m'mene mpingo umakumbukirira utumiki wa Paulo ndi Petulo. Ena sanali kudziwa za anthu amenewa koma akuluakulu okha ndiwo adanditsimikizira zowadziwa anthu ndi nkatchulawo. Tsono pomwepo ine ndidapezerapo mwayi womafotokaza za anthu awiri amenewa Paulo ndi Petulo. Ndiri kufotokoza chomwecho, msilikali wina wachikulire adangofika pa malopo ndi kundiuza kuti ine sindidabwerere kugula watchi koma kudzafotokoza za chikhulupiriro. Ndipo mkuluyo adandipempha kuti ndikhale pansi kuti ndifotokoze bwino za anthu awiri ndimafotokonzawo. Iye adati ndisachite mantha chifukwa onse anaunjikana pa malopo ndi abwino koma adandichenjeza kuti ngati pafika woipa maganizo adzandidziwitsa pogwira bondo langa kundiuza kuti ndilankhule za watchi ndipo akachoka munthu oteroyo azichotsa dzanja lake pa bondo langalo, kumene kuli kundiuza kuti ndipitirize kulankhula za mau a Mulungu. Pa malopo panali anthu ambiri ndipo ine ndinafotokoza za paulo ndi Petulo m'mene adaphedwera chifukwa cha Khrisitu. Ndipo mkulu uja anapitirizabe kukhudza bondo langa akaona munthu wosagwirizana nazo za mau a Mulungu ndipo akachoka

anali kuchotsa dzanjalo pa bondopo, chizindikiro choti ndikhoza kupitiriza uthenga wanga. Ulendo wokacheza ku malo asilikaliwo unali kuchitika kawirikawiri mothandizidwa ndi asilikali otembenuka mtima achi-Russia. Chifukwa chokacheza ku malowo ena ambiri asilikali adalandira Yesu. Mabuku ambiri anali kutumizidwa ku malowo mwachisinsi ndipo ambiri amathandizika.

Ena mwa abale ndi alongo amu utumikiwu ankawagwira ndi kuwamenya kwambiri koma palibe ndi m'modzi yemwe adaulula za utumiki obisikawu.

Tinalinso ndi mwayi womakumana ndi abale ndi alongo amu utumiki omwewu obisika omwe amagwirira ku Russia ndipo amatiuza zambiri zomwe anali kukummana nazo. Ambiri a iwo aphunzira sukulu za chikomunisiti koma adayesetsa kusunga chiyero pa maso pa Khrisitu.

Anthu aku Russia otembenuka mtima amakhala ochititsa chidwi chifukwa chikhulupiriro chawo sichisinthika wambawamba. Nthawi ina anthu aku Russiawo adandiuza kuti; "Timadziwa kuti chikwangwani cha nyenyezi nyundo ndi chisikiro timakoloweka pa malaya kapena pa chisoti chimatanthauza kukana Khrisitu." Ndipo amanena mau awa ndi chisoni ndipo anthu amenewa ndiwo adathandiza kwambiri kufalitsa uthenga.

Zizindikiro zonse za moyo wa mkhrisitu waku Russia ali nazo koma chinthu chimodzi ndi akhrisitu opanda chimwemwe. Kawirikawiri chimwemwe chawo chimaoneka pa msonkhano pokha basi. Ndipo ine

powafunsa kuti chifukwa chiani saonetsa chimwemwe, iwo adati nkobvuta chifukwa pakati pawo amakhalira kuopana chifukwa atumiki ambiri ndi akazitape a boma la chikomunisti. Iwo adati chimwemwe chawo chiri pansi pa mtima ndipo sangathe kuonetsera kunja monga amachitira akhrisitu aku maiko ena. Kwathu kuno chikhrisitu munthu sangathe kuchimvetsetsa, chifukwa ife tikamutengera munthu kwa Ambuye m'malo moti tisangalale timaganiza kuti tamutengeranso ku ndende kotero kuti ana ake adzakhala pa mabvuto opanda bambo kapena mai. Ndiye chimwemwe choti mzathu tamutengera kwa mbuye chimasokonezeka ndi chisoni chifukwa choganiza kuti mwina munthuyo amangidwa ndipo ana ake adzakhala pa mabvuto. Zoterezi ku maiko ena kulibe." Adatero ena polankhula za chikhrisitu chawo.

Monga mmene timaonera ena kuti amaonetsa ngati akhrisitu koma chonsecho ali akunja ndi mmenenso ziriri ku Russia kuti ena amaonetsa ngati kuti ndi achikomunisiti pamene sali choncho koma ndi akhrisitu owona mtima.

Nthawi ina ndi nakumana ndi bambo ndi mkazi wake ndipo pamene ndidayamba kuwalankhulitsa za Mulungu iwo adandiyankha kuti kulibe Mulungu. "Ife sitimakhulupirira za Mulungu koma tikuuzani chinthu china chochititsa chidwi chimene chidationekera." Lidatero banjalo polankhula nane.

Mkulankhula kwawo pondisimbira nkhaniyo adati "Nthawi ina pamene timaumba chifanizo cha mtsogoleri wathu Stalin, mkazi wanga anandifusa kuti kodi amuna anga muganiza bwanji za dzanja, popanda manja

ndi zalazi kapena zalazi zikanakhala ngati zakumwendo ndiye kuti mwezi tikulephera kunyamula zinthu kapena kugwira ntchito monga tichitiramu. Ndiye pamenepa tingati ndani adalenga manjawa. Ineyo ndi amuna angawo tidaphunzira kuti dziko la pansi ndi kumwamba zidadzilenga zokha. Sizidalengedwe ndi Mulungu ndiponso kulibe Mulungu izi ndi zimene tidaphunzitsidwa ku sukulu ndipo timazikhulupirira. Koma ngati Mulungu sadalenge dziko la pansi ndi kumwamba nkoyenerabe kumtamanda chifukwa cholenga dzanja chifukwa popanda dzanja bwenzi moyo wa munthu suli ngati mmene ulirimu sitikadakhoza kugwira china chirichonse.

Timatamanda anthu awa monga Edison, Bell ndi Stephenson chifukwa choyambitsa ndikupeza magetsi, matelefoni ndi maulendo apa njanji ndi zina zotere, nanga chifukwa chiyani osayamika ndi kuthokoza iye amene adalenga dzanja? chifukwa anthu amenewa popanda chikhato kapena kuti dzanja sakadatha kukonza zinthu zonsezi. Tsono pa ichi ndi bwino ndipo nkoyenera kumlambira Mulungu chifukwa cholenga dzanja la munthu."

Malankhulidwe a mkazi wawo, adamukwiyitsa mwamunayo monga mwa chizolewezi kuti mkazi akalankhula za nzeru amuna ambiri amakwiya chonsecho pansi pa mtima akudziwa kuti akulankhula mkaziyu ndi za nzeru. "Wosalankhula za utsiluzo, iwe udaphunzitsidwa kuti kulibe Mulungu basi ndiponso kulankhula kotere kudzakuika m'mabvuto wadziwanji mwina chitseko nchosatseketsa ndipo mkwapafupi ena kukumvera ndi kukuika m'mabvuto. Dziwa ichi ndipo osadzaiwa-

lanso zomwe tidauzidwa kuti kumwamba kulibe Mulungu, kumwamba kulibe ali yense!"

Poyankha mkazi wakeyo adati, "Ngati kulibe Mulungu monga mmene makolo anthu amakhulupirira chomwe chinali chinthu chopanda nzeru ndiye kuti manja athuwa anangodza pa okha popanda chiyambi. Koma ngati kumwamba kulibe kanthu, ine ndi mtima wanga onse ndizipembedza" Kulibe kanthuko Komwe kudalenga dzanja."

Ndiye kuchokera pamenepo banjalo lidayamba kupembedza "a Kulibe kanthu" (Mr Nobody)" Iwo adakhala ndi chikhulupiriro choti Kulibe kanthu ndiye adalenga zonse zabwino tionazi, monga moyowu, maluwa, ana, nyenyezi manja ndi zina zotere.

A Wurmbrand; nkhani adamva ku banjali, idawa Kumbutsa ku Athens komwe Paulo adakapeza anthu akupembedza kwa mulungu wosadziwika. Banjali lidakondwa pamene ine ndidawalimbikitsa kuti chikhulupiriro chao ndi chowona kuti kumwamba kulibe Kalikonse chifukwa choti Mulungu ndi mzimu wa chikondi, wachowonadi ndi wamphamvu yonse, ndipo ndiye adatumiza mwana wake kuti adzatifere pa mtanda kutiombola ifeyo ku chirango choopsya.

Kuchokera apo ndidawathandiza kuwalangiza bwinobwino za chipulumutso. Tsiku lina ndidaona mtsikana kapena nditi mayi wina alikuyenda mu msewu ndipo ine ndidamukodola ndikumuthamangira. Nditafika ndidapepesa kuti andikhululukire chifukwa simwambo wake kukodola mkazi wodziyendera mu msewu. Ndipo kenaka ndidamuuza kuti ine ndine Mbusa ndipo cholinga changa ndimafuna kulankhula nanu za Khri-

situ. Mayi-adandifunsa ngati ndimamkonda Khrisitu. "Ndimankonda kwambiri ndi mtima wanga wonse." Ndidatero pomuyankha mkaziyo. Iye atangomva zimene ndidayankhazo adandikumbatira ndi kundipsyopsyona mowirikiza kotero kuti kwa ine ndidauma thupi kapena kuti manyazi chifukwa mbusa sayenera kutero kupsyopsyonedwa ndi mkazi wapa njira wosamudziwa. Ine ndidabwezera kupsyopsyonako kuti anthu aziti ndife anansi. Iye adafuula kotere kwa ine "Ndimankonda Nanenso ndimankonda Khrisitu." kuchokera apo ndinamtengera ku nyumba kwathu."

Nidye tikucheza ku nyumbako, nkumene ndidadziwira kuti mkazi-yo samadziwa zambiri za Khrisitu koma amangodziwa dzinalo basi. Iye amankonda Yesu kwambiri koma osadziwa kuti Yesuyo ndi mpulumutsi wa moyo wa munthu. Chipulumutso nacho samachidziwa. Zoti Yesu adamufera ndipo kuti adadzuka ndi zonse zachiphunzitso chake samazidziwa. Ndipo ine zidandidabwitsa kwambiri kuti zitheka bwanji kuti munthu angakonde dzina osamudziwa mwini wake?

Nditafunsa, mayi-yu adati iye ali mwana, ankaphunzitsidwa zinthu za maina osiyanasiyana ndipo zinthuzo timazidziwa chifukwa cha zithunzi zomwe amatisonyeza kotero kuti ndi momwemonso ndidaphuzirira kwa makolo anga za dzina loti Khrisitu chifukwa padali chithunzi chake ndipo dzinali lidakhazikika mu mtima mwanga ndipo ndimalikonda kwambiri kwa ine limandipatsa chimwemwe. Pamene anali kulankhula za nkhaniyi ndinakumbukira buku la Filipi lomwe limatiuza kuti bondo lirilonse lidzamgwadira iye. Ndipo ndi zowona kuti ngakhale akunja adzamvomereza kuti Yesu

ndi Ambuye.

Kuchokera pamenepo nditamaliza kufotokoza zonse mayi-yo anasangalala ndi kumulola Yesuyo kuti akhale mu mtima mwake nthawi zonse.

Nthawi yonse ndakhala ndi anthu aku Russia ndaphunzira zambiri za moyo wawo. Tsiku lina chemwali wina pamene amalalikira mu sitima adapereka keyala yanga kwa ofisala wina n'cholinga choti adzakumane nane. Tsono izi zidachitikadi kuti usiku wa tsiku lina munthu wina wamtali wokongola adalowa m'nyumba mwanga ndi kundigwira dzanja nati "Ndikukupempha ndi mtima wanga wonse kuti usandisokeretse. Ine ndine mmodzi mwa anthu amene ali mu m'dima. Tandiuzani chonde kodi mau awa ndi a Mulungudi?" Ine ndidamutsimikizira kuti ndi mau a Mulungu. Pamene ndidayamba kufotokoza, iye anakhala chete kumvera zonse ndimalankhulazo ndipo pa mbuyo pake adalandira Khrisitu.

A Russia ndi anthu achidwi ndi mau a Mulungu ndipo akazindikira chowonadi samabwerera wamba. N'chifukwa chake a Russia akangolandira mau samalekera pomwepo naonso amapita kunka nafotokonzera ena za uthenga wabwinowu. Mtundu umenewu ndi wokonda chipembedzo kuposa maiko ena ambiri m'dziko la pansi.

Nthawi ina m'sitima ndinakhala ndi ofisala wina ndipo ndinali kumulalikira za Khrisitu. Koma iye adakana nkwantuwagaru kuti kulibe Mulungu ndipo adalankhula nkhani iyi nthawi yaitali ndipo anali kutchula mabuku a Stalin, Marx, Voltaire ndi Darwin omwe amasimba kuti kunja kuno kulibe Mulungu. Atamaliza

kulankhula, ine ndinamufunsa kuti chifukwa chiyani iwo amapemphera akakhala pa masautso pamene akudziwa kuti kulibe Mulungu. Ndipo sindidafuna kuti alankhulenso mpaka atayankha funso langa. Iye adabvomeradi kuti nthawi zina aRussia atazingidwa ndi maGerman adapemphera. Ndipo adandiuza kuti ankangochitiramo osadziwa chonena popempherapo.

Utumiki wathu wakabisirawu unagwira ntchito kwambiri mwakuti ambiri adatembenuka chifukwa cha utumikiwu. Ndikukumbuka mnyamata wina dzina lake Petulo yemwe anali wa zaka zosachepera 20 adafika ku Rumania ndi asilikali a nkhondo ndipo pokumana naye tidamthandiza kuti alandire Yesu ndipo kenaka anabatizidwa. Ndipo chifukwa cha chikhrisitucho adamugwira ndi kumutsekera m'ndende ndipo adafera mndende mommo. Iyeyo ankakonda mau apa buku la Luka 24 pamene timawerengapo za nkhani ya Yesu atakumana ndi wophunzira awiri pa ulendo waku Emau. Mnyamatayo amakonda kudabwa kuti chifukwa chiyani Yesu adafuna kupitirira pa mudzi paja chonsecho adalinso ndi chirakolako chofuna kucheza ndi wophunzirawo. Ine ndidamuuza mnyamatayu kuti Yesu ndi wodzichepetsa, Yesuyo adafuna kuti awone ngati wophunzirawo ankamufunadi ndipo ataona kuti ankamufunadi adalolera kulowa m'nyumbamo. Ndinamuuza Petulo kuti Yesu asiyana ndi mmene amachitira achikomunisiti chifukwa iwo amachita zinthu mophanga kapena kuchitira nkhondo kuti zawo zimveke. Safuna za wina aliyense koma za chikomunisiti nchifukwa chake pali ponse tingomva za chimenechi; kuyambira m'manyuzipepala, wailesi, mapositala, mka-

nema ndi mmisonkhano momwe safuna kumva za wina koma zawo za chikomunisiti. Koma Ambuye Yesu adatipatsa ife ufulu wosankha. Ichi nchifukwa chake amagogoda pa khomo ndipo kuli ndi mwini nyumba kutsekula kapena ayi. Mnyamatayu adandiuza kuti ufulu wa Yesu ndiwo udamutembenuza mtima kuti akhale mkhrisitu. Mnyamata petulo adandithandiza pomakapereka mabaibulo mobisa ku Russia ndipo kenaka adamugwira ndipo anali m'ndende mpaka m'chaka cha 1959 panopa ndizokaikitsa ngati ali ndi moyo adziwa ndi Ambuye.

**Utumiki Wathu Wobisika Kwa Anthu Ozunzika**

Utumiki wathu sunali wolinga ku Russia kokha ayi komanso tinali ndi utumiki womwewu m'dziko la Rumania. Zinthu ku Rumania zidafika poopsya kunyengerera kumene amachita achikomunisiti pofuna kuti mtchalichi azichita zofuna za bomalo kunatha tsopano amangochita nkhaza poyera. Ndipo akhrisitu ambiri anali kumangidwa, ifeso nafe tinachirimikira kulalikira anthu ambiri kuti amudziwe Yesu kotero kuti panalibenso kubisa chifukwa zinthu zinafika pobvuta kwambiri. Kenaka nanenso adandigwira ndikunditsekera m'ndende pamodzi ndi anthu omwe ndidawalalikira. Banja lina lomwe linali nane m'ndendemo lidasiya ana asanu ndi mmodzi ndipo chinali chachidziwikire kuti anawo anali kubvutika ndi njara. Ine kenaka ndidafunsa banjalo ngati anachiona choipa kuti ine ndinawatengera ku ndende chifukwa cha uthenga wa Ambuye. Iwo pondiyankha adati: "Ndiribe mau yothokonzera pondibweretsa ine kwa Ambuye. Panalibeso njira ina

imene ine ndikanalandirira chipulumutso."

Nthawi imeneyi kulalikira kunali kobvuta, ndipo chimene tidayamba ndicho kusindikiza mabuku a mau a Mulungu ambiri ndipo pa mwambapo timaikapo chithuzi cha mtsogoleri wa chikomunisiti a Karl Marx ndi cholinga choti achikomunisitiwo aziti ndi mabuku awo pamene mkati mwenimweni mwa mabukuwo timasimbamo za chipulumutso. Mabukuwa adafalikira m'dziko lonsero ndipo adathandiza kwambiri chifukwa a bomalo samadziwa kuti mkati mwa mabukuwo muli nkhani yanji. Timati tikapereka mabukuwo pamene aziwerenga pofika mkati mwa buku ndi kupezamo za Mulungu ndi uthenga wa yesu ife titachoka tiri kutali.

Mdziko la Rumania anthu anali pa mpanipani kwambiri chifukwa zawo zonse zidatengedwa ndi boma la chikomunisitilo. Onse amene anali ndi minda adalandidwa, masitolo, chirichonse chimene munthu amadalira pa moyo wake boma la chikomunisiti lidaalanda anthu onse adabvutika ndi umphawi pafupifupi banja liri lonse linali ndi mnansi ku ndende. "Chifukwa chiyani Mulungu wachikondi alola zoterezi kuti zichitike." Uku kunali kulankhula kwa anthu ambiri m'dzikolo zinthu zitathina. Ngakhale wophunzira aja sikunali kwa pafupi kuti alalikire nthawi ija Yesu atamukhomerera pa mtanda anafuula mau woti: "Mulungu wanga Mulungu wanga mwandisiyiranji ine."

Koma chodziwika nchakuti ntchito idachitika osati chifukwa cha ife koma Mulungu mwini wake. Ndipo mkhrisitu wa chikhulupiriro akudziwa mayankho ake.

Yesu adatiuza za Lazalo wa zilonda wozunzika ndi njara ndipo agaru amanyambita zironda zake koma

pomaliza pa moyo wake angelo adakamuika pa chifukwato cha Abraham.

**Chalichi Chobisikacho Mmene Chidagwirira Ntchito Yake Poyera**

Utumikiwu tinkachitira m'nyumba zobisika, m'nkhalango, m'mapanga ndi m'malo ena otere ndipo m'menemo ndi mmene timagwirizirana za umo tingalalikire poyera. Ndipo zonse timachita modziwiratu kuti izi tikuchitazi ndi ngozi komabe tidayesetsa mpaka kumalalikira m'njira poyera. M'njira imeneyi timatha kulalikira kwa anthu ambiri. Mkazi wanga anali wolimbikira, anthu amasonkhana pa gulayi pa mseu nkuyamba kuyimba nyimbo zabwino ndipo mkazi wanga amafika pamalopo mosaopa nkuyamba kulalikira pamene amabwera a polisi iwo atamaliza atapita.

Masana ena pamena ine ndinali kulalikira kwina mkazi wanga anali kulalikira kwa anthu wogwira ntchito pa kampani ya Malaxa mu mzinda wa Bucharest. Iwowo adalalikira za chipulumutso ndi kuwauza anthu kuti Mulungu ndani. Tsono m'mawa wake, anthuwo sadakondwere ndi makhalidwe omwe anali kuwachita pa kampanipo malinga ndi uthenga umene analandira kuchokera kwa akazi a Wurmbrand ndiye chifukwa cha ichi asilikali a bomalo adapha anthu onsewo ndi futi.

Tinali atumiki a mpingo wobisika koma timagwira ntchito ngati Yohane mbatizi chifukwa tinali kulankhula poyera kwa anthu osiyanasiyana nkudzanso akuluakulu a bomalo za Khrisitu.

Kanthawi kenakake pamene Nduna yaikulu ya dziko la Rumania amatuluka m'nyumba ya boma Akh-

risitu awiri adamuthamangira ndi kumuuza chowonadi cha Ambuye. Ndunayo dzina lake anali Gheorghiu Dej ndipo chifukwa chomuchitira umboni mkuluyo, akhrisituwo adawaponya m'ndende. Koma patapita zaka Ndunayo inadwala kwambiri ndipo idadzakumbuka zomwe adamuuza Akhrisitu aja ndipo pomwepo adagwidwa chisoni ndi kupereka moyo wake kwa Khrisitu. Iyo idamvomereza yesu kukhala mpulumutsi wake ndipo pomwepo ali wodwala adayamba kuchitira umboni. Matendawo anali akulu kotero kuti sanakhalitse anamwalira. Apa ndiye kuti adapita kwa mpulumutsi wake. Iyeyu adapulumuka chifukwa cha anthu awiri aja adamulalikira tsiku limene amatuluka m'nyumba ya boma.

Utumiki wathu unali wokonzeka pa chirichonse chimene chikadachitika koma chachikulu tidafuna kuti uthenga wa Ambuye ufalikire ponseponse ndipo utumikiwu ukugwirabe ntchito yake mpaka pano.

Kawirikawiri timalandira masautso ku utumikiwu bomalo tidalisowetsa mtendere chifukwa munthu amati akatembenuka mtima kumakhala kobvuta kuti abwerere m'mbuyo. Amadziwa kuti munthu akhoza kumuika m'ndende koma chikhulupiriro samachitha kuchiika m'ndende.

China chimene tidachita ndiko kuloleza akhrisitu ena kuti akalowe ntchito ya atolankhani a polisi ndi kumakamvala zomvala za chikomunisiti ncholinga choti iwo azikathandiza ena kumeneko paza moyo wa uzimu komanso kuti azidzatifotokozera zomwe boma likuchita pa mfundo zopitiriza kuzunza akhrisitu. Tsono chifukwa cha ichi tinali kudziwa mmene timalizembera

bomalo pa ntchito yathu ya utumiki.

Nditanyamulidwa nthawi ina pa msewu anakandiika ku ndende ya ndekha. Ndiye pofuna kuti anzanga andidziwe kumene ndinaliri mkhrisitu wina yemwe anali dokotala adakalowa ntchito ya upolisi ndipo komweko ankagwirabe ntchito yothandiza wodwala a m'ndende ndipo nthawi ina anakandipeza ndiri m'ndende ya m'dzenje mwamdima ndiyekhayo amene adandipeza ine patatha zaka zisanu ndi zitatu ndiri m'ndende ndipo ndiye adakauza anthu kunja kuti ndikalipo ndi moyo. Ndipo m'chaka cha 1956 atalowa m'malo a Eisenhower-Khruschev akaidi ambiri adawatulutsa ndipo poti gulu lambiri la iwo anali akhrisitu adapempha boma kuti nanenso anditulutse ndi mmene ine ndinatulukira. Pakadapanda mkhrisitu uja kukalowa ntchito ya upolisi ine sindikanatuluka kapena kudziwika kuti ndiri moyo kapena ayi. Njira imeneyi yolola ena kuti akalowe ntchito ya upolisi idathandiza kwambiri mu utumikiwu. Cholinga sichinali ntchitoyo koma kukadziwa zomwe limachita boma pa mfundo ya akhrisitu.

Anzathu amagwira ntchito m'bomawo amatithandiza potichenjeza pa zina zimene boma limakonza pa chiwembu chofuna kupha utumiki. Nafenso pakati pa anthu opemphera padalinso ambiri wokatinenera ku boma pa zolinga zathu iwowa tinkawatcha a Yudasi ndipo nthawi zambiri timapeza mabvuto chifukwa cha iwowa.

# MUTU 2

Linali tsiku la pa 29 February 1948 nthawi ya m'mawa pa ulendo wanga wopita ku chalichi ndipo ndiri pa njira ndinatengedwa mwadzidzi ndi apolisi. Nthawi imeneyi anthu ambiri wokhulupirira anali kutengedwa mosadziwika bwino ulendo waku ndende. Ndipo nthawi imeneyi ndinangowona galimoto ya polisi itaima kutsogolo kwanga ndipo anthu anayi anatuluka ndi kundigwira kunikankhira m'galimoto.

Kuchokera pamenepo sindidaonekenso mpaka padapita zaka zisanu ndi zitatu. Ndipo palibe ndi mmodzi yemwe amadziwa kuti ndiri ndi moyo kapena kuti ndinafa. Tsiku lina a polisi adapita kukaona mkazi wanga ndipo chimene adachita n'chakuti adambala zobvala ngati za anthu omasulidwa ku ndende ndipo adakamuuza mkazi wangayo kuti ine ndafa ndipo kuti iwo anali nawo ku mwambo woika maliro angawo. Atamva nkhaniyi, mkazi wangayo adasweka mtima ndi kulira. Akhrisitu ambiri wochokera ku mipingo yosiyanasiyana anali kuwamanga, nthawi imeneyi, ndipo anali kutenga aliyense ngakhale anyamata ndi asungwana komanso ngakhale akhrisitu wamba. Ndipo kukhala ku ndende ya mdziko la Rumania chinali chinthu chozunza chifukwa akaidiwo sakhala mu mtendere ayi. Pali zambiri anali kundichitira zoti sindinganene chifukwa

zimandichititsa mantha kotero kuti sindingagone kuti ndiziganiza zimenezo. M'buku lina lake ndidalembamo za zimene ndidakumana nazo ndiri mu ukaidi.

**Mazuzo Osasimbika**

Mbusa wina wake yemwe dzina lake ndi Florescu, ali m'ndende, anakumana ndi mazunzo akulu. Nthawi ina, woyang'anira ndendeyo anaika chitsulo cha phanthi pa moto kuti chifiile psyu ndipo anali kumuotcha nacho mthupi lake mbusayo ndi kumamumenya ndi kumucheka. Akatero amamusiya ndi kukatsekulira makoswe omwe amasowa chakudya ndi kuwalola kuti adutse m'paipi kukalowa mchipinda cha kaidi uja ndipo chifukwa cha njara makoswe aja amamuluma mbusayo kuti azidya thupi lake. Tsono chifukwa cha ichi mzathuyo samagona kuingitsa makoswewo. Amalephere kugona chifukwa amati akati agone, makoswe afika kuti azimudya. Mkuluyu amakhala chachiriri usiku ndi usana mpaka padapita sabata ziwiri. Cholinga cha atsogoleri achikomunisiti chidali choti mbusayu asinthe maganizo ndipo awulule komwe kunali anzake wopemphera. Koma iye sadaulule ngakhale ndi mmodzi yemwe. Ndipo atawona kulimba mtima kwake adakatenga mwana wake wa zaka khumi ndi zinai kubwera naye kundendeko ndi kuyamba kumumenya kwambiri kuti abambo ake asiye kukhulupirira Mulungu. Ndipo ataona zimene amamuchitira mwanayo mbusayu analira nati "Alexander undilole ndinene chimene afuna kuti ndi nene zikundisowetsa mtendere ndi mmene akukumenyeramu."

Mwanayo adayankha abambo akewo motere:

"Musanene zimenezo sibwino nkumpereka ambuye wathu kuli bwino kuti ine ndifere dzina la Yesu. Atamva zonena za mwanayo, asilikali adauma mtima ndi kumumenya mnyamatayo mpaka anatuluka magazi womwe anayenderera m'chipinda cha ndendecho ndipo anafa akulemekeza Mulungu. Ndipo bwezi lathu Florescu ataona imfa ya mwanayo analimbikitsidwa kwambiri pa chikhulupiriro chake.

Unyolo umene amatibvaka m'manja unali wa mingaminga yonga misumali. Ndiye chimachitika nchakuti, ukangogwedeza manjawa misomali ija imalasa kwambiri koma ukakhala osagwedezeka umakhala bwinobwino. Ndiye zimabvuta nthawi yozizira chifukwa timanjenjemera ndiye potero unyolo umatipweteka kwambiri.

Zina zomwe amawachita akaidi ku ndendeko amawamangirira ku zingwe mozyolikitsa mitu yawo pansi akulendewera ndi kumawamenya kwambiri, ena amawaika mu filiji ndipo ine adandiika m'ndende mopanda nchofunda chomwe. Ndiye akaona kuti munthu uja thupi lake likutentha amakamuponyanso m'firiji. Mchitidwe umenewu umachitika nthawi zonse. Ndipo ndikaganiza zimenezi nthawi zina ndimaopa kutsekula firiji chifukwa cha maganizo malinga ndi zomwe timaona tiri m'ndende. Nthawi zina amatiika m'mabokosi okulirapo pang'ono kotero kuti kunali kobvuta magonedwe ake chinanso nchakuti m'bokosimo anakhomereramo timisumali ting'onoting'ono ndipo ndi timene timatibaya thupi lonse osapeza bwino. Zimene amatichita a boma la chikomunisiti ndi zothetsa nzeru ndipo zosayenera kuchitika ku moyo wa munthu.

Amati akayamba kutizuza m'ndende-mo amachita kukondwerera ndi kumafuula kuti "Ife ndife zimbalangondo za satana!"

Sitirimbana ndi thupi kapena mwazi koma ndi mizimu yonyasa. Ndinaona kuti chikomunisiti sichichokera kwa munthu koma kwa mizimu ya satana ndipo ndi Mulungu yekha amene akhoza kuthetsa mchitidwe woipawu. Masiku ena ndimati ndi kaona mmene akuzunzira akaidife ndi mawafunsa kuti kodi amamva bwanji mu mtima mwawo, kodi samva chisoni? Koma iwo pondiyankha amati munthu ukafuna kukazinga dzira umayamba waswa dzira-lo kapena kuti ukamawaza nkhuni osalephera mbalu zogwera kutali. Zimenezi amalankhula zomwe zidalembedwa m'mabuku a Lenin. Tsono powayankha ine ndimawauza kuti mitengo ndi mitengo sikumva kuwawa koma munthu ndi munthu amamva kuwawa. Ndiye kwa iwo munthu yemwe ndi mkaidi amamutenga ngati mtengo kapena dzira kotero kuti alibe nthawi yosamala kapena kumva chisoni.

Kuwuma mtima kwa anthu achikomunisiti, sungathe kumvetsa anthu ake ndi wouma mtima kwambiri. Kawirikawiri amakonda kunena kuti kulibe Mulungu ndiposo kulibe chirango china chirichonse, tikhoza kuchita zirizonse tingafune. Wina adanenapo kuti; "Ndithokoza Mulungu yemwe sindimkhulupirira kuti ndakhala ndi moyo mpaka lero ndikulankhula zoipa ziri zonse zimene ndingathe kulankhula." Malankhulidwe ake onyoza ngati kuti akulankhulayo alibe mzimu. Iwo amalankhulira akaidi pa maso ndi pa maso kuti alibe chifundo ndi munthu.

A Wurmbrand adafotokozera akuluakulu aza chi-

tetezo ku United States kuti zomwe boma la Rumania limachita kwa akaidi nthawi zina zinali zochititsa mantha. Nthawi zambiri akaidi-wo amawamangirira pa mitengo ndikuwagoneka pa simenti ndipo ena nkumawagonera pa mwamba mwankhaza. Kwa akaidi achikhrisitu, amawakodzetsa ndikutenga chimbudzi chawo ndikumawadyetsa kuti ati ndi mgonero ndipo amati akatero woyang'anira ndendezo amakuwa namati, Wonani Khrisitu wanu wokongola kwambiri." Ndipo mbusa amamutuma kuti azipatsa anzake mikodzo ndi chimbudzi kuti azidya ngati ali pa mgonero akuti amachita zimenezo chifukwa chosowa njira yokanira. Ndipo ine ndidamufunsa chifukwa chiyani amalolera zimenezo osati abvomere kufa. Iye pondiyankha anandiuza kuti iye wazunzika nthawi yaitali ndipo mazunzo ake kuposa amene adazuzika nawo Khrisitu.

Zambiri sindingathe kunena chifukwa ndi zowopsya ndiponso zolawula. Izi ndizo abale anu mwa Ambuye akumana nazo ndipo akukumananazobe mpaka pano. Mndende zina za m'dziko la Rumania ndi zodzala kwambiri ndi akaidi kotero kuti wolonda ndende-zo samatidziwa maina. Ndipo panali mbusa wina dzina lake Minal Haimovici iyeyu anali wodabwitsa, alondawo akaitana wina kuti akamukwapule zikoti 25, iye amalolera kulowa m'malo mwa winayo kuti iye ndiye akakwapulidwe. Mkuluyu amachita zimenezi nthawi zambiri. Ndipo akaidi ambiri amamuchitira ulemu chifukwa cha chifundo chake chomwe anali nacho kwa anzake. Ulemuwo sunali wake wokha komaso amachitira Khrisitu. Ndi zambiri zimachitika motero kuti sindingathe kufotokoza zonse. Ndipo

panali ena achikhulupiriro chozama samaopa kuchitidwa chirichonse amalolera ngakhale kufa. Panalinso mtsikana wina yemwe anali wotumikira nafe pa modzi mu utumiki wamtseriwu, iye ankalalikira mosawopa komanso amakonda kukhala ndi ana ndi kumawawauza za mau a Mulungu. Ndiye apolisi atamuona, sadafune kumugwira msanga mpaka pa tsiku la ukwati wake. Ndiye tsiku la ukwati litakwana anthu onse adakonzeka, ndipo iye adavala chovala cha ukwati ndipo ali mnyumba akuchita mwambo waukwatiwo, apolisi adafika ndikukankha chitseko. Kwatibwiyo atawona asilikaliwo adangopereka manja ake kuti amumange ndipo adamumangadi ndikumukokera kunja kwa nyumbayo.

Ndiye asanatuluke kunjako mtsikanayo adacheukira kwa bwezi lakelo, ndi kupsyopsyona unyolo anamumvekawo, ndiye anati; "Ndiyamika mwamuna wakumwamba amene wandimveka unyolo uwu lero pa tsiku la ukwati wanga. Ndithokoza kuti ndiyenera kuzunzika chifukwa cha Khrisitu." Atanena mawuwa, anthu onse ku mwambowo analira pamodzi ndi Mkwati yemweyo. Zinachitikazo zinali zomvetsa chisoni chifukwa anthuwo adadziwa kuti mtsikanayo akazunzika m'manja mwa asilikali achikomunisiti. Mkaziyo adadzammasula patatha zaka zisanu ndipo anali atasakazika ndipo amaoneka ngati wa zaka zambiri pamene iye anali wa mng'ono zonsezo nchifukwa cha mazunzo anali nawo ku ndendeko. Iyeyu atatuluka ku ndendeko adakampezabe mwamuna uja akumudikira.

**Mmene Chinapusa Chimakhalira**

Azathu aku maiko akuzambwe ku Ulaya anamvapo

za chinapusa pa nthawi ya nkhondo ku Korea ndiponso ku Vietnam. Ine ndakhala ndi kupusitsidwa mnjira yotero. Ku mupusitsa munthu ndi chinthu chimodzi chowononga maganizo a munthu.

Pa zaka zambiri amandikhazika pansi mokwana maola 17 kumamva zonena za mtundu uwu:

Chikomunisiti nchabwino!
Chikomunisiti n'chabwino!
Chikomunisiti n'chabwino!
Chikomunisiti n'chabwino!
Chikhrisitu n'choipa!
Chikhrisitu n'choipa!
Chikhrisitu n'choipa!
Chisiyeni!
Chisiyeni!
Chisiyeni!
Chisiyeni!

Akhrisitu ambiri amandifusa kuti zidatheka bwanji kuti sindinapusitsidwe ndi mauwo omwe ndimawamvera tsiku ndi tsiku. Ine powayankha ndinati kupusitsidwa sikungatheke ngati mtima wako sutsazira zoterozo pamene mutu wako ukumva zinthu zosayenera mtima wako usamazigwiritse ntchito. Ukaika chikondi pa Khrisitu susunthika ngakhale mabvuto aoneke chotani. Mulungu adzatiweruza pofanizira ndi chikondi chomwe tawonetsera kwa iye. Ine ndine mboni kwa akhrisitu aku ndende za chikomunisiti kuti ndi anthu achikondi ndipo amakonda Mulungu komanso anzawo.

Mazuzo kwa akaidi m'ndende zaku Rumania ndi yosasimbika ndipo palibe nthawi yopuma. Ineyo m'ndende ndidaona zoopsya kwambiri kuti ngakhale

ndi mayesetsa kuwauza wotiyang'anirawo zakufunika koti asinthe m'chitidwe woipawu ndi kulapa machimo awo sanali kundimvera. M'malo mwake amapitiriza kundizuza. Ndikakomoka amandisiya kanthawi ndipo ndikatsitsimuka amandiyambiraso kundimenya. Nthawi imeneyi akaidi ambiri ankafa ndi mazuzowo. Ine m'ndende zambiri zimene ndagonamo, amandithyola nthiti ndi mafupa a msana wanga kuonjezera apo, amandiotcha ndi zitsulo za moto ndi kumandigwaza ndi mipeni m'thupi langa. Moti pano ndikamba pano ndiri ndi zipsyera zokwana 18 za zironda zikuluzikulu.

Madokotala aku Oslo ataona kubvulala kwa nthiti zanga ndi mapapo ndi zironda zomwe ndinali nazo, adandiuza kuti ndikukhala ndi moyo chifukwa cha chisomo, ndikadafa kale.

Ndi zowona ine Mulungu adandisiya kuti ndituluke ndi moyo kuti ndidzachitire umboni zoopsya zimene akhirisitu akuziona m'maiko ena ndikutinso ndidzalankhule kuti tizikumbukira mpingo wa akhrisitu umene ukugwira ntchito yake mobisala; kulimbikitsa anzathu ali mndende, ndi ena onse akumvutika chifukwa cha dzina la Yesu.

### Ufulu Pang'ono---Kenaka Nkumangidwanso

M'chaka cha 1956 adandigwiranso ndikunditsekera m'ndende zaka zisanu ndi zitatu ndi theka. Pa nthawi imeneyi, ndidazuzika ndipo ndi nthawi imene ndikadafa ine chifukwa cha mazuzo omwe amandichita pa moyo wanga. Ndi mamenyedwa mosandisamala ndidaonderatu ndipo samandiwerengera ngati munthu koma ngati chirombo cha kuthengo. Pa kanthawi kena

adandilola kuti ndikalalikire pa kamphindi kochepa monga ngati kundiyesa kuti kapena ndasiya. Ndiye potha pa kulalikira, ndidakhala ngati ndawaputa. Adandiuza kuti ndisadzalalikirenso kapena kupezeka pa ntchito ina iriyonse yokhudza chipembedzo. Izi ndi zomwe ndinkaphunzitsa ku mpingo kwanga kuti zinthu zikafika poyipa ndi bwino kukhala chete. Tsono chifukwa chosawayankha apolisi anapsya mtima ndi kundidzudzula chifukwa chiyani sindimayankha. Ine ndidawauza kuti zinthu zimasintha ndidawauza kuti anthu sadyera mfumu imodzi nthawi zonse. Iwo atamva zonena zangazo adafuula kuti zimene ndimalankhulazo ndi za bodza. Kuchokera pomwepo sadandi lolenso kulankhula pa gulu. Koma wachake ndi wachake, izi zitatha ndidapitiriza mwamtseri kumakalimbikitsa utumiki wanga uja wamtseri ndipo mkazi wanga ndiye amakonda kundiika ku mbuyo kuti ndisamadziwike.

Masiku ena ndi mayesetsa kuwalimbikitsa wokhulupirira anzanga kuti asabwerere m'mbuye ndipo powalimbikitsapo ndinali kuwasonyeza mabala a m'thupi mwanga kuti zoterezi zizitirimbikitsa pa ntchito ya Mulungu. Ndakonzanso njira za momwe akhrisitu angamakumanirane pofuna kuti ntchito yonse yofalitsa uthenga iziyenda mofulumira. Ine ndinali kuwauza anzanga kuti ngati munthu sangathe kuwona dzanja la Mulungu likugwira ntchito momwemonso akuluakulu achikomunisiti sangathe kudziwa zimene akhrisitu akuchita pakati pawo.

Patapita nthawi, pokhala apolisi anali kundiwendawendabe adafikaso pondigwira koma ulendo umenewu anamanga ine ndekha ndikusiya mkazi

wanga. Ulendo uwu adandimanga zaka zisanu ndi zitatu nkudzano miyezi isanu ndi umodzi. Nditamaliza zaka zimenezi ndinakhala kunja zaka zitatu ndiri pa ufulu. Koma zinthu sizidasiyire mpopo adadzanditengaso ndikudzandimanga zaka zisanu ndi theka. Nthawi imeneyi inali nthawi yosautsa kwambiri pa moyo wanga ndipo thupi langa linali lomvetsa chisoni. Komabe ngakhale kunali tero, ndidalolera kufa chifukwa cha dzina la Ambuye motero kuti ndimapitirizabe kulalikira kwa akaidi anzanga koma mobisa.

## Ife Tinatsimikiza Zolalikira Uthenga---Asilikali Nawonso Anatsimikiza Zotimenya Ndi Kutizunza

Chinali chinthu choletsedwa kulalikira kwa akaidi azathu. Kotero kuti adaika lamulo kuti ngati wina apezeka akufotokoza mau a Mulungu kwa mzake munthuyo ayenera kumenyedwa kopanda nako chifundo. Koma ngakhale panali lamuloli, enafe tinalolera kulandira chirangocho chifukwa cholalikira uthenga ndipo mwa ichi tonse tinagwirizana; asirikali mbali yawo yopereka chirango. Ife mbali yathu yolandira chirango. Asirikaliwo anali okondwa pomatimenya pamene ifeso tinali osangalala popitiriza kulalikira uthenga ndiye mbali zonse panalibe woluza aliyense anali wosangalala malinga ndi pa ntchito yake. Nthawi ina yake mzanga ali mkati kulalikira, adabwera asirikali, ndi kumumenya kwambiri kumguza ndikumgwetsera pansi pa simenti anthu akuwona. Ndipo adapitiriza kumumenya mpaka adatuluka magazi mthupi monse atatemedwatemedwa. Atamusiya, iye anakhala pang'ono ndipo mwamwayi

anadzuka nadziongola koma akumvabe kupweteka thupi lose ndipo anasasa zomvala zake napitanso ku gulu lija, nati, "Tandiuzani ndinasiyira pati pamene ndimalalikira. "Kwa ine zotere zinkandichititsa chidwi." Adatero a Wurmbrand kuchitira umboni ku anthu aku maiko ena, makamaka kwa akhrisitu.

Ambiri mwa alalikiwo anali anthu wamba osati abusa koma anthu odzazidwa ndi mzimu woyera ndipo mitima yawo imagonera pa mau a Mulungu chifukwa sichinali chapafupi kulalikira uthenga pa nthawi yamasautso otere ngati omwe anali nawo m'ndende zaku Rumania. Chifukwa chimachitika nchakuti ankampeza munthu akulalikira amammenya kotheratu pafupi munthuyo kufa ndiye sichinali chibwana ayi.

Ku ndende ina ku Gherla kunali mkhrisitu wina dzina lake Grecu, iyeyu adapatsidwa chirango choti adzakhala ali kumenyedwa mpaka atafa nako. Chirangochi chidapitirira mpake masabata angapo.

Iye anali kumenyedwa kwambiri ndipo nthawi zina anali kumumenya miyendo, nthawi zina mbali zina za thupi koma ulendo wina adadzamumenya pa musi pa nchombo ndipo kuti akhale bwino dokotala adachita kumubaya jekeseni. Kuti thupi lake likhale bwino adayamba kumukozera chakudya chabwino kuti thupi lake likhalenso la mphamvu. Tsono chirango chija chidapitirirabe chomamumenya kufikira potsiriza pake anafa ndi kumenyako. Kumenya koteroko kunali kwa pang'onopang'ono koma kwa kupha. N'chifukwa chake pomaliza mkuluyu adamwalira. Iye amene amapereka chirangocho ndi m'modzi wa bungwe la Central Committee ya chikomunisiti ndipo dzina lawo ndi a Reck.

A Reck-wo amati ali ndi mphamvu yopereka moyo kapena kupha ndipo ena mwa azawo anatengerako kulankhula kotere. Iwo amanena kuti Mulungu amene ali kumwamba alibe mphamvu yokusungani koma zose ziri kwa ine. "Nkafuna kuti mufe mufa kaya kuti mukhale ndi moyo mukhala ndi moyo.. Ine ndine mulungu." Ankatero kunyoza akhrisituwo.

A Grecu pamene anali m'mabvutowo, adawayankha a Reck pa zimene amalankhula kuti: "Ndi zowona ndinu mulungu koma simudziwa za umulungu kunena m'njira yake yeniyeni ndi gulugufe malingana mphalabunguyo, ikakula bwino ndikufika pa mlingo wolongosoka. Koma kupanda kutero, imafabe ngati mphalabungu." A Grecu anali kuwauza asilikali aja kuti iwo sadalengedwe kuti azidzanzuza anthu anzawo ayi, koma kuti adzachite chifuniro cha Mulungu. Ichi nchifukwa chake Yesu adauza AYuda kuti ndi milungu chifukwa adalengedwa nchifaniziro cha Mulungu. Ena adachitapo izi muchita inu zomazuza anthu monga mtumwi Paulo koma adadziandikira kuti zimene anali kuchitazo zinali zoipa ndipo sichinali chifuniro cha Mulungu. Ndipo uyambira nthawi imeneyo adayamba kuchita zofuna za Mulungu. Khulupiririrani a Rech ntchito yanu siyoti muzizuza anthu ayi koma kuchita chifuniro cha Mulungu chifukwa inu mudalengedwa n'chifaniziro chake. Koma a Rech samasamala zonena mbaleyo amangowona ngati zopanda ntchito.

Monganso momwe zidachitikira kwa Paul kuti ngakhale Stifano anali ku muuza Paul za Mulungu Paul sadazigwiritse ntchito mpaka Stefano adaphedwa. Koma tsiku lina nkhani imeneyi idagwira ntchito mu

mtima mwa a Reck ndipo adadzadziwa ntchito yawo yoyenera kuchita pa moyo wawo.

Chodabwitsa timachiona ndi chakuti pamene tinali kumenyedwa, zimaoneka ngati omenyedwawo sindife matupi athu amalamulidwadi ndi mzimu woyera kotero kuti sitimadandaula ayi.

Kaburedi kamene timalandira pa sabata kanali kakang'ono ndi supu wachabechabe. Ndiye ife pofuna kupereka cha khumi chathu timatenga kaburediko ndi kumenyako ndikupatsa akaidi anzathu amene amaoneka ngati ofoka kwambiri kusiyana ndi ife kuti adye ndipo timachita izi kusonyeza cha khumi chathu kwa Mulungu.

Mkhrisitu asanaphedwe, amamupatsa mwayi woti awonane ndi mkazi wake ndikulankhula zomwe angafune kunena. Ndipo polankhulapo ankakonda kunena motere: "Mkazi wanga dziwa ichi kuti ine ndirikufa chifukwa choti ndiwakonda iwo amene akundipha. Iwo sakudziwa chimene akuchita. Ndiye ndikupempha kuti usakhale nawo ndi mangawa chifukwa choti andipha upitirize kusonyeza chikondi pa iwo. Zikomo tikakumana kwa Atate kumwamba." Pakumva mau awa polisi wina adachita chidwi kwambiri ndipo zinachitikazo zidamupangitsa kuti iye asinthe moyo wake ndi kukhala mkhrisitu.

Mndende yaku Tirgu-Ocna munali mnyama ta wina dzina lake Matchevici yemwe anali ndi zaka 18. Mnyamatayu chifukwa cha mabvuto aku ndendeko anayamba kudwala chifuwa chokoka mapapo. Ndipo makolo ake podziwa kuti nthawi ina iriyonse akhoza kufa, anamutumizira mankhwala yoti azimwa ali kun-

dendeko. Tsono ofisala yemwe amamuyang'anira, anamuitana ndi kumuuza za phukusi la mankhwalawo. Iye adati ndi wokonzeka kumupatsa mankhwalawo pokhala kuti anali mwana ngakhale kuti sikuloledwa mkaidi kulandira mankhwala. Koma chinthu chimodzi adapempha kwa m'nyamatayo ndi chakutia aulule anzake womwe amalalikira uthenga wa chikhrisitu. Iye adati akatero zimuthandiza kuwauza akuluakulu ake chifukwa chiyani anamupatsa mankhwalawo.

Mnyamatayo poyankha adati kwa iye ifa alibe nayo kanthu sangalole kuti awulule anzake chifukwa choti awombole moyo wake "kuli bwino kufa." adatero mnyamatayu. "Ofisalayo adamuyamika mnyamata-yo chifukwa cha mau ake. Tsono ofisalayo adati chabwino amupatse maina ya anthu amene sagwirizana naye chifukwa cha utumiki wake. Iye adayankha kuti, iye adaphunzitsidwa kuti azikonda m'dani wake. Iwo amene amatinenera ife zoipa akhale chocho koma sindingawabwezere choipa. Iye adati ntchito yake ndi kuwapempherera ndikuwafunira zabwino zonse. A Matchevici adalowa m'chipinda mo kuchokera kwa ofisalayo ndipo sipadapite nthawi iye mkumwalira ndipo pamene anali kufa ine ndinali pomwepo. Anali kufa uku akuyamika Mulungu.

Munthu waumphawi akakhala okonda nyimbo amayesetsa ngakhale akhale ndi k1.00 kupereka kwacha yakeyo kuti amve nyimbo. Ndipo kwa iye alibe nazo kanthu kuti alibe ndarama iriyonse: Chachikulu kwa iye nkuti wamva nyimbo yomusangalatsa. Ichi ndi chimodzimodzi kwa ine palibe kanthu kuti nthawi yanga yaitali ndakhala ndiri m'ndende koma m'ndendemo ndaphun-

ziramo zambiri. Ndakumanamo ndi anthu odzipereka pa ntchito ya Ambuye kufikira ifa, ndamva maumboni osiyanasiyana komaso kulandira zirango zoopsya zimene nkale lonse sindimazidziwa ndipo zimenezi zidalimbikitsa chikhulupiriro changa. Zinthu zosatheka ndi anthu amu mpingo wathu wakabisira zinali kutheka ndi Mulungu. Utumiki wathuwo ndi wukonda kwambiri ndipo ndinkonda Khrisitu powona zimene wakhala akuchita nane pa moyo wa utumiki wamtseliwo.

**Chidachitika N'chiyani Kwa Akazi Anga Ndi Mwana Wanga.**

Pamene ine ndiri ku ndende, sindinkadziwa kuti akazi anga ali kuti kapena mwana wanga ali kuti. Koma patapita zaka zingapo, ndidava kuti mkazi wanga ali m'ndende. Chirango chomwe amalandira azimai ku ndende chinaliso choopsya ndipo amawagwiritsa ntchito zikuluzikulu ngati za amuna. Akakhala atsikana, amangowagwiririra kuchita nawo zoipa ndi kuwazuza mmene angathere. Nthawi zina azimaiwo amawatenga kukawaponya pa dziwe lotchedwa Dnube nkumawawedza ngati akuwedza nsomba ali onyowa ndi kumawaseka ndipo mkazi wanga anali mmodzi wochitidwa zoterozo. Mkazi wangayo kuti akhale ndi moyo amamudyetsa udzu ngati ng'ombe ena amadya njoka ndi makoswe. Inali nthawi yobvuta kwambiri kupanda kutero akadatha kufa ndi njara. Ndi zambiri zimene adakumana nazo m'ndende azimayi-wo chifukwa cholandira mpulumutsi Yesu Khrisitu.

Mwana wanga nthawi imeneyi amangokhalira kuyendayenda m'njira kusowa chochita. Bambo ake ali

ku ndende amayi ake naonso ali ku ndende. Chokondweretsa mwanayu pa msikhu wake onse anali okonda mau a Mulungu. Nthawi imene ife makolo ake tinali ku ndende iye anali ndi zaka zisanu ndi zinayi ndipo pa msikhu wake adakumana ndi masautso ambiri kotero kuti adayamba kuganiza za mmene angagwirire ntchito kuti azipeza ndarama zomadyera. Mwanayu zimene adakumana nazo, anzake a msikhu wake sadakumane nazo.

Kuthandiza banja losiidwa chifukwa choti makolo ake ali ku ndende zimaletsedwa. Ndipo chifukwa cha ichi ana ambiri amene makolo awo anali ku ndende samaloledwa ndi wina aliyense kuwathandiza. Ndipo ngati wina apezeka akuthandiza anawo amamangidwa ndi kumenyedwa kwambiri. Tsiku lina mzimayi wina adayesa kuti athandize mwana wathu, adamumenya kotero kuti lero lina ndi opunduka. Winanso yemwe adamutenga mwana wathuyo adamugwira ndikumuika mndende zaka 8 ndipo komweko anamugwerura mano onse ndi kuthyola mafupa a m'thupi lake lero sayenda.

## Mihai Ika Chikhulupiriro Chako Pa Yesu

Atafika zaka khumi ndi chimodzi, Mihai adayamba kudzigwirira ntchito yoti azipeza thandizo pa moyo wake. Tsono patatha zaka ziwiri, mwanayu adapatsidwa mwayi wokaona mayi wake ku ndende. Ndipo atafika kumeneko mayi akewo amawaonera pa windo ya mawaya ndipo inali nthawi yake yoyamba sadakhulupirire kuti ndi amayi ake chifukwa anali woonda ndipo thupi lawo linali losawoneka bwino chobvala chaku kaidicho chinalinso chakuda. Mayi-wo atangomuwona

mwanayo adanena mau awa: "Mwana wanga Mihai ika chikhulupiriro chako pa Yesu." Mayi atangonena mauwa alonda adawaguza mopsya mtima, ndipo mwanayo powona zinachitikazo adalira kwambiri ndipo adati ngati anthu akhoza kumukonda Yesu m'mabvuto ngati awa ndiye kuti ndi zowonadi Yesu ndi mpulumutsi ndipo moyo wa mwanayo udatsimikiza kutsatira Yesu. "Pa zimene ndawonazi zakwanira kwa ineyo." Adatero mkulankhula kwake.

Mwanayo ku sukulu anali kuchita bwino kwambiri pa maphunziro ake ndipo nthawi ina aphunzitsi adamupatsa tayi chifukwa chochita bwino. Koma iye adawauza aphunzitsi poyera kuti sadzamvala tayi ya anthu amene akusunga makolo ake m'ndende. Akuluakulu atamva mauwo adamuchotsa sukulu ndipo adatha chaka osaimba. Chaka chinachi adakalowaso sukulu ndipo pa nthawi imeneyi sadaulule kuti ndi mwana wa m'khrisitu ndikuti makolo ake ali ku ndende.

Tsiku lina pa phunziro la chimangiriro, iye adalemba za kusiyana kwa baibulo ndi chikomunisiti. Iye adati iwo analemba kuti baibulo sirakanthu ndipo ndi lopanda pake adalemba chifukwa chosalidziwa bwino baibulo. Iye nkulemba kwakeko adati baibulo silidalekane ndi phunziro la sayasi. Iye atamupeza kuti walemba zotere adamuchotsa ndipo sadaloweso sukulu mpaka padatha zaka ziwiri.

Pa nthawi ina yake adamulola kuti akakhale nawo pa sukulu ya seminare ndipo kumeneko amawaphunzitsa za chikomunisiti motsatana ndi zimene adalemba a Karl Marx paza chiphunzitsocho. Mwanayu adalephera kumvomereza ndiye zotsatira zake zinali zongu-

muchotsa pa sukulu ya chikomunisiti. Iyeyu kuti akhale nawo mwayi woti aphunzire samaulula kuti ndi mwana wa a Wurmbrand omwe anali ku ndende. Ndipodi anali kutsutsana nawo ma polofesala m'kalasimo ndipo amangomuchotsa. Mihai analiso kubvutika ndi njara chifukwa monga tanena kale kuti ana omwe makolo awo adamangidwa chifukwa cha chipembedzo samawalola kuti athandizidwe pa chirichonse.

Zina zomwe ndingakuwuzeni nzakuti, mbale wanga wina wake adamumanga chifukwa chopezeka kuti anali mmodzi mwa wogwira ntchito ya Ambuye. Tsono iye adasiya mkazi wake ndi ana asanu ndi mmodzi. Ndipo pa anawo panali ana akazi awiri wina wa zaka 17 ndi wina wa zaka 19. Ndiye bvuto lomwe linalipo ndi loti atsikana akuluwo sanali pa ntchito komaso kunali kobvuta kuti apeze ntchito chifukwa anali ana omwe kholo lawo lidamangidwa chifukwa cha Khrisitu. Tsono chomwe atsikanawo adachita ndi kulowa ntchito ya uhule kuti azipeza ndarama zogulira chakudya pa nyumba chifukwa amayi awo anali wodwaladwala komaso azing'ono awo anali ang'ono kwambiri. Ndipo atayamba uhulewo, mbale wawo wa zaka khumi ndi zinayi adaipidwa nazo ndikuchoka pa khomopo. Ndiye nthawi inakwana bambo uja anatuluka ku ndende ndipo pofika ku nyumba-ko adakhumudwa ndi zochita ana ake akaziwo. Iye adati: "Mulungu ndi bwezereni ku ndende chifukwa sindingathe kumaona zoterezi." Pemphero lake lija lidakwaniritsidwa ndipo bamboyo adamumanganso. Kenaka atsikanawo adalowa ntchito ya polisi yautikitiva ndipo adasiviratu uhule. Apa tisangoti anali atsikana woipa nthawi zina

zinthu zimachitika chifukwa chosowa thandizo pamene kuli kulakwa kapena kulephera kwa makolo pa banjapo koma zidachitikira atsikanawo pamene bambo wawo ali ku ndende. Atsikanawo sichidali cholinga chawo koma nanga inu amene makolo muli pafupi muti bwanji za nkhaniyi.

# MUTU 3

Pa zaka zimene ndinali mu ukaidi zokwana khumi ndi zinayi, zinandiiwalitsa maonekedwe a baibulo kapena buku lina liri lose. Kulemba nako, ndidayamba kuiwala chifukwa cha zomwe zinali kuchitika pa moyo wanga ku ndendeko. Koma tsiku lina lake ndididadzakumbukira za nkhani ya Yakobu yemwe anakagwira ntchito kwa Rakelo zaka khumi ndi zinayi komabe kwa iye zinaoneka ngati zaka zochepa chifukwa amamukonda Lakelo. patapita zaka 14-zo ndidatuluka mu ukaidi chifukwa cha msonkhano womwe udachitikira ku Amerika wokambirana za akaidi a m'dziko lonse la pansi. Nditatuluka ndidakamupeza mkazi wanga akundidikirabe pa zaka khumi ndi zinayi zapitazi. Kuchokera apo tidayamba moyo watsopano chifukwa byuto lidalipo nlakuti munthu akamumanga amamulanda zake zonse nchifukwa chake tidachita kuyambiraso kuti tipeze zotithandiza pa banjapo. Azibusa ndi ena otere omwe adawatulutsa mndende anali kuwapatsa machalichi ang'onoang'ono a m'tauni ndipo ine adandipatsa chalichi chimene chidali mtauni ya Orsova chomwe chidali ndi anthu 35 okha. Pondipatsa mpingowo akuluakulu achikomunisiti kumeneko adandiuza kuti nambala ya anthu ndi 35 ndipo kuti asadzaone atakwana 36 chifukwa zikadzatero zinthu zidzaipa komaso adandiuza kuti ana asamakhale pafupi ndi ku chalichiko. Akuluakuluwo adandipemphaso kuti ndikhale mtola nkhani

wawo womakawauza zochita anthu ena. Umu ndi mmene amafunira kuti mpingo uzigwira ntchito yofuna boma la chikomunisiti. Ine ndidadziwa kuti ngati ndiyamba kulalikira ku mpingoko anthu ambiri akadatembenuka ndiye sindidafune kutero. Chimene ndidachita ndikulimbikira ku utumiki wamtseri uja ndipo ndimawauza zonse zochitika kwa akhrisitu ali mndende. Nthawi imene ine ndinali m'ndende chalichi chobisikacho sichinaime m'malo mwake chinapita patsogolo kotero kuti akhrisitu ambiri aku Amerika anali kutumiza thandizo ndi kutipempherera. Pamene ndinali kupuma m'nyumba ya mzanga wina, adandiuza kuti anthu ambiri ku maiko aku Ulaya sadatiiwale kapena kutisiya.

Nthawi imeneyi anzathu amaiko ena adakoza bungwe lowona za thandizo lopereka kwa mabanja amene akubvutika chifukwa choti anansi awo ali ku ndende. Ndipo bungweli limagwira ntchito yake mosaonetsera kuopa kuti mabanja othandizidwawo angakhale pa mabvuto. M'nyumba ina yake ndidakapeza anthu 6 omwe adadza ncholinga chodzapereka thandizo ndipo pocheza nawo adandiuza kuti iwo akufuna munthu wina amene wakhala m'ndende zaka 14 ndipo ine nditawauza kuti ndineyo sadakhulupirire chifukwa adayembekeza kupeza munthuyo ali ndi moyo wowombwa wachisoni osati monga mmene ndimaonekera ine. Zinthu zidayamba kusintha azathu amaiko ena amatitumizira mabaibulo kotero panalibe bvuto ku mbali ya mabaibulo.

Pamene tinali muukaidi boma-lo limatipusitsa (brain washing) Kumatiuza kuti palibe wina amatiga-

nizira kapena kutikonda. Zoterezi amazinena kawirikawiri. Koma tsopano tidadziwa kuti chinali chiphamaso kutipusitsa. Ndi ambiri amatikumbukira ndi kutipempherera monga anzathu aku Ulaya ndi ku Amerika. Iwo ankafika nthawi ya usiku ndi kulowa m'nyumba zathu ndikumatipatsa mabuku koma asilikali a bomalo osadziwa kapena kupenya. Banja langa likadakhala lobvutika pa nthawi yaitali pakadapanda abale aku maiko akunja kutitumizira zinthu zofunika pa moyo wathu. Kwa ife, kulandira mlendo wakunja ku dziko lina timaona ngati mngelo wotumizidwa ndi Mulungu kudzatichezera. Malinga ndi momwe ntchito imakulira ya chalichi chobisika, chikanakhala chapafupi kuti ndinjatidweso. Mwamwayi panali mabungwe awiri achikhrisitu monga Norwegian Mission ndi Hebrew Christian Alliance amene adasonkha ndarama zokwana £2,500 zoti ine ndi choke m'dziko la Rumania.

## Chifukwa Chiyani Ndidachoka Ku Rumania

Ine ku Rumania sindikanachokako koma anzanga a chalichi chobisika ndiwo adandiwumiriza kuti ndichoke kupita ku maiko afulu wa chipembedzo kuti ndizikawalankhulira azanga a m'chalichi chobisika ku Rumania. Ndipo pofotokozera akhrisitu aku maiko-wa ndinali kuwauza kuti ngakhale ine ndiri kuno, moyo wanga ndi mtima wanga ziri kwathu ku Rumania komwe akhrisitu akuzuzika chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Ndisanayamuke m'dzikolo, boma lo lidandiitana kundiuza kuti ndarama zafika zoti ine ndichoke m'dzikolo. Nthawi imeneyi nkuti dziko la Rumania litayamba kumagulitsa akaidi kuti akhoza kuchoka m'dzikolo.

Nditakonzeka za ulendo wangawo, akuluakulu a bomalo adandiitana ndikundiuza kuti ndikhoza kupita kwina kuli konse, ndipo kumeneko ndiri ndi ufulu wolalikira mau a Mulungu. Koma adati ndisakayese dala kulankhula za bomalo kapena zimene iwo amawachitira pa nthawi anali m'ndende. Akuluakulu-wo adanenetsa kuti ngati ndikayerekeza kunena za bomalo adzachita zotheka kundigwira mwanzeru ndikundipititsa ku Rumania. Iwo adapereka zitsanzo za anthu amene amawaipitsa kunja kwa dzikolo ndipo anthuwo adakawatenga kuwabwezera ku Rumania. Iwo adati ali ndi ufulu wopereka ndarama kwa kagulu kali konse koti kachite zotheka kundigwira. Iwo adati njira ina angachite ndi kupeka bodza loti ine ndimakhala ndi mtsikana ngati bwenzi langa ndi cholinga choti utumiki wanga ufe. Komaso akhoza kupeka bodza loti ine ndidaba ndipo ndine wakuba zosezo kuyesetsa kuononga moyo wanga wauzimu. Iwo anati atachita zimenezi zikhonza kugwira ntchito chifukwa anthu aku Amerika sakhala kukhulupirira zinthu.

Ndipo ndi zowona ambiri amene adapita m'maiko ena akutali adakawatenga mosadziwika bwino mwachitsanzo m'ndende ndinali ndi Orthodoz bishop Vasile Leul yemwe adakamtenga ku Austria kumene amakhala. Koti zimene amalankhula sikunali kuopsyeza chabe ayi ankanena zowona.

Atamaliza kundiuza zimenezi ndidachoka kupita ku Ulaya. Boma la Rumania lidakhulupirira kuti ine ndikapita kwina sindikanena china chirichose monga adachitira ena. Boma la Rumania limakonda kupusitsa munthu ndipo limakhulupirira m'chitidwe umenewu.

Pa mwezi wa December m'chaka cha 1965, tidakoza ulendo wathu. Koma ndisananyamuke chomaliza chimene ndidachita ndiko kukaika maluwa pa manda ya mkulu amene adandiika ine m'mabvuto kuti ndiyambe kumangidwa ndi kuzuzika. Ndidachita zimenezo pofuna kusonyeza chimwemwe changa kwa Yesu ndi achikomunisiti. Inde ndi madana ndi chikomunisiti koma anthuwo ndi wakonda. "Ndimadana ndi chimo koma wochimwayo ndimmankonda." Makomunisiti amapha akhrisitu koma sangathe kupha chikondi chimene anali nacho anthu omwe adaphedwa ndi makomunisitiwo.

# MUTU 4

Ayuda amatsimikiza ndi kudziwa kuti makolo awo adawomboredwa kuchokera m'dziko la Aigupto. Ndikuti pamene Aigupto-wo anawatsatira onse adamira m'nyanja yofiwira. Angero akumwamba anawathandiza a Yuda poyimba nyimbo zothokoza Mulungu wawo chifukwa chowamenyera nkhondo powawombola m'manja mwa Aigupto. Koma pa nkhaniyi Mulungu anati kwa angero, a Yuda akukondwera chifukwa chowomboledwa ndi kuwachotsa m'dziko la Igupto. Ndipo Yehova anauza angelo kuti ayenera kukhala wozindikira kuti Aigupto nawonso ndi anthu anga. Ndipo ndimva nawo chisoni chifukwa chopita ndi madzi.

"Ndipo pokhala Yoswa ku Yeriko anakweza maso ake napenya, ndipo panaima munthu pandunji pache ndi lupanga lache losolola m'dzanja lache. Namuka Yoswa kuli iye nati, umvomerezana ndi ife kapena ndi adani athu?" (Yoswa 5:13) Kukadakhala kuti amene adamuona Yoswayo kuti anali munthu ngati ife akadayamnkha motere, "Ndadzera iwe." Kapena akadati, "Ndadzera mdani wako." Kapenaso mwina akadati "ndiribe mbali." Mayankhidwe wotere ndiwo mayankhidwe a umunthu. Koma iye amene adakumana ndi Yoswayo ndi wochokera mbali zina osati pano pa dziko la pansi nchifukwa chake adayankha mwa njira ina yosamvetsetseka. Mawu adalankhula munthu ameneyu anali wosazindikirika monga mmene adayankhiramo

kuti, "Iyayi" kodi nanga pamenepa pamatanthawuza chiani? Kuyankha kunatanthauza kuti amachokera kumwamba kumene sakhalira mbali ya munthu zinthu zikabvuta. Kwa iwo ndi kusonyeza chisoni cha chikondi. Pa nkhaniyi ndifuna kunena kuti pa mkhalidwe uno wa dziko la pansi akhrisitu azirimbana ndi chikomunisit mozindikira ichi kuti akhrisitu ndi ana a Mulungu wonyamula chiyero pakati pa anthu ena. Ichi nchifukwa chake mazuzo ndaona ine ku ndende sindikhala nawo ndi chiwembu chodana ndi anthu woyendetsa chikomunisiti. Iwo ndi anthuso a Mulungu ndiye zitheka bwanji kuti ndikadane nawo kapena kukondana nawo. Iwo adana ndi Mulungu Koma ine ndimkonda Mulungu.

Zowona ndikanafusidwa ine kuti kodi uli mbali yachikomunisiti kapena ayi? Yankho langa likanakhala losalongosoka. Ndikanati, ine sindichifuna chikomunisiti ndipo ndidzalimbana nacho mpaka chitatha. Koma taganizani ndiri ku dzanja la manja la Khrisitu kumene machitidwe ake ndi ena osiyana ndi kuno ku dziko la pansi. Kumwamba anthu onse ndi ake a Mulungu kuleka machimo omwe amatirekanitsa ife ndi Mulungu. Kumeneko ntchito yawo nkuyesetsa kukathandiza aliyense kuti akakhale mwana wa Mulungu. Nchifukwa chake ine moyo wanga ndi woti ndi falitse uthenga kwa aliyense kuti tonse tikalowe mu ufumu wa Mulungu.

Khrisitu amawakonda makomunisiti; Iye amatiuza kuti amakonda munthu aliyense ndi chifukwa chake adapereka fanizo la munthu uja anali ndi nkhosa makumi khumi ndipo itasowa imodzi, adalolera kusiya zina zonse ndi kukafuna yosokerayo. Wonse wopulu-

mutsidwa amanena chimodzimodzi potsatira mau a Mbuye wathu Khrisitu kuti tizikondana wina ndi mzake. Mwachitsazo a Macary woyera nthawi ina adati? "ngati mutnhu akonda anthu onse ndi kuda munthu mmodzi ndiye kuti iyeyo si mkhrisitu chifukwa sadakwaniritse chikondi cha Yesu. Nawonso a Augustine woyera amaphunzitsa kuti kapena nditi amakonda kunena kuti "Anthu onse pa dziko la pansi akanakhala osachimwa ndi kuti mmodzi yekha ndiye anali ndi uchimo Yesu akadabwerabe kudzamufera pa mtanda. Apa tikhoza kuwona chikondi chomwe akhrisitu tiyenera kukhala nacho. Tiyenera kukonda aliyense ngakhale makomunisiti koma tidane ndi chikomunisiticho osati anthu ayi, Chiphunzitso cha Yesu ndi chomveka chakuti tizikonda aliyense.

Ine ndawona akhrisitu akuzuzika m'ndende atawamangirira unyoro wolemera 50 lbs kuwapsyipsyiriza ndi zitsulo za moto pa matupi awo uku atawathira mchere. Ambiri aiwo kumangogona ndi njara, osamwa madzi, kuwaika pozizira kwambiri ndi kuwakwapula mosaneneka ndi munthu.

Nthawi zina zomwe zimachitika nzakuti makomunisiti okhaokha akapezana mirandu amawakatsekera ku ndende ndipo komweko amakakumana ndi akaidi achikhrisitu aja. Ndiye, akamawalanga akaidi achikomunisiti aja, chimeme nthawi zambiri akhrisitu amachita amalolera kuti amenyedwe ndiwo m'malo mwa akaidi ena. Nthawi zina akhrisitu ku ndendeko amatenga buredi wawo kupatsa makomunisiti a m'ndendewo kuti adye ndikuwapatsanso mankhwala amene woti akhrisituwo akadamwa kuti amwe ndi akaidi enawo.

Malinga ndi zimene akhrisitu anali kuchita m'ndendemo kuchitira akaidi achikomunisitiwo, Nduna yaikulu yakale ya dziko la Rumania a Iuliu Maniu omwe adamwalira m'ndende adanena mau awa asanafe. "Achikomunisiti atagonja pa zochita zawo, dziko la Rumania likanakhala dziko lodala ndi la chipulumutso, chifukwa anthu achikhrisitu akadakhala ndi ufulu onse wolarikira uthenga kwa aliyese.

M'masiku anga woyambirira nditangotembenuka mtima, ndimaona ngati chinthu chapatali kuyenda mbali zosiyanasiyana kunka nifalitsa uthenga. Komabe mtima sindimaupeza ndi nalakalakabe kukumana ndi anthu ndi kumawafusa ngati adamulandira Yesu. Ndipo ndikamva kuti wina mkhrisitu wachimwa ndimamva chisoni kwambiri ndi kulira nthawi yayitali. Ine pa moyo wanga ndi mafuna kuti aliyense alandire chipulumutso mosasankha.

Pamene tinali m'ndende zinthu zidafika poipa sitimatha kupemphera modikiza ndi motsimikiza kamba koti nthawi zambiri timakhala ndi njara ndipo tinali wofoka kwambiri matupi athu anali ngati mafupa okhaokha. Ndiye m'malo mopemphera ndi mangoti, "Yesu ndi kukondani." Tsiku lina lake ndidalandira yankho kuchokera kwa Yesu loti "Undikonda ineso ndikusonyeza chikondi changa." Ndipo ndidamva ngati moto mu mtima mwanga. Ophunzira a Yesu pa ulendo waku Emau adati adamva kutentha mu mtima mwawo pamene anali kulankhula ndi Yesu. Izi zinali chimodzimodzi ndi ine. Ndi zowona chikondi cha Mulungu sichisankha iye amakonda ngakhale anthu ochimwa.

Makomunisiti ndi anthu ochita zaupandu kwambiri kotero kuti palibe njira ina yowathandizira kuti akazindikire kuchimwa kwawo pokhapokha ife akhrisitu tipitiriza kusonyeza chikondi pakati pawo. Chikondi ndi champhamvu kapena nditi chiri ndi mphamvu yonse kufanana ndi mphamvu ya infa imene imamutengera munthu ku manda mosawona msinkhu wake, kutchuka, chuma, kapena udindo wake; Komaso ngakhale ali woyera pa maso pa Mulungu kapena mkunja infa imabwerabe pa onsewo. Ichi ndi chimodzimodzi chikondi. Khrisitu sadzasiya chikondi chake mpaka chikomunisiti chidzatha.

Nthawi ina yake m'ndende mwathumo mudafika mbusa atamenyedwa kwambiri ali magazi okhaokha ndipo sanali moyo anali atakomoka. Azanga akaidi atawona izi anamva chisoni ndipo adayamba kunyoza boma la chikomunisiti. Ine ndidawauza kuti palibe chifukwa chowanenera achikomunisiti. Ndidawapempha kuti akhale chete kuti tiwapempherere makomunisitiwo.

## Mmene Tingawonetsere Chimwemwe Chathu Pamene Tiri M'ndende.

Pa zaka Khumi ndi zinayi ndakhala ndiri m'ndende, nthawi zambiri sindimaonetsa kukhumudwa m'malo mwake ndinali munthu wachimwemwe ngakhale kuti ndinali kuzuzika zirango zosiyanasiyana. Ndipo makhalidwe angawo anali kudabwitsa amene anali kutironda kuti sindimawonetsa chidani china chiri chonse m'malo mwake ndinali kuwasangalalira. Alon-

dawo amati kodi akhrisitu ndi anthu a mtundu wanji wosamva chirango. Izi zimawadodometsa ndipo chifukwa cha ichi samatikaniza kuyimba. Ife akhrisitu timayimba ngakhale wina wa ife amadziwa kuti mawa ndiphedwa koma samasiya kuyimba. Alondawo amadabwa kuti zitheka bwanji kuti akhrisitu azibvina pamene ali pakati pa mazuzo otere?

Ine ndimaganiza zomwe Yesu adali kunena kuwauza wophunzira ake kuti ndi wodala iwo maso awo awona zimene akuziwona.

Nthawi imeneyi wophunzira atangofika kuchokera kokalalikira m'dziko la Palistina, kumene amakumana ndi zinthu zoopsya kuwazuza ndi kuwachita chipongwe china chirichonse chifukwa cha dzina la Yesu. Nthawi zina wophunzirawo anali kukumana ndi mabanja womwe anzawo kapena makolo awo adamangidwa mwina amapeza wodwala zonsezo unali mtolo wawo kuti awatonthoze. Zonsezi zimabweretsa chisoni ndi kulira pakati pawo. Koma ngakhale zinthu zinali chomwechi, Yesu adati wodala iwo akuwona zinthu zoterezi. Yesu sankanena mazuzo okhawo ayi komanso amanena iwo amene adamuona iye amene ali mu wombolo wa anthu wonse. Izi ziri ngati momwe timawonera moyo wa mphalabungu kuti pamene ikubvutika kuyenda kutsamba wosadziwa kuti tsiku lina idzakhala m'moyo wina wa gulugufe nadzawuluka mosabvutika kutera pa maluwa wosiyanasiyana. Umu ndi mmene munthu wokhulupirira adzakhalira pakutha pa moyo uno wa dziko la pansi.

Pa moyo wanga ndawona anthu ambiri akuzuzika kwambiri ngati Yobu kapenaso kuposera Yobu. Koma

ndimakumbuka chotsatira cha mazuzo cha Yobu kuti zonse zake zomwe zidaonongeka adazirandiranso mowirikiza ndipo mabvuto ake onse adatha. Komaso ndakhala ndi anthu awumphawi ngati Lazaro amen analibe chakudya ndipo sanali kusamalidwa koma pamapeto a moyo wake adakalandiridwa ndi angero kumuika pa chifukwato cha Abraham. Ndipo iwo amene ndakhala ndi kuwawona mozuzika motere nawoso tsiku lina lake adzakhala pa bwino.

Ndipo iwo amene amalanga anzawo chifukwa cha chikhulupiriro chawo ndi mawaganizira monga zomwe zidachita kwa Paulo kuti iye adali munthu wakupha akhrisitu koma kenaka adadzatembenuka mtima. Ndimakumbukiranso wolonda ndende kuti nthawi ina yake adafuwula kuwafusa kuti, "Nditani kuti ndipulumuke?" Chomwe adafusa mlondayu ndi zomwe iwo akhala akutizuza mndende tsiku lina adzafusa fuso la mtundu womwewu ndipo ena anafusa kale. Anthu omwe amanyoza Yesu pa mtanda wa golgota ndi omwenso adadziguguda pa chifuwa powona kuti adapereka munthu wosachimwa.

Nthawi imene ndiri mndende pamene ndidazindikira kuti nthawi ina makomunisiti adzapulumutsidwa. Nkomweko ku ndende kudandizindikiritsa ine udindo wanga woti ndizichita pakati pa anthu wozuzika kuphatikizapo makomunisiti. M'ndende-mo ndidaphunziramoso za momwe ndingamawakondere achikomunisiti ndi kuwazindikiritsa chowonadi.

Anasi anga ambiri adaphedwa ndi asirikali achikomunisiti. Koma taonani kudabwitsa kwake kuti asilikali omwewo adakatembenukira m'nyumba mwanga.

Ndi zowona Mulungu sayang ana zinthu monga mmene ife timaziwonera ayi, kwa iye kulibe nthawi. Apa tikhoza kuwona kuti pamene ine ndakhala mndende zaka zonsezi ndi masautso onsewa zingokhala ngati nthawi yaitali komaso mazuzo owopsya koma pa maso pa Mulungu sikanthu. Chifukwatu kwa Mulungu pazaka 1-sauzande ndi kamphindi kamodzi. Ndiye chifukwa cha ichi ndiri ndi chikhulupiriro kuti anthu achikomunisitwa adzatembenuka mtima.

Zitseko zakumwamba ndi zotsekula ndipo kumwamba kukonda aliyense motero mwayi ulipobe woti munthu akalape ndi kutembenuka mtima. Akhrisitu ndi ntchito yathu kuti tikawonetse chikondi kwa anthu akunja osati chikondi cha chinyengo koma chikondi choti chikatengera anthu ku chisomo posiyana zoipa zawo.

Nthawi ina yake ndidaganiza za atsogoleri achikomunisiti, powona kuti mamishonale ena adaphunzirapo za mbiri ya chalichi, mwachitsazo mmene ku Norway adamulandirira Khrisitu. Izi zidatheka kaamba koti poyamba adacheza ndi mfumu ya dziko a Olaf ndi kumufotokozera bwino-bwino za chikhrisitu. Dziko la Russia nalo kale lidali lachikhrisitu chifukwa choti mfumu ya dzikolo m'zaka zimenezo idamvomereza chikhrisitu chimodzimodziso ku Hungary zinthu zidali bwino chifukwa choti Sitifano woyera adali wokhulupirira yemwe adali mfumu ya dzikolo. Zimenezi ndi chimodzimodzi konsekonse monganso ku Poland ndi ku Afrika. KOmwe mamishonale pofuna kuti m'mudzimo anthu alandire chikhrisitu amayamba adzera kwa mfumu ndipo mfumu ikamvomereza basi zinthu

zimayenda bwino. Kuchokera pamenepo ndidayamba kufufuza atsogoleri ena a m'maiko mwina amene angathe kuthandiza kuti maiko awo asinthe ndi kukhala achikhrisitu kuti poyamba tikaone chomwe tingachite ndi atsogoleri a mtundu umenewu. Kutembenuza atsogoleri ndi zinthu zothandiza kuti anthu onse m'dzikolo akasinthe potsatira mtsogoleri wawo. Ndiye apa titati tione kuti Mao Tse-tung kapena Breshnev anthu amenewa monga atsogoleri atalandira Yesu ndiye kuti maiko awo akhozaso kulandira Yesu chifukwa atsogoleri ndi amene ali ndi chisnsisi cha anthu awo.

Fuso ndiro kodi atsogoleri achikomunisiti akhoza kupulumutsidwa? Eya nawonso akhoza kulandira Yesu chifukwatu anthu amenewa ali pa mpanipani alibe mtendere amanjatana wokhawokha ndiponso amaphana kusonyeza kuti pakati pawo palibe mtendere Mwa chitsanzo ku China Nduna za boma monga Iagoda, Iejov, Beria wonsewa ankawoneka ngati kuti ndi anthu a mtendere chifukwa zonse zinali m'manja mwawo koma tsoka nali kuti ambiri ayiwo anafa ndi infa yodzipha chifukwa chosowa mtendere. Mwachitsazo posachedwapa a Shepelin omwe anali Nduna yaza m'dziko ku Russia ndi a Rankovic Nduna yaza m'dziko ku Yugoslavia adawachotsa ndi kuwataya kunja kwa mabomawo ngati sanza zosafunika.

## Mmene Tingagonjetsere Chikomunisiti.

Boma la chikomunisiti liribe mtendere ngakhale anthu amene amaoneka ngati wodya bwino womwe amapeza phindu m'bomamo kwa iwo amakhala ngati alendo osasangalala kwambiri ngati boma sirawo. Izi

zimachitika motere kaamba koti nthawi ina iriyonse akhoza kuwona galimoto ikubwera kudzawatenga pa zifukwa zosiyanasiyana kupita ku ndende. Ndiye ngati anthu moyo wawo uli chomwechi akhrisitu angalephere bwanji kuwalalikira anthuwo kuti akadziwe Yesu yemwe apatsa mtendere weniweni pa moyo wa munthu. Chikomunisiti chitati chatha ndiye kuti zinthu zikhonza kusintha ndikumayenda bwino. Ndiye chisinsi chake chenicheni ndi kutembenuza atsogoleri amaboma achikomunisiti kuti akalandire Yesu tikatero ndiye kuti ena onse m'maikowo sangamvute. Kotero kuti m'maikomo anthu akhoza kumakhala omasuka ndi achimwemwe chifukwa pakati pawo pali Khrisitu. Chikhrisitu chimathandiza kuthetsa udani, kuphana, njara ndi zina zotere. Pa zifukwa izi anthu angachiwone chothandiza kwambiri kulowa chikhrisitu osati mbali ya kuthupi kokha ayi komaso ku mbali ya moyo wosatha, Kutembenuza anthu aulamuliro ndi chothandiza ndipo chipatsa mwayi anthu wamba kuti naonso akatembenuke mtima. Ichi nchifukwa chake Ambuye Yesu adakhazikitsa utumiki wake ku mzinda wa Yerusalemu, momwemonso Paulo adachita zotheka kuti mirandu yake ikamalizikire ku mzinda wa Roma.

Baibulo limati munthu adzadula mutu wa njoka ndipo ife tikati zinthu ziyende bwino tiyenera kukalalikira ku Moscow ndiku Peking ndipo maiko ang'onoang'ono amene amatsatira maiko akuluakuluwa ndi wosabvuta iwo ndi wongotsatira. Ndiye tichite zotheka kufalitsa uthenga monga moyenekera. Paja mau adati "Wotembereredwa iye amene agwira ntchito ya Ambuye mwachinyengo."

Mpingo wakale umagwira ntchito yake mobisala koma modzipereka ndipo ambiri wokhulupirira m'masiku amenewo anali kukhala ndi maina ena wosati awoenieni kuti poteropo asakadziwike pamene agwira ntchitoyi. Momwemoso tiyeni nafeso tikagwire ntchito ya Ambuye mwa nzeru pakati pa anthu achikomunisiti. Ife tikhale anthu wodziwa zizindikiro zina zomwe zingatithadize pa utumikiwu monga anali kuchitira Yesu Khrisitu monga muja adatumira ena kuti apite m'mudzimo ndipo akapeza wina atasenza mtsuko yemweyo akamuuze za pasika. Zimenezi zimandisonyeza kufunika kwake kwa zizindikiro pa utumiki wathu. Titati tigwire ntchito monga mmene amachitira akale tikhoza kuchita bwino kwambiri.

Chomvetsa chisoni nchakuti ku maiko azanthu kuzambwe ku Ulaya m'malo moti akhrisitu azathuwo azisonyeza chikondi kwa anthu akunja iwo amasonyeza kuwalewa ndi kuipidwa nawo. Njira imeneyi singathandize kuti azathu atembenuke mitima ndi kutsatira Ambuye.

Kulankhulana pakati pa anthu mkumene kumathandiza anthu kuti adziwane komaso kuti pa china chirichose chomwe afuna kuti achite chitheka chifukwa pakati pawo palibe kusalana. Ifeso tikhale ndi moyo womwe-wo wokhala ndi chirakolako chomalankhula ndi achikomunisiti kuwauza za mau a Mulungu. Nthawi ina mndende ndidali ndi a Lucretiu Patrascanu munthu yemwe adabweretsa chikomunisiti ku Rumania, iyeyu m'malo moti akadakhala munthu wotetezedwa pa chikomunisiti chawocho koma tawonani zidachitika nzakuti anzake womwe, ndi amene adaka-

muika ku m'ndende kusonyeza kuti kunja kuno kulibe chabwino kwa anthu amene alibe Yesu. Mkuluyu adakamuika pakati pa anthu amisala ndipo komweko adasokonezeka nayeso nkumachita za misala. Mchitidwe uwu adachitiraso Anna Pauker munthu yemwe adali mlembi wa boma. Akhrisitu nawo amawachita chimodzimodzi kuti pa mapeto a moyo wawo akhale amisala.

Ku China nako kuli zirango zoopsya zosiyanasiyana ndipo ngati munthu amamuzuza poyera mu msewu kuli bwanji kwa akaidi amene saonedwa ndi anthu. Mlaliki wina wake waku China yemwe wakhala akulemba mabuku a mau a Mulungu ndi akhrisitu ena adawadula makutu, miyendo ndi malirime awo kamba koti adakana kusiya chikhulupiriro chawo mwa Khrisitu.

Chomvetsa chisoni china chimene achikomunisiti amachita ndi kuphunzitsa ana kuti azidana ndi mau a Mulungu ndi kutenga atsogoleri achikomunisiti kuti ndiwo azitsogolera m'machalichi pofuna kuti za mau a Mulungu zitheretu.

Buku ili sanalilembe ndi inki kwenikweni ayi koma ndi mwazi wa anthu osweka mitima."

Monga zidaliri mnthawi ya Daniel kuti anthu ena atatu adaponyedwa m'moto koma pochoko m'ng'anjoyo sadamveke fungo la moto ndi mmeneso akhrisitu ochoka ku kaidi sakhumudwa chifukwa choti anasungidwa mu kaidi ayi. Ngati munthu aponda maluwa chimene chimachitika nchakuti munthu uja amadzamva fungo labwino lochokera ku maluwa. Chomwechoso munthu wochokera la chikondi. Pamene ndiri ku ndende sindidangokhala chete ndidapitirizabe kuwauza

akaidi amene adamangidwa pa zifukwa zina kufunika kwake komulandira Khrisitu moti ambiri adadzatuluka m'ndendemo ali akhrisitu.

Ndinadabwa kuti ku Ulaya mamishonale amangotaya nthawi ndi kumuuza mkhrisitu wa chalichi china kuti apite tchaichi chake munthu yemwe ndi wotembenuka kale koma iwo amangoyang'ana kwa achiHindu, achisilamu mdi a achiBuddaisiti ndi kusasamala achikomunisiti. Chikondi chotere ndi chosathandiza.

**Kusasamala Phunziro La Mbiri Yakale**

Kale ku mpoto mu Afrika anthu ambiri adali akhrisitu. Koma lero ayi ambiri ndi Asiramu. Izi zidachitika motera sichifukwa china, koma kuti akhrisitu nthawi imeneyo pamene chisiramu chimalowa kumeneko akhrisitu sadasamalire. Ndiye zotsatira zake ndi zakuti chigawo cha Afrika-cho chiri m'manja mwa Asiramu. Akhrisitu adalephera kuwalalikira asiramu kuchokera pa chiyambi pomwe nchifukwa chake zikuoneka zobvuta.

Tiyeni tizikhala ndi mpata womaona umo kale zinthu zidaliri!

Nthawi imene mipatuko idayambika yomwe atsogoleri ake adali a Huss, Luther ndi a Calvin zidadzachitika pamene azathu aku Ulaya analiso kulimbana ndi chalichi cha Katolika chomwe chinali kuweruza m'maiko aku Ulayawo ndiye zinthu sizinali bwino chimodzimodziso lero pamene a chalichi chobisika akulalikira uthenga kwa chikomunisiti anthu m'maiko ambiri akulimbirana ufulu wodziramulira.

Palibe ulamuliro wina wa ndale umene ungathetse

chikomunisiti, komaso achikomunisiti ali ndi zida zoopsya moti kupanda kuwatenga bwino zingathe kuyambitsa nkhondo ya dziko lonse la pansi. Azathu ku Ulaya anapusitsidwa iwo angolimbikira kupeza njira zothetsera matenda koma akuiwala kuti china chimene chawononga anthu ambiri ndi mchitidwe wachikomunisiti.

Atsogoleri aku Russia sagwirizana, wina amachita zake wina achita zake. Mwachitsazo a Kruschev amati a Stalin sadachite bwino pa nthawi yawo adaonongetsa kayendetsedwe ka boma laku Russia. Koma tsono iwo a Khruschev pa nthawi yawo palibe chimene adachita adabweraza kuchita zomwe ankachita a Stalin. Kuwonjezera apo a Khruschev m'chaka cha 1959 adatseketsa machalichi ochuluka chifukwa cha zofuna zawo.

Ku China nako kudayambikaso machitidwe woipa wonga ngati amene ankachita a Stalin ku Russia. Kulibe chabwino ku Russia akhrisitu akungomangidwa, ana akapezeka m'chalichi akumawatulutsira pa windo mochita kuwapodya. Palibe chomwe tingagwiritse ntchito polimbana ndi chikomunisiti koposa kugwiritsa mau a Mulungu basi, kubzolera m'machalichi obisika amene akupezeka m'maiko onse achikomunisiti. Ambiri omwe amakhulupirira chikomunisiti akamafa kapena ali pafupi kufa amalapa kutsimikiza kuti titayesetsa anthu ambiri achikomunisiti masiku ano akukhalira kukangana za ubale palibe zochita zawo ngati agalu wolimbirana fupa. Poyamba ankakhulupira kuti afuna kuti dziko la pansi likhale lodalirika koma tsopano anthu. akufa ndi njara, kulekana ndi zimene amalankhula kuti afuna dziko lino likhale la ulemerero ndi kuti munthu asachulenso za kumwamba kapena Mulungu

ayi.

Makomunisiti afika nthawi yosadalira atsogoleri awo chifukwa onse alephera kuyambira Stalin yemwe wakhalira kupha anthu, Kruschev naye ndiye pachabe chimodzimodzinso atsogoleri ena ambiri monga Rakosi, Gero, Anna Pauker, Rankovici ndi ena wotere. Ndi pokhapokha anthu aku Russia ndiaku Rumania atadziwa za Yesu mpamene angapeze mmpumulo ndi mtendere, ndi chimwemwe pakati pawo.

Yesu adati dzuwa limawalira anthu onse woipa ndi abwino chikondi cha akhrisitu chiyenderera aliyese wolungama ndi wochiwa.

A mipingo ya evangeliko ndi Katolika m'dziko la West Germany pa zaka zisanu ndi ziwiri zapitazi, adapereka ndarama zokwana 125-miliyoni kwacha ndipo aku Amerika adaperekaso zoposera pamenepa. Ndaramazo ndi zogulira chakudya cha anthu amene akukhala ndi njara chifukwa cha Khrisitu.

Chikhrisitu ndi cha anthu amitundu yonse. Wokhulupirira woyamba aja adali ndi nkhawa yomweyi kuti kapena chikhrisitu chinali cha aYuda okha koma kenaka nkudzapeza kuti chikhirisitu ndi cha anthu onse ngakhale akunja. Ichi nchifukwa chake Yesu popachikidwa pa mtanda adatambasula manja ake lina kuloza kuzambwe lina ku bvuma kuti iye ndi mfumu mbali zonse za dziko la pansi. Komaso Yesu adati powuza wophunzira aja. "Pitani lalikirani kudziko lonse la pansi." Yesu adakhetsa mwazi ndipo mwaziwo adakhetsera aliyense.

**N'dapezanji Ntangotuluka Ku Ndende**

Nditafika kuchokera ku ndende, mkazi wanga ndi damupeza ndipo nkulankhulana kwathu adandifusa ngati ndiri ndi maganizo ena. Ine ndidamuyankha mkazi wanga kuti cholinga changa ndi kukapitiriza kufalitsa uthenga wa Ambuye. Mkazi wangayo adandiuza kuti nayenso anali ndi maganizo womwewo.

Ndisanamangidwe ndinali ndi mphamvu ndi ojijirika koma chifukwa chokhalitsa m'ndende ndi mazuzo, thupi langa lidatha mphamvu. Koma moyo wanga unali wotakasukabe ku ntchito ya Ambuye. Amene adandizuza ndinalibe nawo kanthu chimene ndinali kuwachitira ndi kuwapempherera ndi kuwasonyeza chikondi changa chose.

Ndiri ku ndende sindimakhulupirira kuti tsiku lina ndi dzatuluka, Ndipo m'maganizo anga ndi mati ngati nditatuluka ndikakhala kwina kumene ndikapitiriza kugwira ntchito ya Ambuye.

Kutuluka kwanga M'ndende kunali ngati kutulo ndipo ndi zowona Mulungu ndi chilungamo, mau a Mulungu ndi yowona ine ndidatuluka pamene sindimayembekezera. Kunalembedwa kuti mwana wa munthu adzadza pamene ife sitiyembekezera. Tinangowona zitseko azitsekula Khrisitu adabwera kudzatitsekulira zitseko za ndende. Moyo wanga suli pa nkhondo ya thupi ayi koma ndifuna ndikamange nyumba zopemphereramo.

Nthawi imene nditatuluka ku ndende, boma limatha kuitana mbusa wina aliyense ndikumufusa anthu amene anafika ku tchalichi ndipo ndi angati amasonyeza kudzipereka kwambiri kapena kudya mgonero ndipo

ngati mbusayu safotokoza zenizeni amamuchotsa pa udindo wa ubusa ndi kuikapo wina. Chocho zinthu zinali zobvuta kwambiri. Ambiri anali kupereka anzawo m'malo moti iwo asachotsedwe pa udindo.

Atsogoleri onse a mipingo anali kusankhidwa ndi akuluakulu a boma ndi kuwauza zofuna za boma. Ine powona zimenezi ndidamva chisoni chifukwa kumeneko kunali kupha chikhrisitu. Izi zidandisowetsa mtendere ndipo ndinadana ndi chikomunisiti koposa kale lonse. Ambiri anali kubwera kwa ine kundiuza kuti tsopano zonse zinthu ziri m'manja a boma palibe kuti wina akhale ndi munda wakewake. Ndiye chifukwa cha ichi panali njara pakati pawo. Ana kusowa mkaka, kusowa zipatso, buledi ndi zakudya zina zotere zimene amakhala nazo chikomunsiti chisanayambike. Ena anali kundifotokozera machitidwe ankhaza mzintchito. Anthu wophunzira amawauza kuti ndi ntchito yawo kuti aziwuza anthu kuti kulibe Mulungu. Pafupifupi theka la dziko la pansi lidaonongeka ndi chikomunisiti.

Ndi anthu ambiri nthawi imeneyi ndidayamba kuwaganizira amene pa moyo wawo anakakhala ku nkhalango koma chifukwa cha zochitika pakati pa anthu osiyana adabwerako kukathandiza kuwonetsa chowonadi pakati pa anthuwo. Ena mwa anthu ndi monga Anthony woyera a Bernandria ndi ena wotere.

Anthu ambiri woyera mtima adakhala ali kumangidwa ndipo panalibe wina wodandaula. Ena mwa iwo kumangidwa chifukwa choti amagawa mabuku a mau a Mulungu. Ena mwa wokhulupirikawo anali kuwatenga ali ndi unyolo m'manja mwawo kukawapereka kuzirombo za mthengo kuti ziwadye zonsezi zidadza ndi

chikomunisiti. Tsono pa mpingo panali akhrisitu osiyana ena wopembedza mu mzimu ndi nchowonadi pamene ena anali kukhala pa chalichipo ndi kumachita zofuna za boma.

**Chifukwa Chiyani Sindikupeza Mtendere M'maiko Akuno Ku Zambwe.**

Kuno kuzambwe ku Ulaya zinthu sindikuziwona bwino chifukwa choyamba nchakuti ndimalingalira kwambiri za chalichi chobisika m'maiko achikomunisiti. Komaso ndikalingalira kalalikidwe ka azanthu m'chalichicho nkosalongosoka chifukwa ambiri alalikiwo ndi anthu amene akhala m'ndende zaka zambiri ndipo analibe mwayi wowerenga baibulo koma sanakhaleko ku sukulu ya mau a Mulungu. Ambiri mwa iwo akati atengedwa kupita ku ndende samawalola kuti atsazike ku ana awo ayi. Kundendeko kulibe chabwino chakudya choipa komaso chodya pa nthawi. Ndipo kwa iwo kumanga nyumba kunali kutaya nthawi chifukwa bomalo limalanda nyumbayo. Tsono chifukwa cha ichi akhrisitu kumeneko satekeseka zomanga nyumba. Yesu adati mwana wa munthu kuphatikizano iwo amene amutsatira alibe potsamira mitu yawo. Koma ndichochititsa chidwi kuti ngakhale amakhala mwa mtundu umenewu sadandaula chimodzimodziso Mbuye wawo pa mtanda Yesu adaitanabe dzina la Mulungu ngakhale kuti Mulungu adamuchokera pa mtanda paja. Iye amene akudziwa za chalichi chobisika akhoza kuona yekha kusiyana kwa chipembedzo cha m'maiko ena kumene kulibe chikomunisiti ndi ku mene kuli chikomunisiti. Ndiposo machalichi ambiri aku zambwe ku

Ulaya ndi akufa sakutha ntchito. Oswald Spengler adalemba kuti mpingo ku Ulaya ndi maiko ena kumene kulibe chikomunisiti ukutha mphamvu. Izi zikuoneka mnjira zambiri monga kumenyana kwa anthu a dziko limodzi kusowa kwa chuma ndi ziphunzitso zina za chilendo zosagwirizana ndi moyo wa uzimu, monga kulekana pa banja mosabvutikira ndi mopanda chifukwa chokwanira, kuletsa kubereka zosezi ndi zizindikiro zosonyeza kuti mphamvu ya chikhrisitu ikutha simonga mmene amakhalira azathu aja m'masiku a baibulo.

A Wurmbrand adati ndi zomvetsa chisoni kuti akhrisitu kuno kuzambwe ntchito yawo ndikukambirana zinthu zomwe siziri zaphindu ku moyo wa uzimu ichi ndi chifukwa china chimene chikubwezera m'mbuyo chikhrisitu. Ndipo ndi zowona ukakhala ku maiko komwe kulibe chikomunisiti umangoti kunja kulinji kapenaso zimene zimanenedwazi umayesa njerengo pamene ziri zenizeni kuti anthu ena akubvutika kwambiri chifukwa cha moyo wa chikhirisitu. Mwachitsazo m'chaka cha 1959, ndinali ndi mkaidi wina dzina lake Lazarovici iyeyu adamuchotsa makadabo kuti ati amvomere zinthu zomwe iye sadachite zomunamizira kuti adapha mtsikana. Iyeyu chifukwa chomuzzuza chochi amaoneka ngati wamkulu pamene anali wa zaka 30 kamba ka mazuzo a boma la chikomunisitiro. Ine nkhawa yanga njakuti bwanji akhrisitu akuno ku zambwe sitifuna kuthandiza anzathu amene akubvutika chochi. Ine ndikamaona zikuchitika m'maikowa ndimalakalaka kukakhala kwa ndekha kuti zoterezi zisamandikhudze. Kuli bwino ndikakhale kwina chifukwa

chikomunisiti chikuthaza kwambiri kotero ndi ntchito yathu monga akhrisitu kulimbikirabe kulalikira chowonadi. Ndikanati ndi kapume kwina kwake kwa ndekha zikanakhala zosapindula komaso ndi ngozi ku moyo wanga. Zibvute zitani ine ndidzapitiriza kufotokoza chowonadi cha Ambuye ndipo ngati nditasowa ndiye kuti anditenga asirikali achikomunisiti chifukwa ndikukumbukira mmene adanditengera m'chaka cha 1948 ndikundika m'ndende. Nthawi ina yake mlembi wa boma la dziko la Rumania a Anna Pauker adauza kazembe wa dziko la Sweden za bodza zenenao iye Wurmbrand. A Wurmbrand adalemba kalata kuti zonse zidanenedwazo ndi za bodza ndipo adati ngati a Wurmbrand-wo adzaphedwa adzawapha ndi achikomunisitiwo.

Iwo adapitiriza kulongosolo mkalatamo kuti zimene amanena za iwo monga zokhudza kuba, dama ndi zina zokhudza ndale ndi za bodza. Koma kuti a polisi ali ndi chiwembu chofuna kundipha osati munthu wina wapadera ayi. A Wurmbrand adati ngakhale amunenere zotani sadzaleka kuchitira umboni za Khrisitu. Ndipo ndikuliwuza boma la Rumania kuti lizimvetsetsa zomwe ndi malalikira pa uthenga wanga ngakhale kuti bomalo limandisinjirira kuti ndine wozungulira mutu; chifukwa choti ndidakhala mndende nthawi yayitali izo ziribe kanthu koma choti mudziwe nchakuti chikomunisiti nchimene chikuononga anthu mnjira zambiri. Maiko aku zambwe ku Ulaya asagone ndi nthawi yokhala maso ino.

Anthu ena akakhala m'mabvuto achikhrisitu ngati amenewa amafuna njira yothawira kapena kuzemba.

Ine zimenezo sindingachite kuli bwino ndi bvutike kusiyana ndi kuloza chala munthu wina, kuti ndiye wandipweteketsa.

Pa nthawi yonse ndakhala ndiri ku Ulaya ndakhala ndikuyenda ku sukulu za ubusa zambiri ndipo komweko ndamva zoti ati iye amene adalemba buku la chimvumbulutso adali wa msala, kuwuka kwa Yesu sizowona mafupa ake akuwasunga kwina kwake, zoti aIsraeli adawoloka pa nyanja powuma akuti ndi bodza zoti kudali chigumula cha Nowa akuti ndi nthano chabe, za chirengedwe cha dziko akuti ndi zopeka ngakhale nkhani ya adamu akuti sizedi. Koma kwa ine baibulo ndi mau a Mulungu ndipo ndi woyera.

Zomvetsa chisoni kuti lero ku sukulu za mau a Mulungu anthu akuphunzirako zinthu zosiyana ndi mau a chowonadi. Ndiye zingatheke bwanji kuti munthu wodziwa chowonadi angamakhulupirire zinthu zotere zomanena kuti Mulungu adafa. Azibusa a mtundu uwu ndi wolembedwa ndi boma la chikomunisiti wosati woitanidwa ayi. Ine udindo wanga ndi kumuwuza munthu chowonadi ndipo ngati amangidwa sichifukwa, malinga iye wamva ndipo ambiri adatembenuka chifukwa chowachitira umboni ndi kuwauza mau a Mulungu. Kwa ine ndimafuna bvuto la chowonadi likhale langa osati ndi namizire munthu wina ayi zimenezo pa moyo wanga sindidzalola.

Mkulu wina wake adati Yesu sadachite bwino chifukwa nthawi ina adawadzudzula afalisi pa gulu la anthu pamene iye yemwe akuti tizikonda aliyese. Mkuluyu yemwe dzina lake ndi Montefiore adalankhula nkhani ya Yesu-yi chifukwa chosazindikira. Yesu ama-

konda aliyese. Ndi anthu ambiri amene samadziwa kulitanthawuzira bwino bukuli. Tsiku linaso ndi dakumana ndi mkhrisitu wina yemwe adazuzika nthawi ya ulamuliro wa Nazi ndipo mkhrisituyo adandiuza kuti iye ndi ine ndife wogwirizana pa chikhulupiriro chathu koma adandiuza kuti polalikira ndisamatchule dzina la chikomunisiti. Ine ndidamuza kuti sindingangotchula mau a mbuku loyera osachula chinthu chimene tikulimbana nacho ngati kuli tero akhrisitu sakadayenera ku mutchula Hilter pa nthawi ya nkhondo ya Germany. Iye adati Hilter adapha anthu 6, miliyoni ine ndidamuwuza kuti Chikomunisiti chapha anthu 30-miliyoni kuphatikizapo aku China ndi maiko ena. Ndiposo chikomunisiti ndicho mdani wamkulu wa chikhrisitu. Munthu ayenera kukhala ngati mmene adaliri Khrisitu ndipo ngati sitikhala chocho ndiye basi tagwera m'chikomunisiti, chomwe chiakhulupirira kuti munthu akafa amakhala kapena zinthu zina zolengedwa.

Palibe chifukwa chonyengererana pakati pa akhrisitu ndi achikomunisiti ife akhrisitu titenge za Yesu basi Cholinga cha chikomunisiti ndi kupha chikhrisitu ndiye sitingalolele zoterezi ndipo chomwe tidziwa nchakuti chikomunisiti nchakutha.

# MUTU 5

Pano sindilankhulanso za chalichi chobisika.

Chalichi chobisikachi chimagwira ntchito yake mobvutika kwambiri.

M'maiko achikomunisiti mau awo achiphunzitso ali pa chikomunisiti. Maboma a maiko-wo, amalola akuluakulu kupitiriza zimene adazikhulupirira kuchokera kale, koma mbali ya ana amawaphunzitsa zimene iwo amati zamakono za chikomunisiti kotero salola kuti anawo azimva za makolo awo kapena kuzikhulupirira. Zipangizo zonse m'maiko aku Russia ndi Rumania ndi kwina kuli konse kuli chikomunsiti zimagwira ntchito yofalitsa zomwe mabomawo amazikhulupirira. Monga mawailesi, wailesi zakanema, kanema, zisudzu ndi malo osindikizira mabuku zonsezi ntchito yake ndi imodzi kufalitsa chikomunisiti ndi kupha chikhulupiriro choti kuli Mulungu.

Atumiki a m'chalichi chobisika alibe mphamvu yokwana yotsutsana ndi boma. Ndiponso atumikiwo sanakhalepo pa baibulo sukulu, kapena kudzozedwa pa ntchitoyi.

Tsiku lina lake ndidakumana ndi mlaliki wachinyamata wachirussia yemwe amayendetsa utumiki wake mobisa, ndipo ndidamufusa kuti ndi ndani adamdzoza kukhala mbusa. Iye pondiyankha adati palibe adamdzoza chifukwa abusa wodziwika ndi bomalo samalola kumdzoza wina aliyense amene

sadamvomerzedwe ndi akuluakulu a boma. "Ndiye chimene tidachita tonse poti tiripo khumi tidapita ku manda ya bishopu yemwe adafa ndi kulola awiri aife kugwira pa chirizacho ndipo azathu ena adatizungulira ndikuyamba kupemphera kupempha mzimu wa Mulungu kuti utidzoze. Ndipo pa chifukwa ichi tiri ndi chikhulupiriro kuti Yesu adatidzoza ndi manja ache." Kwa ine mnyamatayo ndi odzozedwa monga mtumiki wina aliyense. Atumiki a mtundu umenewu ndi ambiri amene alibe mwayi wokhala pa sukulu naphunzira mau a Mulungu mmene amachitira ena komanso ambiri ayiwo alibe mabaibulo ndipo sadziwa zambiri za m'bukuli. Koma chodabwitsa ndi chogwira mtima nchakuti akutha kugwira ntchito ya Mulungu ndi kuikwaniritsa bwino kusiyanaso ndi iwo amene anakaphunzira ku sukulu. Iwo amagwira ntchito yawo monga atumwi woyamba aja womwe adakhoza kutembenuza dziko lonse la pansi ndi kulizindikiritsa chowonadi cha Ambuye. Koma chosecho ambiri ayiwo anali wosaphunzira, analibe mabaibulo koma anagwira ntchito modabwitsa. Zosezo zidatheka chifukwa choti Mulungu adawalankhula.

Ife a mpingo wobisika ku Ruamania, tiribe nyumba zopempherer amo zokongola. Ndiponso chomwe tidziwa ife nchakuti kulibe nyumba yokongola yoposa ntambo wakumwamba. Tikamapemphera kuimba kwa mbalame kumakhala ngati nthetemya zothirira mang'ombe pa misonkhano yathu.

Ku woneka kwa maluwa a m'ngalangomo ndi zomvala zochoka nazo ku ndende kwa iwo amene angomasulidwa kumene kwa ife zimaoneka bwino kusiyana ndi

bishopu amene wabvala chobvala cha ubusa. Nyenyezi ndi mwezi ndizo nyali zathu ku misonkhano yathu ya usiku ndipo wotiunikira ndi angero. Ndikunena izi kukupatsani chithunzi cha momwe zinthu ziriri mbali zina za dziko lino. Sindidziwa kuti ndingafotokoze bwanji za mmene zinthu ziriri pakati pathu. Nthawi zambiri tikangomaliza kupemphera tirikutuluka nthawi yomweyo ena mwa ife amatengedwa asanafike ku nyumba. Unyolo umangokhala ngati kuti ndi mphete imene munthu amalandira kwa bwezi lake ndi chisangalalo. Ku ndendeko umakhala ngati ukulandira chipsyopsyono kwa Ambuye ndipo umaona chimwemwe kusiyana ndi munthu amene amakhala ku nyumba ya mfumu. Ngati kuli anthu kunja kuno achimwemwe chodzala tsaya ndi anthu wopemphera mchowonadi; akhrisitu enieni. Iwowa amasangalala ngakhale pamene akuzuzika m'ndende ngakhale kuti sapempherera m'nyumba za bwino za makono.

Chalichi chathu chobisikacho, chiri ndi anthu ambiri ndipo ngakhale bomalo limayesetsa kuponderеza kuti chisagwire ntchito yake bwino komabe pakati pa apolisi a bomalo amakhozaso kutiteteza mnjira zina chifukwa ena mwa iwo ndi anthu okhudzidwa ndi mapemphero.

Popereka chitsimikizo cha nkhaniyi, atolankhani a bomalo adati mzimayi wina amene amagwira ntchito yofalitsa nkhani za dzikolo, amati akaweruka amakakumana ndi mwamuna wake ndikukalowa ku malo ena komwe amakasonkhana ndi ana ndi kumawaphunzitsa mau a Mulungu ndipo kenaka ndi kumapemphera. Zimenezi amachita nthawi ija yoti atha kudya chakudya

chamadzulo asanakagone. Zoterezi zimachitika konsekonse m'maiko achikomunisiti. Alipo anthu zikwikwi amene amadzionetsera ngati wokhulupirika ku boma koma pansi pa mitima yawo ndi anthu wopembedza Mulungu weniweni kotero kuti amakumana mwatseri kupemphera ndi kumalimbikitsana.

Akhrisitu wobisikawa, amachita zinthu zawo pamodzi ndi momverana ndipo alibe nthawi yomakangana paza ubatizo kapena za mtumiki wina aliyense wa m'baibulo koma ndi anthu ochititsa chidwi akamawatsimikizira achikomunisiti kuti kuli Mulungu ndipo amalankhula mfundo zogwira mtima. Poyankhana nawo achikomunisiti amawauza motere, "Kodi atakuitanani ku chakudya kodi chakudyacho munganene kuti chaphikidwa chokha. Ndi chimodzimodzi dziko la pansi. Dzikoli lidakonzedwa ngati phwando lathu ndipo alipo adalikonza kukozera ife anthu kuti tidye ziri mmenemo.

Nkhaniyi amawauza a chikomunisitiwo kuti ndi chimodzimodzi munthu atalankhula kwa mwana amene sanabadwe, kumuwuza moyo ali nawowo siwokhalitsa, kodi mwanayo angati chiyani yankho lake? Iye angathe kuyankha monga momwe muyankhira inu achikomunisiti paza ufumu wa Mulungu ndi gehena. Mwanayo akhoza kunena kuti chipembedzo chiribe ntchito chifukwa iye maganizo ake akhoza kuganiza kuti zinthu ziri monga mmene azioneramu. Maganizo amenewo ndiwo amene achikomunisiti ali nawo sadziwa kuti kuli moyo wina pakutha pa moyo uno. Koma mwanayu atati aganize mozama, angathe kudabwa kuti chifukwa chiyani manja akuphukira m'thupi mwanga, miyendonso nayo

ikutuluka zonsezi ndi za chiyani pakuti muno palibe poti nkutambasulira manja. Miyendonso nayo ndiribe nthawi yoyenda kwanga nkupindika basi. Ndiye mwina amadzati manjawa adzagwira ntchito mtsogolo ndipo miyendoyi ndizidzayendera. Chimodzimodzi maso palibe chifukwa chokhalira ndi maso ine muno m'mopanikizika sindingaone kutali ndiponso ndi mu m'dima palibe chifukwa chokhalira ndi maso. Ndiye kenaka amadzati mtsogolomo ziripo zomwe ine ndidzafuna kuziwona. Ndiye mwanayo akaona zikuchitika mthupi lake amadzadziwa kuti kuli dziko lina akadzachoka m'thupi la make ndipo kumeneko nkumene kudzafunikira zomwe zikutuluka m'thupiri. Ndi chimodzimodzi ife, nzeru zomwe tiri nazozi zoganiza za moyo wakutsogolo ndi zimene zititsimikizira za moyo wosatha. Chifukwa kukadapanda kutero panalibe chifukwa chokhala ndi nzeru zoganizira zinthu zakuya pamene tikudziwa kuti tsiku libwera ndipo tidzalowa m'manda. Chifukwa chiyani mwana adayamba kukhala ndi maso, miyendo, manja ndi ziwalo zina zotere ndi chifukwa choti kuli china chotsatira kutsogoloko. Chomwechoso ife tikukula mu nzeru ndi mu mzimu chifukwa cha zimene zikubwera kutsogolo kwathu. Ife tikukonzekera kudzachita zinthu zazikulu mtsogolo muno titamwalira.

Paza Yesu, achikomunisiti amati kulibe Yesu koma a chalichi chobisikacho amawauza kuti kuli Yesu ndipo nthawi zina amawafusa ngati wina ali ndi nyuzipepala ndi kuwafusa kuti ndi ya liti akati ndi yapa 14 January 1964 ndiye amawafusa kuti kuwerengako kudayambika liti? Mkuyankha kwawo amati kudayambika kale kwa munthu woyamba wosadziwika. Ndipo wokhulupiri-

rawo amawatsimikizira kuti kuwerenga masiku kudayamba pa nthawi ya Khrisitu. Komabe Khrisitu asadabadwe analiko masiku koma kubwera kwa Khrisitu anthu adayambiranso kuwerenga ndipo nyuzipepala yanuyo ikutsimikiza kuti Yesu sinkhani ya nthano chabe ayi.

Atumiki a mu mpingo wa chalichi chobisika ndi atumiki a chalichi cha boma amangokhala osakanikirana woti kuti uwadziwe atumiki enieni ukhoza kuwadziwa malinga ndi machitidwe awo pa utumiki.

Chalichi cha boma la chikomunisiti chidayamba ndi bungwe la Russia lotchedwa Russian Socialist Revolution ndipo mbusa wake anali Sergius.

Chitangoyambika chalichi cha mtundu umenewu, adalengeza poyera kuti cholinga cha chalichicho nkulowa m'malo mwa chalichi chenicheni cha Mulungu ndipo kuti cholinga nkufafaniza chalichi cha chikhrisitu. Ndiye kuchokera ku dziko la Russia chisokonezocho chidawanda m'maiko onse achikomunisiti monga ku Hungary komwe otsogolera wake anali Balogh ndipo ku Rumania anali Burducea. Mabomawo amauza anthu kuti afuna kukhazikitsa ulemerero weniweni pano pa dziko la pansi kotero kuti palibeso zoti munthu azilankhula za kumwamba. Kumwamba kwa iwo ndi pompano pansi. Machalichi achikominisiti ndi wongofuna kuti aziwona bwino za akhrisitu ndi kumawagwira ngati achita zinthu zosagwirizana ndi maboma a m'maikowa.

Pa nthawi imeneyi ena atsogoleri a mipingo amawanyengerera kuti azikaneneza anzawo ku boma za zimene akhrisitu ena akuchita. Koma ampingo wa chalichi chobisika palibe ndi mmodzi yemwe adalolera

kuchita za upandu zotere zokanenera wina ku boma chifukwa choti akuphunzitsa ana nthano za m'baibulo.

Ndipo ena mwa akuluakulu aboma la chikomunisiti omwe amalimbana ndi kuthetsa mapemphero adafa chifukwa cha zolinga zawo. Akhrisitu, nkhondo yawo iri mchikhulupiriro ndipo chifukwa cha ichi mphamvu ya machalichi okhazikitsidwa ndi boma-wo ikunka niitha ndipo ngakhale chiwerengero cha mamembala awo chikunka chitsika. Nyumba zawo zopemphereramo ndi zing'onozing'ono ndipo zosadziwika bwino. Machalichi abomawo akutha mphamvu chifukwa chakulimbikira kufalitsa uthenga kwa mamembala a chalichi chamtseri chobisika.

## Akhrisitu A Mpingo Wobisika Ndi Mabuku A Chikomunisiti

Akhrisitu a mpingo wobisika ndi anthu ochenjera pa kagwiritsidwe ka ntchito ka mabuku achikomunisiti ndi mabaibulo. Iwo amawerenga zonena za akomunisiti monga momwe ankalandirira chakudya mneneri Eliya kuchokera ku zikwangwala. Koma akatero amafatsanso ndi mavesi a baibulo omwe akomunisitiwo akuwanyoza ndipo pomwepo amadziwadi kuti makomunisiti sakudziwa chimene amanena paza baibulo. Mau a m'baibulo sasintha ngakhale kuti wowalankhula ndi munthu wakunja wonyoza mau a Mulungu sadzasintha. Nyumba yosindikizira mabuku a chikomunisiti amakonda kulandira makalata ambiri kuwapempha kuti asindikize mabuku ambiri momwe muli mavesi am'baibulo ndipo makalatawa amachokera ku mamembala a chalichi chobisika ndi cholinga choti akhale ndi mavesi ambiri a m'buku lopatulika. Ndipo mbali ina kunali

kuwaseka a bomawo.

Mhunzitsi wina wa mkulu wa chikomunisiti, adauza anthu kuti Yesu anali munthu wamatsenga. Mhunzitsiyo anatenga beseni la galasi ndipo munali madzi, ndipo adauza anthuwo kuti chimene adachita Yesu ku ukwati ndi ichi kuti iye pamene amati wasanduliza madzi kukhala viyo sizinali zowona iye m'manja mwake mudali paudala wofiyira ndipo adatenga pa udalayo mobisa ndi kuthira m'madzimo ndipo madzi adasandulika kukhala ofiila ndi ozuna. Iye powatsimikizira anthuwo adatenga madziwo ndikuthiramo paudala wofiira ndipo madzi adasandulika ofiira. Atatero adauza chinantindi cha anthu-wo kuti izi ndizo zimene adachita Yesu ku ukwati. Mkuluyo adati Yesu adachita izi mwa nzeru kuti anthu asadziwe kuti adali ndi paudala. Iye adauza anthuwo kuti iyeyu akhoza kuchita zoposa adachita Yesu. Popitiriza kuwatsimikizira anthu aku msonkhanowo adatenga madzi ofiyira aja ndi kuikamoso paudala woyera ndipo madziwo adasandulika woyera.

Poyankha wina mwa Akhrisitu pa msonkhanowo, adati ndi zowona mwatichititsa chidwi pa zimene mwachita. Koma ndikukupemphani mphunzitsi kuti mumwe madzi mwasandulizawo. Poyankha mkuluyo adati sangathe kumwa chifukwa paudalayo ndi wowawa wakupha. Mkhrisituyo adamutsimikizira mphunzitsiyo kuti kusiyana kwa iye ndi Yesu kunali pamenepo. Kuti waini wopangidwa ndi Yesu atipatsa ife chimwemwe mpaka pano ngakhale kuti papita zaka 2-sauzande. Pamene inu waini wanu amatisowetsa mtendere ndipo ndi wakupha. Atangolankhula chom-

wechi pa msonkhanowo sadamlekerere adamunjata kupita naye ku ndende. Koma akuti nkhaniyi idafalika kutali ndipo ambiri akhrisitu adalimbikitsidwa pa moyo wawo wa chikhrisitu.

Ife ndife a Davide ofoka koma ndife a mphamvu kusiyana ndi a goliyati achikomunisiti chifukwa choti Mulungu ali ku mbali yathu ndipo chowonadi chiri ndi ife.

Nthawi inaso panali msonkhano wa anthu wogwira ntchito pa kampani ndipo msonkhanowo adaukoza kuti anthuwo awafotokonzere za chikomunisiti. Ena pa msonkhanowo anali akhrisitu ndipo onse anakhala chete kumvera zimene wolankhulayo ankanena zotsutsana ndi Mulungu. Iye anauza anthuwo kuti kulibe moyo wa uzimu. Kulibe Mulungu, kulibe Khrisitu ndipo kulibe chiyembekezo cha moyo wina uli onse munthu ali ngati china chirichonse alibe mzimu. Iye adabwereza kulankhula zimenezi nthawi yaitali pa msonkhanowo.

Pofuna kuyankhapo pa nkhaniyi ku msonkhanowo, wina mwa akhrisitu adapempha ngati angaloledwe kulankhulapo. Tsono ataloledwa iye adatenga mpando umene adakhalira ndi kuwunyamula m'mwamba ndikuwugwetsa pansi ndipo kenaka adauyang'anitsitsa pa kanthawi. Atatero adapita kutsogolo kwa munthu wolankhula uja ndi kumumenya ku maso ndipo munthu uja adakwiya ndipo adauza anzake kuti amumange.

Ndipo mkulu wa chikomunisiti-yo adafunsa munthu anamuomba pamayo kuti chifukwa chiyani adammenya khofi ku maso?

Ndipo mkhrisituyo adamuyankha kuti wolankhulayo wadzitsutsa pa zomwe anali kubwebweta kuti ndi zabodza. Iye amati anthu onse ndi zina zonse ndi chimodzimodzi zongothera pano pa dziko la pansi ziribe moyo wina kutsogolo. Mkhrisituyo anauza onse kuti iye poyamba anaponya mpando wake pansi ndipo mpandowu sudabwezere koma pamene wakaomba khofu mkulu wolankhulayo, wasonyeza kukwiya ndipo pamenepo padasonyeza kusiyana munthu ndi chinthu china chirichose chopanda moyo kapena mzimu. Chinthu chonga mtengo kaya mwala sichibwezera monga amachita munthu. Izi tsono zasonyeza kuti zomwe amalankhula mkuluyo sizowona ayi koma za bodza. Munthu ndi woposa china chirichonse munthu ndi wa mzimu.

Ndi zambiri zakhala zikulankhulidwa pakati pa akhrisitu ndi achikomunisit m'misonkhano yosiyanasiyana nkudzanso m'ndende. Wina wake m'ndende adafusa mkhrisitu kuti mpaka liti adzakhala akukhalabe mkhrisitu, ndipo pomuyankha ndidati ndawona ambiri a chikomunisiti wosakhulupirira Mulungu akudandaula pa nthawi ya kufa kwawo chifukwa choti sadasamalire za moyo wawo pazaka zonse anali ndi moyo. Iwo pakufa satchula maina ya Marx kapena Lenin kuti awawombole. Atamva nkhaniyi wacikomunisiti adaseka ndi kumvomereza zimene adanena mkhrisitu mzathuyo. Mkhrisitu-yo adaperekanso chitsazo chakuti akatswiri womanga milato yodutsapo njanji sangakhutire kuti mlatowo ndi wolimba chifukwa choti chona kapena mphaka wadutsa pa mlatopo. Koma amatsimikiza kuti mlato ndi wolimba ngati sitima idutsa pa mla-

topo popanda kuthyoka mlato. Ichi ndi chimodzimodzi zinthu zikamayenda bwino sikuti chikomunisiti nchabwino ayi koma chidzadziwika kwenikweni pa nthawi yomaliza. Chitsanzo chinali choti ngakhale a Lenin alemba mabuku ambiri achikomunisiti ku Russia ndipo ngakhale kuti anali Nduna yaikulu ya dzikolo, koma a Lenin-nthawi ina zinthu zitafika poipa adaiwala zachikhulupiriro chawo ndi kupemphera kwa Ambuye. Ife monga akhrisitu kwathu n'kudikira ndipo tichita zinthu mosapupuluma monga mmene achitira a chikomunisiti. Nawonso a Augustine woyera adati "Mtima sukhazikika pokhapokha ukakhala mwa Ambuye.

**Tingawapambane Bwanji Achikomunisiti**

Mpingo wobisikawu mothandizana ndi akhrisitu aku maiko ena komwe kulibe chikomunisiti angathe kugonjetsa machitidwe a chikomunisiti-ndipo dziko la pansi lingasinthe kwenikweni. Mau-wa ndi kulankhula motere chifukwa kunena zowona chikomunisiti ndi chochita kudza sichachirengedwe Ambiri makomunisiti amanena motsimikiza kuti anthufe ndife zolengedwa monga zina ziri zonse kungoti ati akuti ifeyo tinalengedwa mnjiora zina ziri zonse kungoti ati akuti ifeyo tinalengedwa mnjira ina yake ya padera. Iwo amati tiri ngati zolengedwa zina ziri zonse kotero kuti tikafa timakhala mchere, soda kapena miyala ina ya chirengedwe. Tsono pamenepo ukawafusa kuti, "Nanga zimatheka bwanji kuti m'maiko ambiri achikomunisiti ena amapereka miyoyo yawo pa zomwe adazitsimikiza ngati kuti ndi zinthu zoti munthu nkubvutikira pa moyo wake akudziwa kuti mapeto ake adzakhala zinthu

monga zina ziri zonse? Kodi zinthu zopanda moyo zingadzipereke nsembe m'malo mwa ena? Ukawafunsa motere iwo amangokhala chete wosayankha.

Moyo wa nkhaza anthufe timangochita koma sitidalengedwe ndi moyo umenewu. Ndipo munthu sadzakhala ndi moyo wa nkhaza mpakana kalekale. Chitsanzo tidaona umo anthu a Nazi adathera. Anali anthu ankhaza koma lero ali kuti. Ena mwa iwo adadzipha okha pamene ena amwayi anadzitsutsa m'mitima mwawo nalapa ndi kubvomereza kulapa kwawo.

Moyo wachikomunisiti ndi wonyenga ndipo ulibe maziko enieni. Kusimba za anthu aku Russia ndi anthu abwino achifundo ndi wothandiza koma chimawabvuta nchakuti amasokonezeka ndi machitidwe achikomunisiti. Makomunisiti amafunitsitsa atakhala ndi moyo wautali ndi wosangalatsa ichi nchifukwa chake amakonda kuledzera mowa kuti kapena angaonere mwina koma ayi ndithu amangowonabe kuti moyo wawo susintha ichi nchifukwa choti sadziwa kuti ndi chowonadi chokha chimasintha moyo wa munthu.

Nthawi ina ku Bucharest maRussia atangolanda boma la Rumania ndinapita ku nyumba yomwera mowa (beer hall) ndipo pa ulendowu ndidauza mkazi wanga kuti andiperekeze. Titafika kumeneko tidapeza chimpwirikiti chifukwa choti anthu ambiri anali atakhuta kale. Tsono pakati pawo panali msirikali ndi futi yake m'manja, ataledzera koma akufuabe wina mowa. Iye ankaopsyeza anthuwo kuti ngati samupatsa mowa wina awaombera ndiye anthu anali kukhala mowopa. Anthu sadafune kumupatsa wina mowa chifukwa mkuluyo anali atakhuta kale. Ndiye zimene ndidachita ine ndi-

napita kwa mwini wogulitsa mowayo kuti andipatse mabotolo atatu ndi kumutsimikizira kuti ndikakhala pafupi ndi msirikaliyo ndiyo sachita chipongwe china chirichonse. Ine ndi akazi angawo sitimamwa koma iye anapitiriza kumwa mosathekera ndi munthu chifukwa iye anali chidakwa chosamva kuledzera. Ndiye pomwepo ndidayamba kulankhula naye za Khrisitu ndipo anali ndi chidwi cha zomwe ndinkanenazo. Pomaliza adati, "mwandiuza kuti ndinu ndani ndipo inenso ndi kuwuzani za ine." Ine ndine mbusa woyamba wa mpingo wa Orthodox ndipo ndine woyambirira kutsutsa za chikhulupiriro mazunzo atangoyambika ndi Stalin. Ndipo ndinali kupita ku mudzi ndi mudzi kuwauza anthu kuti kulibe Mulungu ndi kuti ineyo pa ubusa wanga ndinali kuwanamiza anthu kuti kunja kuno kuli Mulungu. Ndinali wonama monga m'mene akunamira alaiki ena onse. Ndipo kenaka ndidalowa ntchito ya usilikali wobisika ndipo ndi dzanja langa ili ndapha ambiri. Tsono chimene chikundipangitsa kumwa mowa mwauchidakwa chonchi nkuti kapena nkuiwala ndidachitazo.

Koma zikulephereka kuiwala ngakhale ndimwe chotani.

Ambiri achikomunisiti akhala akudzimangirira ndipo ena mwa wochuka ndi a Essenin mkulu wa ndakatulo zake, a Maiakovski. Ndiponso a Faeev, womwe ntchito yawo inali yolemba mabuku adadzipha atangolemba buku lomwe mutu wake unali "Chimwemwe" m'bukuli ananenamo kuti munthu ungakhale wachisangalalo m'moyo wako ngati sutopa kugwira ntchito yokweza mchitidwe wa chikomunisiti. Koma iye chi-

sangalalo chimene amanenacho ndi chimene chidamupangitsa kuti adziphe ndi mfuti. Ena ndi a Joffe ndi a Tomkin amene anali atsogoleri amphamvu achikomunisiti koma pa mbuyo pake atawona zomwe chikomunisiti chikuchita ndi zotsatira zake sanakondwere chifukwa palibe chabwino adawauza anthu ndiye adangodzipha.

Anthu achikomunisiti si anthu amtendere ayi ngakhale iwo amene ali pa ulamuliro si anthu a mtendere ndi anthu okhalira mphanthi. Mwachitsanzo mtsogoleri wawo Stalin yemwe adapha onse akuluakulu sadakhalebe mu mtendere amangoyenda cheucheu kuopa kuti ena angamuchitire mankhwala kapena ku muthirira ku chakudya. Anali ndi nyumba yaikulu ya zipinda zake zogona zokwana zisanu ndi zitatu. Ndipo panalibe m'modzi amadziwa kuti lero agona chipinda chiti zipinda zonse amazitseka chimodzimdzi. Chakudya samadya wamba pokhapokha waphikayo ayambe kudya pomwepo ndi kuona kuti zonse zri bwino mpamene iye amayamba kudya. Apa tikohoza kuwona tokha kuti chikomunisiti sichibweretsa mtendere ngakhale kwa atsogoleri a maiko achikomunisitiwo chifunika kwa iwo ndi kumulandira Yesu.

Kuthetsa chikomunisiti kungabweretse moyo wina wothandiza wosati kwa iwo wokha ali m'ndende koma kwa aliyese. Mpingo wobisika uli pa ntchito yofunika kwambiri yothandiza kuthetsa mchitidwe woipawu ndipo afuna chithandizo chochokera ku maiko ena amene sali pa mabvuto chifukwa chachipembedzo.

Ntchito ya utumiki wa mpingowo imadziwika ndi mfundo yake ya chikhulupiriro.

Mbusa wina dzina lake George adafotokoza za nkhani ina m'buku lake imene idamuchitikira. Iye adati panali mnyamata wina wake amene anali ndi udindo pakati pa asilikali ngati kaputeni, iyeyu nthawi ina adapita ku Hungary komwe adafuna, kuti akakumane ndi ine pa ndekha. Mnyamatayo anali wodzimva kuti ndi mwamuna pa yekha, wochangamuka ndipo ena anamutsogolera kumene ine ndinali. Atafika pa chitseko cha m'chipinda ndinalimo adaona mtanda pa chitsekocho. Ndipo adati mtandawo ndi wongophimba anthu m'maso makamaka anthu wosauka. Mbusa atatsekula chitsekocho adamulola kuti alowe ndipo ali momwemo kaputeniyo adati iye sadafikire chibwana koma kuti mbusayo anene kuti yesu samukhulupirira kuti ndi mwana wa Mulungu. Mbusayo adaseka ndi kuti.

"Mnyamata ndikukuuza mosabisa kuti ine ndi makhulupirira. Ndipo ndi zowona. Kuti yesu ndi mwana wa mulungu."

"Ine sindinabwerere zocheza ayi kapena kudzataya nthawi kuno ndabwera kuti mundiuze zenizeni. Palibe chifukwa chosekera!" adatero msirikali nkulankhula kwake. Ndipo nthawi yomweyo msilikaliyo adasolola mfuti yake yaying'ono yochedwa volovolo ndi kuyika pa fupi ndi mbusayo. Ndipo mosataya nthawi adalankhulanso moopsyeza kumuuza mbusayu. "Ngati simumvomera kuti Yesu simwana wa Mulungu ine sindichitira mwina ndikuwomberani pompano."

Abusawo adati, "Ndi zowona Yesu ndi mwana wa Mulungu." Pomwepo msirikali-yo adalumpha ndikuponya kumbali kafuti kaja ndi kukankumbatira mbusa uja misozi iri m'maso akusisima ndi mau awa: "Ndi

zowona, ndi zowona ineso ndimakhulupirira." Iye adauza mbusayo kuti samadziwa kuti munthu angakhale ndi chikhulupiriro choti mpakakulolakufa. Msirikaliyo adathokoza mbusa George kuti chikhulupiriro chake chamulimbikitsa msilikali uja kotero kuti nayeso adati ndi wokonzeka kufera dzina la Khrisitu.

Ndikumbukaso nthawi ina yake aRussia atangotenga boma la Rumania asilikali ena awiri adafika ku chalichi ndi futi zawo. Iwo atalowa menemo adanena mokweza ulaliki uli nkati kuti "Sitikhulupirira za chkhulupiriro chanuchi. Ndiye pano onse amene ali kumbali yathu yosakhulupirira chikhrisitu atuluke tisanayembe kukuomberani. Ndipo nthawi yomweyo panali chimpwirikiti anthu kuthawa kumapita ku nyumba zawo. Ndipo anthu pang'ono okha ndiwo adatsalira m'chalichimo. Kenaka asilikali aja adauza otsalirawo kuti iwo ndi amodzi okhulupirira mau a Mulungu ndipo amafuna chiyanjano ndi okhulupirira enieni amene ali okonzeka kufera dzina la Khrisitu. Ndipo pakati pawo panali chimwemwe.

Mnyumba zambiri ku maiko anzathu ku Ulaya tsiku lonse amangokhalira kumvera nyimbo za dziko samaganizaso kuti kunja kulinji. Koma ku Rumania timakhala nazo nyimbozo tikakhala kuti tiri pamapemphero kuti anzathu a nyumba zoyandikana asadziwe kuti tikupemphera kuopa kuti angakatineneze ku boma.

A Wurmbrand anali kuwuza anthu kuti iwo ndi wotumidwa kunena zosezi m'malo mwa ampingo waku Rumania womwe alibe chirichonse koma afuna ine kuti ndikhale wowalankhulira kunja kwa dziko la Rumania. Chonde akufuna mapemphero anu ndi chithandizo chi-

mene mungamatumize kwa akhrisitu a mpingo wobisikawo womwe akuzuzika chifukwa cha Yesu yemweyu.

Chikomunisiti tidzachigonjetsa chifukwa Mulungu ali mbali yathu. Chachiwiri chimene tidzagonjetsere chikomunisiti nchakuti ife tiri ndi uthenga umene umakoza mtima wa munthu.

Akuluakulu ena achikomunisiti ku ndende amene anamangidwa pa nthawi ya ulamulilo wa Nazi adanditsimikizira ine kuti ndi zowona pa nthawi ya masautso anali kupemphera. Ndipo ine ndidaona atsogoleri achikomunisiti akutchula dzina la Yesu pa nthawi yawo ya kufa. Ndiposo machitidwe azinthu zathu siachilendo kapena chisokonezo tiri ndi mabuku ambiri akale osimba za moyo wa chikhrisitu. MaRussia angathe kuletsa kuti anthu asamawerenge mabuku amau a Mulungu. Koma ubwino wake, tiri nawo mabuku akale monga wolembedwa ndi a Tolstoi ndi a Dostoievschi ndipo m'mabukumo anthu amawerengamo za Khrisitu. Chimodzimodzi mabuku a Geothe m'dziko la kubvuma ku Germany, Azienkiewicz ku Poland ndi kwina kotere. Ku Rumania nako kuli wina dzina lake Sadoveanu amene analemba buku loti "Miyoyo ya anthu woyera" bukuli ngakhale achikomunisiti adalilemba ndi mutu wosiyana ndi mutu wake woyambirira komabe anthu oliwerenga amaphunziramobe zofunika. Mabuku a Raphael, Michel-angelo, Leonardo da Vinci amenewa sangayathe kuyasandulizira m'njira ina chifukwa muli zinthuzi zimene zimakumbutsa za Ambuye Yesu.

Pa moyo wanga ndaonaso iwo amene amakhulupirira za zipembedzo zomwe siziri za chikhrisitu kuti asanayambe kulankhula amapemphera kwa Mulungu

kuti awathandize pamene ali kulankhula. Ndaonaso akuluakulu kapena nditi atsogoleri achikomunisiti akupita mwatseri kukapemphera ndi mamembala a chalichi chobisika ndipo pobwera kumeneko akawafusa kuti munali kuti samaulula. Tsono akayankha motero amamva chisoni ndi kulira kuti sanakhulupirike ndiposo awonetsa mantha osayankha zowona zake. Munthu chikhulupiriro chake mwa Ambuye chikamakula satekeseka ndipo sabwerera m'mbuyo. Khrisitu amawakonda anthu achikomunisiti ichi ndi chimodzi chotilimbikitsa kuti anthuwo mapeto ake adzagonjera kwa Yesu Khrisitu. A chalichi chobisika ndi ntchito yawo ku wona kuti akufalitsa uthenga kuli konse ngakhale amu ndende. Monga Yesu adanena kuti lalikirani kwa minthu yonse ndipo sadanene kuti musiye a mndende ayi koma onse amene. Ndipo tingathe kuwalalikira akaidi akumeneko podzera kwa abale a chalichi chobisika m'dziko la Rumania.

**Pali Magulu Atatu Amene Amapanga Chalichi Chobisika**

Gulu loyamba ndi la iwo amene anali azibusa amene adawachotsa m'mipingo yawo chifukwa chakuti sadafune kuchepetsa mphamvu ya mau a Mulungu. Iwowa anamangidwapo. Ndiye lero amakapemphera ku chalichi chobisikacho.

Gulu lachiwiri ndi la asirikali omwe iwowo sikuti ndi akhrisitu wamba koma wodzipereka ndipo kwa iwo sakhulupirira kuti munthu angakhale mkhrisitu osatembenuzapo wina. Gulu limeneli silamasewera ayi ndi akhrisitu amene akulira pakati pa mazuzo koma osate-

keseka. Nyuzipepala ya za chitezo yaku Russia yotchedwa 'Red Star' nthawi ina chifukwa chosazindikira, idadzudzula akhrisitu chifukwa choti ati akhrisitu amafuna aliyense akhale mbali yawo. Koma sadadziwe kuti akhrisitu ndi anthu amene amathandizana pa mabvuto kaya wina wadwala wina wa nyumba ina amakhoza kubwera kudzathandiza mzake.

Boma la chikomunisiti limabvomereza kuti akhrisitu ali ndi njira zambiri zofalitsira uthenga wawo kaya nkumsika, kumadzi usiku monsemo ali ndi njira zawo zolalikira uthenga. Anaso nawo amalandira maphunziro a mau a Mulungu. Pamene boma la chikomunisiti liwonjezera nkhaza zozuzila akhrisitu mpamene akhrisitu amamva kulimbikitsidwa ndikupeza njira zambiri zolalikira mau pakati pa anthu osiyanasiyana.

## Gulu Lachitatu Ndi La Abusa A Chalichi Cha Boma Omwe Kumbali Ndi A Chalichi Chobisika.

Gulu la chitatu ndi la abusa omvomerezedwa ndi boma. M'maiko ambiri achikomunisiti monga ku Yugoslavia, Poland, ndi Hungry azibusa a kumeneko amapezekanso kwambiri ku chalichi chobisika. Iwowa bvuto lake ndi lakuti saloledwa kulankhula za Khrisitu, kupempherera mzawo akadwala kapena kuphunzitsa ana mau a Mulungu. Nchifukwa chake kuti zawo ziyende bwino ku moyo wa uzimu amakasonkhana nawo ku machalichi osamvomerezeka ndi boma komwe amakalimbikitsidwa. Ndipo abusa abomawo akapezeka akuchita zosiyana ndi zimene boma limawauza amawagwira kupita nawo ku ndende zaka zambiri. Kotero

kupita kukapemphera nawo ku chalichi zina sichinthu cha masewera koma kusonyeza kunkonda Khrisitu.

Mkulu wina wake amene amakonda kukayenda ku maiko achikomunsiti, ali komweko amakhala ndi chidwi chofusa anthu a m'maikowo umo ntchito ya Mulungu ikuyendera ndi kuwafusa mipingo yawo. Pomuyankha amamuuza kuti iwo ndi "Ana a Mulungu," Kapena kuti "Wokhulupirira." Ndiye chifukwa cha ichi mkuluyo adawona ngati kuti chalichi chobisika kunalibe. Chifukwatu anuwake kumeneko samadzitcha a chalichi chobisika ayi. Izi ziri ngati utapita ku chigawo chapakati cha ku Afrika ndi kukakumana ndi anthu osaphunzira podzanena ku dziko la kwanu umadzanena kuti sindidawapeze wophunzira ku Afrika. Pamene wophunzirawo aliko koma kuti samadziwa chimene woyendawe umafuna kudziwa. Mwachitsanzo Akhrisitu woyamba sanali kudziwa kuti iwo ndi Aisrael kapena kuti wokhulupirira a Yesu. Mwinaso amati ndi ana a Mulungu. Dzina loti Akhrisitu lidadza mbuyo mwalendo ndipo lidayamba kumveka ku dziko la Antokeya. Ndi chimodzimodzi wotsatira Luther samadziwa kuti ndi a Lutheran ndipo ngakhale Luther mwini wake amakana dzinali zosezo zimachitika chifukwa chosadziwa.

Apa ndifuna kunena kuti dzina loti Chalichi Chobisika linabwera ndi achikomunisiti ndi akhrisitu aku maiko aku Ulaya Kuzambwe. Koma eni ake ku maiko achikomunisitiko sadziwika ndi dzina limenero. Iwo eni ake amangoti ndife Akhrisitu, kapena kuti ana a Mulungu nthawi zina amati Wokhulupirira koma chosecho onsewo amapemphera malo amodzi mobisala n'chifukwa chake amati chalichi chobisika.

Mwachitsazo ungathe kuyenda ku maiko aku Ulaya osamudziwa mtikitiva waku Soviet Union. Ndiye munthu sunganene kuti ku Ulaya kulibe mtikitiva waku Soviet Union. Sizingatheke mtikitiva kudzionetsera kwa anthu oyenda ndiye kuti ntchito yake ithera pomwepo anthu amudziwa ndipo satha kugwira ntchito yake chifukwa waonekera poyera.

# MUTU 6

Ndalankhula zambiri zimene ine ndakumana nazo pa utumiki wachisinsi wofalitsa uthenga wa Khrisitu, wa pakati pa asilikali aku Russia ndi makomunisiti aku Rumania. Ndipo ndikupemphani kuti muthandize kufalitsa uthengawu kwa anthu amene ali kuzuzika chifukwa cha chikhrisitu chawo.

Kodi utumiki wa maso mphenya angawa ungathe "kugwira ntchito?"

Kodi ndi utumiki wothandiza?

Nanga ku Russia, uliko utumiki wa Chalichi Chobisika? Kodi nanga utumikiwo ukugwirabe ntchito mpaka pano?

Pa mafuso utumikiwo ukugwirabe ntchito potsatira pa nkhani zina.

Anthu achikomunisiti lero ali pa chisangalalo choti atha zaka 50 chiyambire cha ulamuliro wawo wachikomunisiti. Koma kusekerera kwawoko ndi kopanda phindu. Woyenera kukondwerera ndi akhrisitu chifukwa ndiwo achita zotheka pa moyo wa munthu wosati chikomunisiti. Kampani yosindikiza nkhani ku Russia ndi yodzadza ndi nkhani za akhrisitu ndipo izi zikudziwika bwino lomwe ndi atolankhani a m'dzikolo. Malinga ndi momwe ziriri zinthu chalichi chobisikacho chikuopsyeza pa ntchito zake ichi nchifukwa chake dziko la Russia likutekeseka ndi ntchito za akhrisitu.

Dziwani ichi kuti chalichi chobisika chiri ngati

chinthu china chake chimene mbali yaikulu sichioneka.

Apatu ndingofuna kufotokoza pang'ono pa nkhani ina yokondweretsa.

Pa 7, November 1966, ku Suhumi kunali msonkhano waukulu wa akhrisitu a chalichi chobisika. Ku msonkhanoko kunafika, Akhrisitu ambiri wochokera ku mizinda, yosiyanasiyana. Ndipo pomaliza pa ulaliki, anthu okwana 47 adalandira Khrisitu ndipo nthawi yomweyo anabatizidwa m'nyanja yotchedwa Black Sea. Zidachitikazo sizidasiyane ndi zimene zinkachitika kale zomwe timawerenga m'buku loyera.

Kale kudalibe nthawi ya malangizo kwa munthu amene wadzipereka kwa Ambuye. Tangoganizani pa zaka 50 zapitazo panalibe mabaibulo, kapena sukulu za seminare ndiponso abusa a mpingo wa chalichi chobisika sadakaphunzire ku sukulu za ubusa.

Ngakhalenso Filipo yemwe adali mkulu wa mpingo sanaphunzitsidwe za mau a Mulungu. Ndipo pamene adakumana ndi mdindo wa Kandake mfumu yaikazi yaku Aitiopiya atamuthandiza za mau aMulungu pa mphindi yochepa, mdindoyo adanena "Taona madzi awo chingandiretse ine kubatizidwa nchiyani?" Filipo anamuyankha "Ngati ukhulupirira ndi mtima wako wonse ukhoza kubatizidwa." Nthawi yomweyo anatsikira ku madziko ndipo mdindoyo anabatizidwa. (Machitidwe Atumwi chapter 8:36-38.

Pa msonkhanowo, akhrisitu a chalichi chobisikacho adalankhula ngati m'mene zinthu zimakhalira m'masiku akale monga mmene timawerengera m'baibulo.

Mnyuzipepala ina ya Teacher's Magazine yapa 23

August 1966, inafotokoza kuti ku Rostov-on-Don a Baptists adakana kuti mpingo wawo ukalembetse ku boma ndikuti azitsatira zofuna za boma la chikomunisiti paza kayendetsedwe ka ntchito yofalitsa uthenga. Ndipo chifukwa cha ichi, padachitika ziwonetsero za ziwawa m'misewu yonse ya mtauniyo. Monga mmene idaliri nthawi ya yesu kuti adachiritsa munthu wodwala pa tsiku la mulungu kunyazitsa Afalisi, nawoso a mpingo wobisikawo anawonetsa nthchito zawo poyera ndi cholinga chonyazitsa zochita za boma la chikomun-siti. Tsono izi zimachitika motere kuti tsiku limene adaliika achikomunisiti kuti ndi lokumbukira chikomu-nisiti chawo ndilomweloso limene akhrisitu amachita zawo kusonyeza kutsutsa machitidwe woipa achikomu-nisiti. Ziwonetsero zawo a Chikomunisitiwo zimachit-ika pa 1 May ndipo ndi pameneso akhrisitu amaonetsera zawo m'misewu yomweyo.

Pa chiwonetsero chomwe chidachitika ku Russia cha boma la chikomunisiti, kudapitaso akhrisitu wok-wana 15-handeredi amene naoso anakaguba m'misewu mosawopa kuti kuteroko angathe kumangidwa. Akhri-situwo, amadziwa kuti ndende zikudikira iwo nkudzaso mabvuto ena ali wonse. Ndipo chifukwa cha chikondi chawo pa maso pa Mulungu adawonabe kuti kunali kofunikira kuti akhrisituwo akawonetse zionetsero zawo zotsutsana ndi mchitidwe wa chikomunsiti. Ku Russia amadziwa bwino za lamulo loopsya lomwe a mpingo wa Evangelical adaalilemba kuti ngati akhrisitu achita zin-thu zosiyana ndi lamulo la bomalo amalandira chirango cha kupha. Mwachitsazo mlongo Hmara waku mudzi wa Kulunda adalandira uthenga womuuza kuti mwam-

una wake ku ndende anafa kotero kuti mwamunayo anasiya mkaziyo ndi ana anayi. Mtembo wa bambowo utafika, mayiwo, adaona kuti mwamunayo anali ndi zibambi zotenthedwa ndi moto m'manja ndi ku mapazi, komaso pasi pa mchombo panali pobaidwa ndi mpeni mwendo waku dzanja wotupa ndipo thupi lonse linali losakazika ndi mabala. Ndiye ngakhale onse adadziwa za mmene mzawo adafera sadachite mantha adadziperеka kufa infa ya mtundu wina uli onse.

Pa maliro a mzawoyo, padali anthu ambiri ndipo onse adatenga zikwangwani m'manja zolembapo kuti

"Musaope iwo amene amapha thupi ndi kulephera kupha mzimu" Ku mandako ndidaona mimbunda ya iwo adafa chifukwa cha mau a Mulungu.

Chitsazo cha anthu ophedwa motere chifukwa cha chikhulupiriro chawo chidalimbikitsa anthu aku Rostov-on-Don. Anthu adasonkhana mu unyinji wawo pafupi ndi nyumba ina yake ya mphepete mwa msewu ndipo ena mwa iwo chifukwa chakuchuluka anthuwo adakwera m'mitengo ena anakhala pafupi ndi tsidwi za nyumba ndipo pa nthawiyo zidaoneka ngati nthawi ya Zakeyo pamene adakwera m'mwamba kuti akamuone Yesu pamene azikadutsa mnjira. Unali msonkhano wodabwitsa ndipo anthu amene adatembenuka mtima adakwana 80 ambiri mwa anthuwo anali achinyamata. 23 mwa anyamatawo anali a bungwe la chikomunsiti. Pomaliza pa msonkhanowo anthu wonse adayenda mu mzindawo pa umodzi wawo ulendo waku mtsinje kukabatizidwa. Iyi inali nthawi yochititsa chidwi ndi yopambana kwambiri.

Boma la chikomunisiti litaona chikhamu cha anthu

chotere lidatekeseka ndi kutumiza asilikali m'galimoto zingapo futi ziri m'manja kuti akagwire iwo amene amatsogolera msonkhanowo, Chifukwatu kudali kobvuta kuti akagwire anthu onse 15-handeredi. Asirikaliwo atafika adakapeza anthuwo atafika kale ku mtsinje ndipo asilikaliwo adakafika komweko ndi kuwazungulira. Akhrisituwo atawona zimene ankafuna kuchita asirikali pa malopo, onse adagwada ndikupemphera pamodzi kupempha Mulungu kuti ateteze anthu ake ndi kuwalola anthuwo kuti atsirize ntchito yawo yobatiza anthu adadziperekawo. Ndipo zikuchitika izi, ena mwa abale ndi alongo adayima mwakuzungulira wobatizawo kuti asirikali asapeze mpata osokoneza mwambo wa ubatizowo. Ndipo zinthu pa mwambowo zinafika pobvuta kwambiri.

Ku Rostov kudamvekaso malipoti woti anthu a mpingo wa Baptist ali ndi kampani yosindikiza mabuku a mau a Mulungu yomwe akuyendetsa mobisa. Mabukuwo ndi wolimbikitsa ana kuti azikhala ndi chikhulupiriro chozama pa mau a Mulungu. Akuluakulu osindikiza mabukuwo akumalemba nkhani yofotokonzera makolo kuti aziwalola ana awo kumakhala nawo pa mwambo woika maliro kuti anawo asamachiwona ngati chinthu choopsya, koma kuti azidziwa kuti kufa ndi njira yopita ku moyo wina watsopano. Makolowo akuwauzaso kuti azikhala ndi nthawi yokwanira yomaphunzitsa ana sukulu sande kuti anawo azidziwa choyankha achikomunisiti akamafuna kuwasokoneza ndi chiphunzitso chawo cha chikomunisiti.

Mnyuzi pepala ya Teacher's Magazine amalembamo nkhani zosiyanasiyana kuwuza aphunzitsi kuti

azilimbikira ntchito yawo asamakhala amanyazi pophunzitsa ana pa za moyo wa uzimu. Ndiposo amafotokozamo za mirandu imene achikomunisiti amazenga nayo akhrisitu.

A mpingo wa tichalichi chobisika ndi anthu wolimba mtima kwambiri ndiponso wopirira ndi wopanda mantha. Anthu amenewa nthawi ina yake adakaima pa likulu la boma la chikomunisiti ku Russia, kukauza bomalo kuti akhrisitu azikhala ndi ufulu wachipembedzo chawo m'dzikolo. Iwo adapita ku bomako mosawopa kuti akamenyedwa, kapena kutengedwa ku ndende.

Atsogoleri a mpingo wa Baptist womweso ndi a chalichi chobisika alinso ndi zikalata zosimba fundo zosonyeza kusagwirizana ndi zochita za boma la chikomunisiti monga pa zomwe amachita a Karev zomakondwera asirikali achikomunisiti akamapha akhrisitu. M'zikalatazo amalembamo kuti iwo akhrisitu azikhala ndi ufulu wachipembedzo m'dzikomo. Ina mwa kalata ya mtundu umenewu yolembedwa, "Moyo wa lero ku Soviet Union." Adaitumiza ku maiko aku Ulaya mozembetsa. Mkalatayo muli nkhani yosimba za chiwonetsero cha akhrisitu chosonyeza kusakondwa chifukwa choti ku Soviet Union alibe ufulu wolalikira poyera. Ndipo kalata imeneyi idalembedwa motere:-

**Nkhani Yofunika Mwansanga**

Abale ndi alongo wokondedwa, tikufunirani madalitso opambana ndi mtendere wochokera kwa Mulungu ndi Ambuye wathu Yesu Khrisitu. Tikukudziwitsani kuti pa 16 May 1966, nthumwi za mpingo wa Baptist,

zokwana 5-handeredi zinapita ku mzinda wa Moscow ku Russia ku ofesi yaikulu ya bomalo ndi kukaliuza bomalo kuti zonena za akhrisitu azizigwiritsa ntchito makamaka pa mfundo yoti akhrisitu azikhala mwa mtendere ndi kumatumikira Mulungu wawo popanda choletsa. Paulendowo, adatenga kalata Yokapereka kwa Mlembi wamkulu wa boma la Russia-lo a Brezhnev. Ndipo anthu 5-handerediwo adakhala pa bwalo la ofesilo tsiku la thunthu. Iyi inali nthawi yoyamba kuti akhrisituwo awonetse kuipidwa kwawo ndi zochita za bomalo. Pakutha pa chionetserocho, anthu anadandaula kuti a stroganov amakana kuwatengera mthenga woti adzatule kwa a Brezhnev ndipo ankawaopsyeza kuti awamanga ndi kuwachita china chirichose.

Ndipo anthuwo malingana nkusagwirizana komwe kudalipo, adakhala pa msewu wapa nyumba ya ofesiyo usiku onse. Ndipo ena amabwera ndi galimoto zawo kumadzawathira matope, kumawaseka ndi kuwanyoza. Ndipo ngakhale kumagwa mvula akhrisituwo sadatekeseke adakhalabe pa malopo mpaka m'mawa. Pa tsiku limeneli anthu 5-handeredi-wo adawaiola kuti alowe mu ofesiyo kuti akakumane ndi maofisala ang'ono. Koma akhrisituwo adakana chifukwa kawirikawiri akapita kumeneko ndi zifukwa amakonda kuwamenya ndi kuwachita za chipongwe zosiyanasiyana chocho adafuna akumane ndi wamkulu weniweni Brezhnev. Ndiye zinthu zitafika pothetsa nzeru, chimene adachita a bomalo ndi kutumiza mabasi okwana 28 kukawatengapo anthuwo ndikupita nawo ku ndende. Pamene asirikali amafika pa malopo, panali kulimbana kwambiri kuwamenya akhrisitu mopanda chisoni. Akhrisituwo

anagwirana manja molimba, nyimbo ya Mulungu irimkati ya mau ake otere:- "Masiku athu abwino m'moyo uno, ndi masiku amene tinganyamule mtanda wa Khrisitu" Kumenyako kunapitirira anali kuwamenya ku maso ndi kuwaguza, ndi kumakawaponya m'mabasi kuyimba kuli mkatibe osaleka anthu a Mulungu. Ambiri aiwo anali kukawaika m'basi poguza tsitsi lawo. Ndipo kwa akhrisitu amene amachita mnjunju kapena kusonyeza kukana amamenyedwa mpaka kukomoka. Onse atadzala m'mabasimo anapita nawo ku malo komwe samadziwa kuti akupita kuti. Ndipo nyimba zidamvekabe m'mabasimo.

Zitangochitika izi, abale awiri anafika pa ofesi pompaja, iwowa ndi mbale G. Bins ndi mbale Horev. Zinthu zidachitika ngati muja zidachitikira kwa Yohane mbatizi kuti atangomangidwa, nthawi yomweyo Yeşu adayamba ntchito yake yolalikira uthenga umene Yohane adabvutikira. "Lapani chifukwa ufumu wa Mulungu wakumwamba wayandikira." Anthu awiriwa adafusa boma kuti awauze kumene adapita nawo akhrisituwo ndi kuti awamasule. Kenako abalewo sadaonekeso, ndipo patapita nthawi zidamveka kuti anawaika m'ndende yaku Lefortovskaia.

Anthu a mpingo wobisikawu anali anthu opanda mantha chifukwa zitangotha izi, adalembaso chikalata china chonena kuti "kwapatsidwa kwa inu kwa ufulu chifukwa cha Khrsitu si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa chifukwa cha iye." (Afilipi 1:29) Ndipo Akhrisituwo amalimbikitsana ndi mau apa buku la (I Atesalonika 3:3) "Kuti asasunthike wina ndi zisautso izi, pakuti mudziwa nokha kuti adatiika ife

tichite izi." Komaso amagwiritsa mau apa buku la (Ahebri 12:2) "Yesu ameneyo, chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pa maso pache anapirira mtanda, nanyoza manyazi, nakhala pa dzanja la manja la mpando wa chifumu wa Mulungu."

Chalichi chobisika chimaonetsera poyera kuti zimene achita achikomunisiti ndi zinthu zakutha ndi zoononga. Akhrisituwo amadana ndi zomwe amachita ku Rostov ndi ku Moscow zomaphunzitsa ana maphunziro achikomunisiti womwe cholinga chawo ndi kuononga ana kuti asadziwe za uzimu. Akhrisitu a chalichi-chi akuchita zotheka kutsutsa atsogoleri a chalichi zomvomerezeka ndi boma kuti asamangolandira ziri zonse zochokera ku boma zimene amalemba m'nyuzi pepala zawo zoti, "Masiku ano satana ali pa ulamuliro ndi kuti chirichonse chonenedwa ndi boma kaya ndi chotsutsa malamulo a Mulungu a chalichi azingomvomereza." Nkhaniyi idalembedwa pa 4 October, 1966. Nkhani inaso imene idalengezedwa inali yokhudza a Alexei Neverov, Boris Garmashov ndi Axen Zubov amene adapezeka ndi mlandu chifukwa chomvera ulaliki wapa wailesi wumene umalakikidwa ku Amerika. Anyamatawo adatepa ulalikiwo ndi kugawira anzawo kuti nawo akamve za uthengawo. Nkhani ina yomwe anawayimbira mlandu ndi yoti ankachititsa misonkhano mwatseri monga momwe ankachitira wokhulupirira woyamba mu mzinda wa Roma.

Pa nyuzipepala ya pa mwezi wa September 15 1966, padaliso nkhani yodandaula kuti akhrisitu akungolalikira poyera mosasamala lamulo loletsa kulalikira pali ponse. Ndipo china chimene adalemba mnyuzi-yo

ndi chonena kuti mu sitima yochoka ku Reni kupita ku Chisinau munali anyamata atatu ndi asungwana anayi anali kuyimba nyimbo za Mulungu njira yonse. Ndipo mnyimbomo amati "Tiyeni tiwapereke ana athu kwa Khrisitu." Amene amapereka lipoti la nkhaniyi anadandaula chifukwa cha mchitidwe umenewu womalalikira pali ponse msitima, m'basi pa siteshoni m'misika ndi malo ena otere. Izi ndi ntchito zake za utumiki wa chalichi chobisika, m'dziko la Russia.

Pa nthawi yozenga mlanduwo, anati akhrisituwo ndi wolakwa chifukwa anali kuyimba malo osaloledwa. Ndipo Akhrisitu atangomva zimenezo onse pamodzi adagwada pansi ndi kufuula kuti: "Tipereka miyoyo yathu m'dzanja lanu Mulungu. Tikuthokozani Ambuye chifukwa choti mwalola kuti ife tikazuzike chifukwa cha chikhulupiriro chimenechi." Ndipo atagamula mlanduwo kuti anjatidwe, nthawi yomweyo anthu mu khotimo adayamba kuyimba nyimbo yomweyo, imene anzawo amangidwa nayo.

Pa mwezi wa May, akhrisitu a m'mudzi wa Copceag ndi mudzi wa Zaharovka adakoza msonkhano wamapemphero omwe adakachitira ku nkhalango chifukwa choti m'midzimo mudalibe nyumba zopemphereramo. Nthawi zina amakhonza misonkhano yonga ngati yokondwerera kubadwa kwa mzawo pamene inali misonkhano ya mapemphero. Ndipo misonkhano yotereyi imachitika chaka chonse. Mpingo wa chalichi chobisika sudasiye ntchito yake chifukwa chomangidwa kapena kuphedwa ayi monganso mmene zinaliri kwa akhrisitu woyambirira m'masiku akale.

Nyuzipepala ina imene imanenanso zambiri za

mazuzo akhrisitu ku Russia ndi ya Prada Ukraini ndipo yapa mwezi wa 4 October 1966, adanenamo zambiri zosimba za mbale Prokofiev yemwe ndi mmodzi watsogoleri a chalichi chobisika. Iyeyu wakhala akumangidwa kawirikawiri chifukwa choyambitsa maphunziro a sukulu Sande. Iye adafotokoza kuti ndende yaku maiko ena monga ku Ulaya iriko bwino akaidi amaona popumira koma ndende zaku maiko achikomunisiti ndi ndende zowopsya kwambiri ndipo mndendemo muli mazuzo osasimbika monga, njara kumenyedwa kwa kupha ndi kumpanga munthu kuti asamaganize pa yekha koma kuti boma liziganiza m'malo mwa munthu; kumene kuli kumpusitsa munthu.

China chimene amachita atsogoleri a chalichi chobisika ndi kusindikiza mabuku a mau a Mulungu koma pa chikuto ndi kuikapo zina zonga za chikomunisiti ndi mkati pang'ono koma pamene mkati mwenimweni muli chiphunzitso cha mau a Mulungu. Kuteroko nkuphimba m'maso boma kuti lisadziwe. Kuti ndi mau a mulungu.

Nkhani zina zimene zimalembedwa zimakhala zonamizira akhrisitu pofuna kuwononga utumiki wawo mwina kuwanamizira kuti awononga nyumba zopemphereramo kapenaso kunena kuti adana ndi akhrisitu anzawo. Izi sizikusiyana ndi zimene ankamunamizira Yesu pamene a Falisi, a Saduki ndi Alembi ankamupereka Yesu kwa mfumu Pilato. Koma ngakhale pali manenedwe otere anzathu a chalichi chobisikacho sanabwerere m'mbuyo pa utumiki wawo. Pamene zinthu zifika poipa mpamene mamembala a mpingowo amankabe patsogolo pa ntchito yawo.

Pakalata ina yake imene idalembedwa pa 27 April 1966, adalembamo kalata yolembera Nadia ndipo kalatayo inali yotere;

Tamverani Mpongozi Nadia, ndikufunirani madalitso onse ochokera kwa Ambuye wathu wokondedwa. Iye amakukondani kwambiri, ndipo ife sitiri kanthu pa maso pake. Mpongozi Nadia ndiri ndi chikhulupiriro kuti mau awa mumawadziwa: "Uzikonda adani ako, ndi kuwadalitsa iwo amene amakunyoza ndi kuwachitira zabwino iwo amene adana nawe ndipo apempherereni amene, amakugwiritsani ntchito mosayenera." A Peter Serebrennikov omwe adathandiza anyamata ambiri achikomunisiti kulandira Ambuye adawamanga. Ndipo akuti a bomalo adawerengaso zomwe adanena mkuluyu kuti sangamvere zina ziri zonse chomwe akudziwa iye nchakuti kwa iye lamulo la mphamvu ndi baibulo. Iye adanena mauwa pamene a boma adamuuza kuti boma la chikomunisiti sirilora mwana kapena wa chinyamata kumuuza za mau a Mulungu. Tsono iye mkuyankha kwake adati adzamvera baibulo kusiyana ndi zina zonse.

Mnyuzi pepala ina yotchedwa Sovietskaia Justitia NO 9 ya 1966, adasimbamo zambiri za mmene anthu amachitira misonkhano yawo nthawi ya usiku. Nyuziyo idati anthu amadzaza m'nyumba yobisika kotero kuti samatha kugwada chifukwa chosowa malo. Kanyali kawo kamene amagwiritsa ntchito ndi kochepa konga kakaliboli ndipo anthuwo amadza thukuta chifukwa chakuchepa kwa chipindacho. Akamapemphera wina amakhala ali kunja kuona ngati kukubwera apolisi. Mtsikana yemwe dzina lake ndi Nina pa nthawi yake yoyamba kukapemphera kumeneko anadabwa kwam-

biri ndi mmene adamulandirira ku msonkhanowo. Akhrisitu ku msonkhanowo, adamulandira ndi chisangalalo chimene wina aliyense sanamuchitirepo. Iye adanena poyera kuti tsopano adawona kuwunika m'moyo wake ndipo sangasamale ngakhale maofisala aboma atamangomudutsa osamulankhulitsa kaya ngakhale atamamunenera mau onyoza chotani kwa iye sangazigwiritse ntchito chifukwa walandira chowonadi. Enaso mwa anyamata adakalowa nawo ku mapemphero adatsimikiza kumutumikira Khrisitu.

Akhrisitu akawatenga kokawazenga mlandu ndi kuwafusa chifukwa chiyani amafuna onse atalowa mpingo wawo omwe ndi oletsedwa. Mlongo wina anayankha woweruzawo kuti "Cholinga chathu nkuti dziko lonse likamudziwe Khrisitu. Woweruzayo adanena mwa ukali kuti "Chipempedzo chanu sichanzeru zakuya za sayansi." Mtsikanayo adauza mkuluyo kuti sadziwa zambiri za sayansi monga mmene amadziwira Einstein kapena Newton awa ndi akatswiri aza sayasi koma anali wokhulupiriria. Mtsikanayo adauza bwalo kuti ngati sayasi yathu sitidziwa nayo Mulungu tiri chabe ndipo tidzafa mchibvundi. Ndiposo pali ambiri ophunzira monga a Pavlov komaso iwo amene mumawadalira a Marx adanena kuti chikhrisitu chimachotsa chimo pa moyo wa munthu. Ndiye mkazi-yo adati chimodzimodzi iye anali wochimwa koma chikhrisitu chinamuchotsera chimo. Ndiye adafusa bwalolo kuti nanga pali chifukwa chiyani chomuyimbira mlandu. Ndiye akuti atalankhula motero bwalo lonse linamgokhala chete kusowa chonena. Pa mlandu wokhala ngati womwewu, woimbidwa mlandu adatsimikizira abwalo

kuti pakati pawo panalibe wodziwa kwambiri ngati a Simpson womwe adatulukira mankhwala osiyana-siyana. Koma a Simpson-wo nthawi ina atawafusa ntchito yawo, iwo adayankha kuti kwa iwo simankhwala adatulukirawo ayi koma kuti adazindikira kuti anali munthu wochimwa ndi kuti mwachisomo cha Mulungu anapulumutsidwa.

Akhrisitu-wo ndi wolimba ndi wogwirizana ndi-poso wokonzeka kufa chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Iwo ndi wokondana ndi womangirirana chi-fukwa chachikondi cha mpulumutsi wawo. Tsono pa chifukwa ichi nkobvuta kuwatha akhrisitu.

Mkalata ina yake yomwe adasindikiza a mpingo wobisikawo adalembamo kuti, "Ife sitirikupemphera ndi cholinga choti tikhale akhrisitu wopeza bwino koma kuti tikhale akhrisitu amene Mulungu amawadalira: Akhrisitu wofanana ndi Khrisitu, akhrisitu amene ali wokonzeka kunyamula mtanda wa Yesu chifukwa cha ulemerero wa Mulungu."

Mnkhani inaso imene idalembedwa pa 15 January 1966, inali yosimba milandu ya anthu angapo ndipo wina wa iwo ndi mtsikana dzina lake Maria Sevciuk. Iye adamufusa kuti ndi ndani adamtengera kwa Khrisitu. Iye poyankha adati, "Mulungu ndiye adanditengera ine ku mpingo wake." Ndipo wina adamufusa kodi mtso-goleri wako ndani? Iye poyankha adati alibe mtsogoleri monga munthu.

Ana pa mlandu womwewo adawafusa kuti ndi ndani wati muchotse matayi a boma pa khosi panu. Iwo poyankha adati adachotsa matayiwo mwakufuna kwawo. Pokabatizana, anthuwo amabvala zophimba ku

maso kuti a boma asawadziwe.

Nthawi ina yake, panali msonkhano wofotokoza za phunziro la chikomunisiti ndipo utantha msonkhanowo, wokhulupirira amene anakamvera nawo msonkhanowo, anawafusa komwe anakaphunzira za chikomunisiti chomwe iwo eni ake sachitsatira monga kuti usabe, usaphe. Akhrisituwo adauza amalankhula ku msonkhanowo kuti iwo monga akhrisitu, zawo zonse zimachokera m'baibulo lomwe achikomunisiti amatsutsana nalo. Ndiye pomwepo zinthu zidasokonezeka akhrisitu adawonetsa luntha lawo ndipo manyazi anali kwa achikomunisitiwo.

## Mazuzo Akupitirirabe Pakati Pa Akhrisitu.

Anthu achikomunsiti ku Russia akupitirizabe kuzuza anthu opemphera cholinga cha boma laku Russia nkuthetsa chalitchi chobisika. Pakali pano anthu ambiri akutengedwa ku ndende. Malipoti aposachedwa akuti ku malo kwina anthu 82 adakawaika ku malo ena ndi kumanena kuti anthuwo ndi wopenga kapena kuti amisala. Ndipo ena 24 adafa patangotha masiku ochepa chifukwa ati "adapemphera nthawi yaitali" Chodabwitsa nchakuti kuyambira liti munthu anafapo chifukwa chopemphera nthawi yaitali. Apa tikhoza kuwona kuti anthuwo anawazuza mpaka kufa. Chirango china chimene amachita kwa makolo opemphera ntchakuti ngati apezeka akuphunzitsa ana awo anawo amawalanda ndi kupita nawo kwina komwe sadzabweraso mpakana kutha kwa moyo wawo.

Pa msonkhano wa bungwe la United Nations pomwe dziko la Soviet Union lidalipo adagwirizana kuti

anthu a m'maiko azikhala ndi ufulu wophunzirira pamodzi komaso kuti anthu azikhala ndi ufulu wa chipembedzo chimene afuna.

Pa nkhaniyo a Karev mtsogoleri wa tchalichi cha boma ku Russia adalemba m'nyuzipepala kuti zimene amagwirizana ku United Nations za ufulu wa sukulu ndi chipembedzo ndi zimene zinali kuchitika ku Russia lomwe lidaali bodza la poyera. Koma tamvani tsono pofuna kutsutsa za nkhaniyi: Mai Markrinkowa amene anali ndi ana 6, anawo lidadzawatenga boma ndikukawaika ku sukulu kwina chifukwa choti mai-wo anali kuwaphunzitsa za Chauta komaso samawalola kumvala matayi. Mayi Markrinkowa polankhulapo za nkhaniyi, iwo anati, "Ine ndikuzuzika chifukwa cha chikhulupiriro." Boma lidauza mayiwo kuti aziwalipirira ana ake ku sukulu kumene ali komwe tsopano akuphunzira maphunziro achikomunisiti. Nkhani imeneyi idamvetsa chisoni azimai ambiri m'deralo.

Pa nkhani ina ya mtundu womwewu, makolo adafusidwa kuti ayankhe ngati akufuna Mulungu kapena mwana wawo wa mkazi amene boma lidalanda pa banjapo. Bambo poyankha adati sadzasiya chikhulupiriro chawo.

Paul anati nkulankhula kwake "Zonse zichitira ubwino." Ndawona ana omwe adachotsedwa pakati pa makolo awo chifukwa choti makolowo amawaphunzitsa mau a Mulungu, kuti anawo kumene adapitako m'malo moti akagwiritse ntchito zomwe boma limafuna kuti adziwe anawo samazigwiritsa ntchito m'malo mwake amaphunzitsa ana anzawo za moyo wa chikhrisitu.

Baibulo limati iwo amene akonda ana awo kuposa

Yesu sali ache a iye. Mau awa ali ndi tanthauzo kwa anthu amene ali kuzuzika m'ndende. Tangoyesani muthe sabata osawaona ana anu mpamene mungadziwe bvuto ali nalo azathu ku Russia.

Akhrisitu wochuluka kuphatikizapo azibusa, alaliki, mabishopu, adutsa m'mabvuto olekanalekana. Mndende zawo. Mulibe chirichonse choti angamawerenge, kulibe kudya m'gonero, kulibe kudzozedwa, kapena kumvala zomvala zaukalasitiya kapena kuwona zinthu monga timazionera m'machalichi ena ayi. Chakudya nacho ndi chaumve chosakwanira komaso chodya pa nthawi; zosezitu nchifukwa cha chikhulupiriro chawo mwa Khrisitu. Chomwe chiri pafupi ndi azathu ali kukaidiwo ndi pemphero lolankhula ndi Mulungu ndipo Mulungu amawalimbikitsa ndi kuwadzoza mwa padera pa masautso awo.

Umu ndi mmene zinthu ziriri ku Russia. Mtsogoleri wina wake ku Russia Archbishop Yermogen waku Kaluga sakudziwika kumene ali chifukwa choti adakana mpingo wake kuti ugwirizane ndi chalichi chimene amati cha boma ku Russia-ko.

Papita zaka makumi asanu tsopano, chikhazikitsire cha chalichi chobisika m'dziko la Russia. Ndipo chozwizwitsa nchakuti mpaka pano mpingowu ukupitabe patsogolo kutumikira Mulungu ngakhale kuti umakumana ndi zowopsya zimene amawachitira achikomunisiti. Maiko a chikomunisiti tingathe kuwagonjetsa ngati tonse akhrisitu titapitiriza kugwirizana ndi kumathandizana pa ntchitoyi.

Pofuna kuti anzathu ena adziwe m'mene achipembedzo chobisika amalankhulira pa masautso awo

ndafuna ndikuwonetseni makalata angapo wosimba za akhrisitu azathuwo.

### Mmene Varia Mtsikana Wa Chikomunisiti Adamlandirira Khrisitu Komaso Mmene Amachitira Umboni

Makalata oyambirira atatu ndi wochokera kwa Maria amene adatembenuza mai Varia kukhala wache wa Khrisitu.

.....Ine ndikanalipo ndi moyo ndipo iwo amene andiyang'anira amandikonda. Tsiku lina wina mwa atsikana amene amatiyang'anira adati sakutha kumvetsa kuti ndine munthu wa mtundu wanji, powona kuti amandizuza ndi kundichitira chipongwe china chirichonse koma ine sindibwezera m'malo mwake ndi masonyeza chikondi kwa iye. Pomuyankha ndinamuuza kuti Mulungu adatiphunzitsa kuti tizikonda aliyense osati abwezi okha koma ndi adani omwe. Mtsikanayu asanafike pondizuza kwambiri ndidampempherera mokhudzidwa kwambiri. Atandifusa ngati ineyo ndi mankondaso mtsikanayo, ine mwakumusonyeza chikondi chonse ndinankumbatira ndipo tonse tinalira. Lero pano ndikamba pano tikupempherera pamodzi.

Chonde muikizeni m'mapemphero dzina lake ndi Varia.

Monga mwa nkhaniyi, ukamamva ena akukana Mulungu zimangowoneka ngati akunena zowona. Koma moyo umasonyezabe kuti pasi pa mtima pali chilakolako chofuna Mulungu. Anthu wotere amafuna kena kake koti kakakwaniritse mtima wawo.

Ndine mlongo wanu mwa Khrisitu, Maria

**Kalata Ya Chiwiri,**

Mkalata yanga yoyamba ndinakuwuzani za mtsikana wachikomunisiti Varia. Tsopano ndikuwuzani anzanga wokondedwa kuti Varia walandira Khrisitu kukhala mpulumutsi wake motero kuti akuchitira umboni za Yesu kwa munthu aliyense. Atangomlandira Khrisitu adayamba kumva chisoni pokumbuka zimene ankanena zoti kulibe Mulungu. Pano akutsimikiza kuti kuli Mulungu.

Pa ulendo wina wake wopita ku msonkhano wa anthu akunja achi komunisiti, tidapitira limodzi ndipo ine ndidamuuza Varia kuti akayambe wakhala cheter. Koma sadathe kuwugwira mtima. Pamene nyimbo zinkayimbidwa za chikomunisiti iye Varia sadaimbe nawo ndipo kenaka adapempha kuti alankhule. Ndiye wonse achikomunisiti pa msonkhanowo anadabwa pomva kuti amalankhula zina zosiyana ndi chikomunisiti. Mtsikanayo, adatsimikizira anthu aku msonkhanowo kuti kumwamba kuli Mulungu. Iye adati poyamba samadziwa ndipo adapempha iwo amene sakudziwa za ici kuti nawonso atembenuke chifukwa ngati satero adzalangika ndi chirango chowopsya.

Anthu onse ku msonkhanowo adangokhala chete ndipo mtsikanayo adaimba nyimbo ya Mulungu mogwira mtima. Mawu a nyimboyo anali wotere: "Sindichita manyazi kulalikira dzina la Yesu amene anandifera kundiwombola podzera pa infa yake yapa mtanda." Ndipo pakutha pa zonse anthu kumeneko adafuwula nati 'Atitengera Varia, atitengera Varia." Panopa sitidziwa kumene ali Varia Mulungu yekha ndiye adziwa

amene adampulumutsa iye. Mpemphereni!

Ndine wanu Maria

**Kalata Ya Chitatu**

Patangotha masiku ochepa ndidadzatulukira kuti Varia ali mndende, moyo wanga udadzala ndi chisoni chifukwa Varia ndi mwana wa mng'ono wažaka 19 mwana wokonda Ambuye koma chisoni kuti nthawi zambiri amakhala ndi njara. Titadziwa tsono kuti ali ku ndende tidayamba kumutumizira zakudya koma tsoka ilo samalandira zonse ayi.

Nthawi ina nditakumana naye adandimvetsa chisoni chifukwa anali woonda chifukwa cha njara komaso chifukwa chomenyedwa. Iye adandiuza monditsimikiza kuti iwo amene sadalawe chikondi cha Khrisitu sangathe kumvetsa pa zobvuta zimene timakumana nazo. Komatu ndi wokhawokha adamulandira Yesu amene sangasamale zobvuta zina ziri zonse. Pamene ndimalankhula naye pa windo la zitsulo laku ndende ndidamufusa ngati akudandaula chifukwa cholandira Yesu kukhala mpulumutsi wake. Iye adandiyankha kuti sadandaula mpang'ono ponse ndipo atati amutulutsa adati akhoza kupitaso kukawachitira umboni.

Ndikupemphani tsono abale kuti tipitirize kumupempherera chifukwa zobvala amulanda mwina angamutumize ku Siberia. Ndipo ngati kuli tero, zinthu zomwe ndidalandira kwa abale zoti ndi mupatse ndi mupatsa akamanyamuka. Varia ndi mwana wokonda Ambuye ndipo ali ndi chimwemwe pa moyo wake ndiri ndi chikhulupiriro kuti Mulungu apitiriza kumulimbikitsa. Ndipemphero langa kuti Mulungu amuyang'anire.

Ndine Maria

**Kalata Ya Chinayi**

Mzanga wokondedwa Maria, ndiri wokondwa kukulembera kalata. Ife kuno tinafika bwino ndipo kumalo tikukhala pali mtunda wa 10 mailosi kuchokera ku tawuni sindinganene zambiri za moyo wanga poti zose ukuzidziwa. Ine ndithokoza Mulungu chifukwa chondisamalira. Moti ndimatha kugwira ntchito bwino lomwe. Ine ndi mzanga X timagwira ntchito mu wakishopu ndipo ntchito timagwirayo ndi yotopetsa kotero kuti Chemwali X amalephera kuitha ndiye chimene ndimachita nchakuti ine ndikamaliza ndimamthandiza iye. Pa tsiku timagwira mawola 12 nthawi zina 13 chakudya chathu chiri ngati chakumeneko chochepa. Komabe izi ndi zosadetsa nkhawa.

Moyo wanga uthokoza Mulungu chifukwa choti adandikumaniza ndi iweyo kuti ine ndikalandile chipulumutso. Pano ndi madziwa cholinga cha moyo wanga ndi chifukwa chomwe ndikuzuzikira. Nthawi zonse ndimakhala ndi chirakolako chochitira umboni dzina la Yesu ndi chipulumutso chimene ndiri nacho. Ndi ndani angandisiyanitse ine chikondi changa ndi Mulungu wanga. Palibe ngakhale ndende kapena zuzo lirilonse sizingathe kundisiyanitsa ndi Mulungu wanga. Mabvuto wa ndi njira imene Mulungu akutirimbikitsa. Mndende ndimangokhalira kutozedwa ndipo amandipatsa ntchito yambiri ati poti ndimalankhulalankhula za umboni wanga. Ndingakhale bwanji chete pamene ndikudziwa kuti moyo wanga udali nichitayiko. Ine ndidzapitirizabe kulankhula ndi kuchitira umboni kwa aliyense za chikondi cha Mulungu.

Pamene timapita ku ndende kwathuko, pa njira

tinakumana ndi abale ndi alongo mwa Yesu. Poyamba kunali kobvuta kulankhula nawo chifukwa sungadziwe kuti anthuwa ndi andani koma kenaka ukazindikira kuti ndi abale umadzala ndi chimwemwe. pa njira tinakumanaso ndi mayi wina amene anatipatsa chakudya ndipo analankhula mau ake atatu 'Mulungu ndi wamoyo.'

Titafika kuno anthu adatirandira ndi manja awiri ndipo kulonjerana kwake kunali koti mtendere ukhale ndi inu iwoso potiyankha adati tikulandirani mwamtendere. Ndipo madzulo atsiku limenelo tinakhala womasuka monga anthu a banja limodzi.

Pafupifupi hafu ya akaidi kuno ndi anthu opulumutsidwa. Ena ndi alaliki amphamvu, ena woyimba mogwira mtima ndipo nthawi ya madzulo titamaliza ntchito zathu timakhala pamodzi kuyimba ndi kupemphera izi zimatirimbikitsa kwambiri. Ukakhala mkhrisitu umapeza mtendere kuli kose ungapite. Kuno ndaphunzira nyimbo zambiri zatsopano. Nditakwanitsa zaka 19 ndinali pa chikondwerero choti ndatha chake chimodzi chimulandirire Khrisitu kukhala mpulumutsi wanga.

Maria ine pamodzi ndi abale ena 7 tabatizidwa. Pa nthawi imeneyi ndidalakalaka iwe utakhalapo kuti ndikupepese kachiwiri chifukwa chokuzuza popanda chifukwa. Komaso kuthokoza chifukwa cha chikondi unandionetsera pa nthawi ijayo imene ine ndinali mu m'dima. Ndi bwino kwambiri kuti tsopano tiyima pamodzi pa maso pa Mulungu. Abale onse kuno akukupatsa moni ndipo ndi okondwa kuwona kuti chikhulupiriro chako chikupitirirabe. Ngati ukhala ndi mpata wolembera ena uwapatse moni wochokera kuno kwa abale awo.

Ndine Varia

**Kalata Ya Chisanu**

Wokondedwa Maria, ife kuno tonse tiri bwino kuphatikizapo mlongo X. Ife tsopano ....Anatitumiza kuno....Ndikukuthokoza Maria chifukwa chondisamalira ine. Tinalandira zonse zimene udatikonzera. Koposetsetsa ndi kuthokoza chifukwa cha baibulo unanditumizira zikomo kwambiri. Ndipo undithokonzere kwa onse chifukwa cha zimene akundichitira. Malinga ndi zimene Mulungu akundichitira pa moyo wanga sindisamala za zuzo limene anthu ena angandichitire chifukwa kwa ine kupulumutsdiwa ndi chisomo chokhachokha sindidayembekezere ayi. Chonde mundipempherere kuti moyo wanga usabwerere m'mbuyo. Ambuye akusungeni ndi kukulimbikitsani pa ntchito ya uzimuyi.

Ineyo pamodzi ndi mzanga X tikupsopsonani ndi chikondi. Ndiri ndi chikhulupiriro kuti nthawi ina ndidzakulemberaso kalata ina. Osadandaula nafe. Ife tiriokondwa chifukwa mphoto yathu yaikulu iri kumwamba (Mateyo 5:11-12).

Ndine Varia

Iyi inali kalata yomaliza yochokera kwa Varia. Mtsikana yemwe anali wachikomunisiti koma analandira Khrisitu ndipo amachitira umboni za Yesu. Pano ali kundende kumene akugwira ntchito yakalabvula gaga. Komabe papita nthawi tsopano, ndiye sitidziwa kumene ali. Koma chikondi chake ndi umboni wake ndi zogwira mtima.

# MUTU 7

Ine ndikudziwika ndi mau woti kapena dzina loti "Mau a m'chalichi chobisika." Sikuyenera ine kutchedwa dzina lotere lomwe liimira chiwalo cha Khrisitu. Mzaka zonse ndakhala ku maiko achikomunisiti, ndinali mtsogoleri wa chalichi chobisikachi. Ndipo modabwitsa kwa Ambuye ndinalinso m'ndende zaka khumi ndi zinayi nkudzaso zina ziwiri zowonjezera ndipo ndinali kuzuzika kosaneneka. Koma mwa chisomo cha Mulungu kudamukomera iye kukalowa m'ndendemo ndikukanditulutsamo kuti ndibwere kuno ku maiko akuzambwe ndidzakuwuzeni za zimene zikuchitika m'maiko achikomunisiti.

Ine ndikulankhula nkhaniyi m'malo mwa anzathu omwe adamwalira kale, ndi iwo amene pakali pano akukumana m'mapanga ndi mnkhalango kukambirana za chipulumutso cha Yesu.

A Chalichi chobisika ndiwo adakoza kuti zinthu zikhale motere kuti ine ndibwere kuno kudzafotokonzera inu akhrisitu anzathu zomwe anzanu akuziona ku maiko komwe kulibe ufulu wa chipembedzo. Uthenga umene andituma nawo woti ndidzanene ndi uwu: "Musatisiye tokha!"

"Musatiiwale!"

"Musaleke kutiwerengera!"

"Tipatseni zida zimene tikufuna ndipo tidzazigwiritsa ntchito moyenera!" Uwu ndiwo uthenga adandi-

tumiza kuti ndidzakuwuzeni.

Ndikulankhula nkhaniyi m'malo mwa mpingo wochita mwakachetechete, mpingo wobisika, mpingo wopanda mawu. Akhrisitu aku maiko achikomunisiti sakupempha njira ya mmene angathawire m'dzikomo ayi kapena kuti apeze njira yoti zawo ziziyenda mopanda zobvuta ayi, koma akupempha zida zoti ziziwathandiza pa ntchito yopititsira mtsogolo utumiki. Akufuna mabaibulo kuti ana awo ndi iwo pamodzi aziwerenga ndi kuthandiza ena pa ntchitoyi.

Chalichi chobisikacho ku Rumania chilingati sitima yomwe yagundana ndi izake ndipo anthu ambiri afa. Momwemo dokotala akamapita pakati pa mitemboyo amakhoza kunena kuti ndikadakhala ndi zipangizo ena akanapulumuka. Dokotalayo anali nawo mtima wopulumutsa koma alibe zipangizo. Umu ndi mmene mpingo wobisika ulili ku Rumania ndi maiko ena komwe kulibe ufulu wachipembedzo. Chalichi-cho ndi chokonzeka kuthandiza koma chiribe zida zogwirira ntchito. Tsono pempho lathu ndi mabaibulo.

## Akhrisitu Mungathandize Bwanji

Akhrisitu wochokera m'maiko aufulu wa chipembedzo angathe kuthandiza m'njira zosiyanasiyana. Azathu achikomunisiti samakhulupirira kuti pakutha pa moyo uno kuli moyo wina. Sadziwa kuti kuli mphamvu ina yochokera kwa Mulungu imene munthu amathandizidwa nayo. Tsono akhrisitu angathe kuthandiza pa mayendedwe awo osati monga mmaonekedwe a thupi koma m'chikhulupiriro moyanjana ndi Mulungu. Akhoza kuthandiza polimbana ndi machi-

tidwe woipa womazuza akhrisitu podzipereka iwo ngati sembe pa maso pa Mulungu. Inu akhrisitu azathu mukhoza kumatipempherera ngakhale kuti nthawi zina pa mbuyo pa pemphero zinthu zimafika poipa; m'malo moti akhrisituwo awasiye kuwazuza ndiye amaonjezera kulandira zilango zina zoopsya. Tsono tisaiwale kuti ngakhale pemphero la Ambuye wathu ku Yerusalemu lidawonjezera bvuto pa moyo wake mpaka Yesu adapachikidwa. Koma patangotha masiku ochepa anthu 5,000 anaguguda pa chifukwa chawo ndiku tembenuka mtima. Pemphero liri lonse lomwe mwini wopempheredwayo akalikana limabwerera kwa iwe wopemphera ndi dalitso lalikulu ndipo wolikanalo kumakhala temberero kwa iye. Apa zitsimikiza kuti pemphero siripita pa chabe limabwera ndi mdalitso. Pofuna kutsimikiza kuti pemphero siripita pa chabe limabwera ndi mdalitso. Pofuna kutsimikizira mau a Khrisitu, ine ndi akhrisitu ena pa nthawi ya nkhondo ya Hitler ndi anthu ake tinakhala tikupemphera ndipo sindikaika kuti mapemphero athu adagwira ntchito yogonjetsa Hitler. Tiyenera kukondana nawo anzathu monga tidzikonda ife eni. Chocho makomunisiti ndi anzathu tiyenera kuwakonda monga mmene tingakondere wina aliyense.

Chikomunisiti chidadza chifukwa choti ife akhrisitu sitidakwanitse mau a Khrisitu woti: "Ndadza ine kuti akhale ndi moyo ndi kukhala nawo wochuluka." Akhrisitu sadabweretse moyo wochuluka kwa munthu aliyense, ichi nchifukwa chake kunja kuno kuli chikomunisiti.

Choyenera kudziwa nchakuti bvuto liri ndi ife akhrisitu chifukwa tachita dyera mmalo mosonyeza chi-

kondi kwa aliyense ndi kumuuza za chipulumutso; ife takhala tikuzengereza ndi zina ichi nchifukwa chake pali chikomunisiti. Pa chifukwa ici tiyeni tiziwapempherera azathu achikomunisiti kuti adziwe chowonadi.

## Mabaibulo Ndi Mabuku Ena Amau A Mulungu Akufunika Mwansanga

China chimene akhrisitu angathe kuthandiza ndikutumiza mabaibulo ndi mabuku ena a Chiuta kwa anzathu aku maiko achikomunisiti. Malinga ndi njira zake zotumizira mabukuwa angathe kumafika popanda kugwidwa ndi bomalo. Pakali pano ine chibwerere cha kuno ndatumizapo kale mabaibulo ndipo anafika bwinobwino. Mabukuwa akufunika kwambiri akhrisitu zikwizikwi ku Rumania sanawaone mabaibulo. Anthu ena awiri wowoneka mwa umphawi adafika ku nyumba kwanga tsiku lina kudzapempha ganyu kuti apeze ndarama zoti agulire baibulo lakale. Tsono pokhala ine nthawi imeneyi ndipo ntangolandira mabaibulo kuchokera ku Amerika ndi nawapatsa anyuwani osati lakale. Ndiye anthu aja atapita kwawo anakalemba kalata yothokoza kwambiri chifukwa cha ma baibulowo. Pakalatapo, anthu amene adasainapo anali okwana makumi atatu ndipo akuti chimene chidachitika nchakuti mabaibolowo adawang'amba ng'amba ndikugawana ndiye akamawerenga amasinthanasinthana.

Ndizobvetsa chisoni kuti anthu ena amasinthanitsa ng'ombe zawo kuti apeze baibulo. Ndikumbuka munthu wina adasinthanitsa ring yake ya ukwati ndi baibulo. Komaso kwathuko kulibe khisimisi khadi ndipo chimachitika nchakuti wina akalandira khisimisi kha-

diyo, ndiye kuti mudzi onse amafika pa wa malo kuti amve zowerengedwa pa kahadiro. Iyo ndi njira imodzi a khrisitu angatumizire mabuku ku Rumania.

Chachitatu chomwe akhrisitu angachite ndi kusindikiza mabuku amene akhrisitu aku Rumania angamaphunzitsire ana awo potsutsa zomwe amawaphunzitsa achikomunisiti m'sukulu zawo. Ndipo a Wurmbrand adati mabuku otere ndi ofunika mwa msanga. Iwo adati pakali pano akhrisitu ku maiko achikomunisiti ali kakasi kusowa mmene angamawathandizire ana awo paza Mulungu.

Ana athu amene akuonongeka ndi chiphunzitso cha chikomunisiti ayenera kukhala ndi timabuku monga.... "Yankho la" "Mulungu" "Yankho la mkhrisitu" ndi "Yankho lathu" mabuku otere angakhale othandiza pofuna kutsutsa zolemba za m'mabuku awo achikomunisiti.

Fundo ya chinayi imene tingachite ndiye kugwirizana ndi akhrisitu azathu a chalichi chobisika pomawatumizira ndarama zoti aziyendera pokalalikira m'madera ena a m'dzikomo. Akhrisitu ambiri akulephera kuyenda chifukwa alibe ndarama zoyendera zogonera ngakhale zogulira chakudya. Tsono atamalandira ndarama zokwana £5-£10- pa mwezi ndiye kuti akhoza kukhala omasuka ndi kumapita ku midzi yakutali kukalalikira. Akhrisitu ambiri amene adatsekeredwapo m'ndende amafuna atakachitira umboni kwina koma chifukwa chosowa ndarama amangokhala malo amodzi.

Gawo lina limene Akhrisitu angachite ndiye kumakhala ndi mapologramu a mau a Mulungu pa wailesi zathu. Poteropo tikuthandiza anzathu ku maiko

achikomunisitiwo kuti azimvako zimene zikulalikidwa pa wailesi za kuno. Chifukwa kwawoko, wailesi zawo ndi zongomvera za chikomunisiti. A Wurmbrand adati ena mwa akhrisitiwo ali ndi wailesi zamphamvu zoti zokhoza kumagwira zonena za m'maiko ena akuzambwe ndi ku United States.

## Bvuto La Mabanja Omwe Anansi Awo Ali M'ndende Kapena Adaphedwa

Mabanja ambiri ku Rumania akusauka kwambiri chifukwa choti makolo awo ali m'ndende kapena kuti adaphedwa chifukwa cha chikhrisitu. Ndiye mabanja wotere ndi wofunika ku mawathandiza m'njira ina yake. Chifukwa anthu ena onse kumeneko sawalola kukapereka thandizo kwa wobvutikawo. Ndingakutsimikizireni kuti ine ndi banja langa popanda thandizo lochoka kuno sibwezi ndiri pakati panu ndi kumalankhula zonsezi. Pano bwezi mwina titafa. Pakali pano zinthu ku Russia zabvuta akhrisitu ambiri akuphedwa ndipo otsalawo nawo akungofa ndi njara. Tiyeni tiwathandize azathu ndi zinthu zimene tiri nazo. Ndipo siku Russia kokha ngakhale ku India ndi ku Afrika nakonso nkofuna chithandizo. Ine monga mmodzi wa mamembala a chalichi chobisika ndidadza kuno kuchoka ku Rumania kuti ndidzakudziwitseni za momwe zinthu ziriri m'maiko achikomunisiti. Ndipo ndikhulupirira ndanena zonse zofunikira ndipo zonse tsopano ziri kwa inu.

Nthawi imene ine ndinali m'ndende, atandimenya mapazi anga lirime langa lidalira. Tsono chifukwa chiyani lirime lidalira pamene ndi mapazi adamenyedwa. Lirime lidalira chifukwa choti lirime ndi

mapazi ndi ziwalo zimodzi. Chimodzimodzi inu akhrisitu akuno muli amodzi ndi akhrisitu amene akuzuzika chifukwa tonse ndife ziwalo za Khrisitu. Kodi pamenepa simungamve kupweteka chifukwa cha akhrisitu azathuwo?

Pamene Yesu anali mchisoni m'munda wa getsemani wophunzira anali patali monga ulendo wa Petulo, Yohane ndi Yakobo ndipo tsoka ilo anali kugona ndiye kuli kotani ndi anzathu amene akumva kuwawa kodi sitingawathandize? Tiyeni tiuze abusa athu ndi atsogoleri ena onse amipingo kuti tiwaganizire anzathu amene ali m'ndende kumva zowawa chifukwa cha Khrisitu. Zimene zidachitika poyamba pamene wokhulupirika anali kuphedwa ndi kuponyedwa m'ndende lero zikuchitikaso ndiye sibwino kuti akhrisitu inu amene muli m'maiko aufulu wachipembedzo kuti muzigona m'malo mothandiza anzathu ku maiko ena. Tisachite ngati zimene adachita a Yohane, Petulo ndi a Yakobo kugona pamene mbuye wawo anali pa masautso oopsya. Kodi mudzagonanso pamene anzanu aku buwulu ndi mabvuto chifukwa cha Khrisitu. Kodi mudzawalekerera okha pa nkhondoyi. Tamvani pempho lathu. "tikumbukireni" "tithandizeni" "Musatisiye."

Apa ine ndafotokoza zonse za uthenga wa abale anu womwe ali mu utumiki wobisika, omwe akuzuzika m'ndende komanso kuphedwa chifukwa cha chikomunisiti chiri m'maikowo.

Mwini wake bukuli ndi wokonzeka kulandira kalata kwa wina aliyense.